

MAFUNSO NDI MAYANKHO



Tiyeni titalire titayima kwa mphindi yokha pamene ife tikuweramitsa mitu yathu kwa pemphero.

Atate Mulungu Achisomo, ife tikukuthokozani Inu mmawa uno kuchokera mu kuya kwa mtima wathu, chifukwa Inu ndinu okhoza ndi kulolera kuti muyankhe mapemphero athu. Ndipo ife tikupemphera kuti Inu mulandire kupereka mathokozi kwathu chifukwa cha zimene Inu mwatichitira kale ife. Ife tikuyembekezera ndi chiyembekezo chachikulu kuti Inu mutithandize ife mmawa uno, ndipo pamene ife tizichoka pa makonde a nyumba ino, mulole ife tituluke pano tiri munthu wosinthika kuposa momwe ife tinaliri pamene ife timabwera muno. Mulole Mzimu Woyera utiwumbe ife mmawa uno, makhalidwe athu, ndi kutipanga ife kukhala omvera a mu Ufumu Wanu pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen. (Mukhoza kukhala pansu.)

² Ndikupepesa basi kuti ndachedwerapo pang'ono pokha, koma ine ndinali ndi zinthu zingapo ndithu zoti ndichite, ndiponso anthu odwala ambiri ndi oyankhulana nawo ine ndisanafike mu—ku nyumbayi pafupifupi.

³ Ndipo kotero, ife tiri okondwa kuti tiri pano mmawa uno ndi kukuwonani anthu abwino nonsenu. Ndipo ine ndikufuna kuti ndiwathokoze aja—anthu awo amene anatumizira ife zinthu zabwino zija, mphatso ya kwa mkazanga ndi kwa—ndi—m'bale amene ananditumizira ine mfuti yake ya agwape. Ambuye amudalitse iye. Iye—anati iye wayamba kukalamba ndipo sakanafuna kuti aziigwiritsanso iyo ntchito panonso, ndipo iye wafuna kuti ine ndikhale nayo iyo; kotero i—ine ndine woyamikira ndithudi kwa izo—chifukwa cha izo. Utali wonse pamene ine ndikhale wamoyo, m'bale, momwe ine ndingathe kudzithandizira ndekha, ine ndikhala ndiri nayo iyo. Ine sindimaiyika konse iyo mu dzanja langa kupatula ine nditaganizira za inu ndi kukupemphererani inu.

⁴ Tsopano, ife tiri...Zinthu zochulukira kwambiri zoti zichitidwe lero, ine ndimaganiza mwinamwake pamene ine ndiri kuno ine ndikhale ndi mafunso ena ndi kupeza chimene chinali pa mtima wa mpingo wanga—osiyana awo. Ine ndithudi ndinaterodi! Ine ndiri ndi mafunso okwanira oti akhoza kunditengerera ine mpaka Zakachikwi zidzayambike! Ine sindimadziwa kuti analipo ochulukira chotero amene akanakhoza kupezedwa. I—ine ndiri nawo zana ena pano, ndipo alipo zana kapena kupitirirapo amene abwera muno mmawa uno. Kotero ine sinditha konse kuwayankha iwo, ine ndikulungalira,

molondola, chifukwa...Ndipo i—iwo ndi mafunso abwino, abwino kwenikweni.

⁵ Tsopano, ena a iwo sangati awerengedwe apa pomwe mu chigulu, kotero inu mukudziwa, ine ndawafunsa iwo... Ngati zimene ine sindingathe kuziika pamenepa...Ndi mavuto a m'banja ndipo...inu mukumvetsa. Ndipo i—ine ndawapempha kuti ndikhale nawo onse mwamuna ndi mkazake pa kuyankhulana kwapadera, chotero ine ndithe kuyankhulana nawo iwo mwamseri pa nkhani zimenezi. Si zinthu zoipa; ndi zinthu zoti zikuyenera kuthetsedwa mu banja, kungoti chibadwa cha umunthu ndi mtundu umene ife...nthawi imene ife tiri nkukhalamo ndi zina zotero nzimene zikubweretsa zinthu zizi apo, ndipo awo ndi mavuto amene amapita ku banja la umunthu; ndipo iwo ayenera kuti ayankhidwe. Ndipo kotero, ine ndichita chirichonse chimene ine ndingathe kuti ndiwayankhe iwo mwa njira yopambana.

⁶ Nthawizina poyankha mafunso, izo zimakhala ngati zimatenga nthawi yaitali; ndipo ine sindikufuna kuti ndiphonye lirilonse la iwo. Ine nditenga lirilonse mwapafupi basi momwe ine ndingathere. Tsopano, iwo basi—ine ndinangowalongeza iwo mu thumba pano, ndiwayankha iwo, ndipo—ndiikapo Lemba ine ndikakhala ndiri nalo ilo, n—ndi kuzibwezeretsa izo. Ndiye ine ndinali tsiku lonse dzulo, ndi gawo lalikulula la usiku wausiku watha, ndipo chiyambireni kutangocha pang'ono mmawa uno. . . Ndipo ine ndiri nazo pafupi kawiri kwa zimene zinabwera mmawa uno. Kotero, ine ndikuganiza zimene ife titi tichite, Ambuye akalola, ine ndiwayankha iwo mpaka—momwe ine ndingathere mpaka pafupi dzuwa paliwombo, ndiyeno nkubalalitsa, ndiyeno nkukabwerera kachiwiri usiku uno n—ndi kuyesera kuti titsirizitse ochuluka momwe ine ndingathere usikuuno, ndi kuwona ngati ine ndingathe kutenga—kuwatsiriza iwo apo. Ndipo mwinamwake ine sindichita kuti ndikulangeni inu motalika chotero mu kukomana kumodzi kwakutali kwambiri. Ndipo ine ndikuganiza izo zingakupatseni inu nthawi kuti mupite panja, ndi kukapumula, ndi kupezanso mphamvu pang'ono, kukausa pang'ono kapena chinachake, ndi kubweranso ngati inu mungathe. Ngati inu simungathe, bwanji, M'bale Fred Sothmann, ine ndikulungalira, ali kujambula izi. Kodi izi zikujambulidwa? Chabwino, izo ziri bwino. Eya, iwo ali mu chipindamo akujambula izo, n—ndipo tepi iyi mwina—ngati ziri zabwino—inukhoza kukhala nayo tepiyo; iyo ingasungidwe ndipo izitchedwa *Mafunso ndi Mayankho*, chifukwa muli mafunso ena olimba kwenikweni mkati umu ndi chinachake. . . Ambiri a iwo ali pa chiphunzitso cha mpingowu.

⁷ Tsopano, ine ndikufuna kuti anthu adziwe kuti nthawizina poyankha mafunso awa, ndi zovuta. Zimatengera chisomo chochuluka kuti uyime pano, ngati inu mutadziwa chikondi

chimene ine ndiri nacho pa anthu inu. Ine sindingathe kuchifotokoza icho. Ine sindimachifotokoza nkomwe icho kwa ana anga; ine sindimachifotokoza nkomwe—chikondi changa chakuya kwa mkazi wanga momwe ine ndimayenera kuti ndizichitira, chifukwa nd—ndine wopsyamtima, ndipo ine ndimangopita mu mzere umodzi wowongoka. Pali chinthu chimodzi chokha chimene ine ndingafotokozereko chikondi changa kwa icho: ndiko kwa Mulungu Wamphamvuzonse. Ndipo i—ine ndimangomukonda Iye poyambirira pa zonse. Anthu ena ine ndimawakonda, koma i—ine sindikufuna kuti ndifike—ine sindikufuna kuti ndiwononge chikondi icho chimene ine ndiri nacho kwa Iye; kulola icho kukhala choyambirira. Kotero chotero, pamene ine ndikuyankha mafunso anu, ine ndikuwayankha iwo ndi chikondi mu mtima mwanga kwa inu; koma chinthu chimodzi chiri patsogolo panga nthawizonse: chimenecho ndi Yesu Khristu (mwaona?), mwa njira yomwe Iye akanayankhira izo.

⁸ Nthawizina ine ndingatidi ndiyankhe... Izo zingatidi zipweteke, zingatidi zikande, ndipo i—ine sindikutanthauza kuti izo zikhale mwanjira imeneyo. Ine ndikuyankha izo ndi cholinga chimodzi, monga ine ndinanenera, Khristu patsogolo panga. Ndipo ine ndikuyenera kuti ndizikumbukira kuti Ali Iyeyo amene i... Ine ndidzati ndidzakayankhireko. Kotero chikondi changa choyamba chiri kwa Iye; chikondi changa chachiwiri chiri kwa inu anthu, ndipo kotero i... Mpingo Wake umene Iye anawugula ndi Magazi Ake omwe. Ndipo Iye amakukondani kwenikweni inu kuposa momwe Iye amadzikondera Iyeyekha, chifukwa Iye anadzipereka Iyeyekha pofuna inu. Ndinu ogulidwa a Magazi Ake, ndipo i—ine ndikuzigwira izi mosamalitsa basi ndi moonamtima momwe ine ndikudziwira kutero. Komano, pochita izo nthawizina inu mumaganiza, “Uko kunali kuyankhula kwa mwano zedi ine... pafupi... Izo ziri zosathwa kwambiri ndi zosabisa.” Ine ndikuchita izo ndiri naye Iye mu malingaliro anga (mwaona?) kuti ndiyesere kupanga—kuti ena a—aliyense awone basi kuti izo ziyenera kumakhala mwanjira imeneyi. Izo si chi—chirichonse choti chipweteke kapena osatinso kuposa kungoti nditsimikize kuti anthu azimvetse izo, ndipo ine ndikuyembekeza aliyense azilandira izo mwa njira imeneyo. Ndipo tsopano, mkati umu ife tikupeza zomwe ziri mu malingaliro anu.

⁹ Ndipo pamene ine ndikukuwonani inu nonse mutasonkhana mmawa uno ndi chirichonse chitadzazidwa pozungulira, ndipo ine ndikuganiza tiri ndi khamu losefukira m—mu mpingo wina. Mpingo wapaubale watenga—wailesi kapena china chonga—kulumikiza kwa lamy. Ndizo... Kusefukira kuli mu mpingo umenewo mmawa uno, ine ndamvetsedwa. M’bale... Kapena m’bale wina ali ndi—mpingo umene uli ndi kusefukira kumene kwasamutsidwa kuchokera kuno kupita ku mpingo umenewo.

Izo ziri chomwecho kuti inu musachite kuyima pa mapazi a wina ndi mzake ndi zinthu mutazungulira khoma.

¹⁰ Tsopano usikuuno, Ambuye akalola, ife tikhala ndi—ife tiyamba molawirira usikuuno. Ine ndikufuna kuti ndimupemphe m'busa ndi—borodi ngati iwo angathe...Tiyeni tiyambe molawirira pang'ono pokha usikuuno, chifukwa cha anthu, ena a iwo ali pano, ndipo iwo akhala ndi kuyendetsa kwakutali. Ndipo ine ndikanafuna kuti ndiyambe molawirira ndi ora usikuuno, ngati ife tingathe, ndi kutsirizitsa izo. Kotero inu... Mwamsanga basi inu mukakhala ndi chakudya chanu ikadutsa sikisi koloko kapena nthawi iliyonse, ndiye, ine ndiyamba. Mwaona? Kuti, inu kawirikawiri mumayamba pa hafu pasiti seveni sichoncho inu? Tiyeni tidzakhale, tiyeni, mulole ine ndidzakhale pa nsanja pofika seveni koloko. Mwaona? Ndipo pamenepo pofika eyiti koloko kapena hafu pasiti eyiti, kapena chinachake monga choncho, izo zikupatsani inu nthawi k—kuti mupite ku makwanu ndi kukakonzekera ntchito ya mawa, ngati mawa liripo.

¹¹ Tsopano, Ambuye akhale nanu ndi kukudalitsani inu mochulukitsa, ndipo ine ndipita mwamsanga pamene msonkhano uno utha ndi kukawatenga mafunso ena awa ndi kuyesera kuti ndiwayankhe iwo. Ine ndingolemba pa iwo, pang'ono pokha—zidutswa pang'ono za zolembe ndi zina zotero, zimene ine ndingathe—ine ndingathe...Zimakhala ngati ndingaiwale Malembawo. Ndiye pamene ine ndikakhala mu chipindacho ndikuwerenga, ndiye ine (ine ndikufuna kumalozersano kwa iwo penapake, ndipo ine ndiri nazo izo pano) ndipo—ndangozilemba izo pa chidutswa cha pepala. Ndipo kotero, ngati izo ziri mu—bukhu lolongosola ine ndikuyenera kuti ndikazitenge izo, kapena kufotokoza kwina kwa mawu, kapena dzina, ine ndikhale nditazilemba izo patsogolo panga. Ine sindikusowa kuti ndichite kubweretsa chimulu chachikulu cha mabuku ndi zina zotero; ine ndikhale nazo izo pamenepo.

¹² Tsopano, ngati funsola simunakhutitsidwe nalo inuyo, chabwino, ndiye i—mwinamwake ine ndalakwitsa. Mwaona? I—i—ine mwinamwake ndingakhale nditalakwitsa, chifukwa zinthu izi ziri basi mwa kupambana kwa kumvetsa kwanga. Ndipo ine ndikufuna—atumiki amene angakhale ndi osonkhana awo, kapena osonkhana a mpingo winawake amene angamamvetsere kwa mafunso amenewa...Ine sindikufuna izi...Ngati izo ziri ndi chinyezimiritsa chirichonse pa chiphunzitso chanu ndi o—o—osonkhana anu, ine ndikufuna osonkhanawo kuti amvetse bwino bwino kuti uku ndi kuphunzitsa kwathu basi pa kachisi pano. Ine sindiri ndikuyesera kuti ndizikakamizire izo pa magulu ena onse a anthu. Ndipo i—i—ine ndikufuna kuti ndikhale Mkristu m—mu mtima mwanga, kuti ine ndiziphunzitsa zimene ine

ndimazikhulupirira. Ine ndikuima pa kukhudzidwa kwanga. Ngati ine ndinyengerera pa izo, ndine waupandu kwa Khristu ndi wachinyengo kwa inu; ndipo i—ine ndiyenera kuima momvera pa zimene ine ndikuzikhulupirira kuti ziri Choonadi. Koma munthu wina aliyense ali nawo ufulu kuti azichita mofanana. Mulungu ndi Woweruza wa ife tonse.

¹³ Tsopano, basi ife tisanayambe, ine ndimaganza kuti nditchulepo za wambiriyakale wabwino, Paul Boyd. Ambiri a inu mukumudziwa iye; iye amabwera kuno ku kachisi. Iye wabwerera kumene kuchokera ku Yerusalemu ndipo anakakhala nawo pa Chiwonetsero cha pa Dziko. Iye ali mochuluka kwambiri m—mphuzitsi wa uneneri, ndipo iye ndi wazambiriyakale, mmodzi wa abwino kwambiri. Iye ndi m'bale wa Chimennonite—iye anali—ndipo iye analandira ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndipo kotero iye anakhala mzanga wapafupi kwambiri wanga. Ndipo iye nthawizonse amayang'ana ndi kumasamalitsa chirichonse chimene ine ndinena chokhudza za uneneri, kuti ayang'anire ndi kuwona ngati izo ziti zifike pokwaniritsidwa.

¹⁴ Ndipo tsopano, iye wandilembera ine apa (pamene iye ali kuno mu States kachiwiri tsopano), ndipo izo ziri pa bolodi lazolengeza, ine ndikuganiza, mmawa uno. Ndipo iye walembe apa cholembedwa chimene iye wachiika mu imodzi ya mapepala kapena chinachake kapena imzake, zokhudza mauneneri opambana. Ndipo iye watchula chinthu chachisanu, ine ndikuganiza icho chiri, chimene ine ndinachiwona zaka sate-firii zapitazo chokhudza kupindula kwa—kupita patsogolo, maka, kwa sayansi. Ndipo aliyense wa inu amene mukukumbukira, inu munazilemba izo. Ine ndiri nazo izo mu mabuku anga. Ndi chirichonse chimene Ambuye ananena... amandiuzwa ine, ine ndimazilemba izo, icho ndi chachikulu cho-... kapena chinthu chimene ine ndingawauze anthu.

¹⁵ Ndipo ine ndimaganza mmawa uno, ife tisanayambe ichi... Uwu si ulaliki, koma ife tiri pano kuti tikhale palimodzi kuti tiphunzire kuchokera kwa wina ndi mzake zimene ziri pa mitima yathu. Tiyeni tizipese bwino zinthu izi tsopano, pamene ife tikubwera chotsika kudutsa mu Mibadwo ya Mpingo ndi zina zotero. Ine ndikuganiza ndi chabwino kuima ndi kukhala ndi msonkhano kapena iwiri, ndi kufufuzapo, ndi kupeza zimene ziri pa mtima wa anthu, ndiyeno nkumapitirira kuchokera pamenepo. Inu mukuona? Ndiye nkubwerera mmbuyo kachiwiri ndi—kupita mu ndi mndandanda w—wa mautumiki. Ngati Ambuye alola, ine ndikufuna kuti ndidzakhale nazo izo pano pa kachisi pasanapite nthawi, mndandanda wautali basi wa mautumiki; inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza, w—wa monga maphunziro osiyana; ndi kumapitirira nazo basi mpaka Iye andidzere ine kapena ine ndipite kukakomana naye Iye, limodzi. Mukuona?

¹⁶ Paul Boyd walembe apa zokhudza zinthu zisanu ndi ziwiri zija zimene ine ndinaziwona mu 1933, zomwe zinali zoti zidzachitika. Ndipo iye akuziyang'ana izo mwatcheru basi, mwaukatswiri, momwe iye angathere, chifukwa iye ndi wazambiriyakale. Ndipo iye amaziyang'anitsitsa izo, ndendende basi zimene iwe unena. Ndipo iye anawona zinthu zija zimene zinanenedwa zaka zambiri zapitazo: za momwe Mussolini...ndi zomwe zikanadzamuchitikira iye, ndi Hitler, ndi zomwe zikanadzakhala za iye; ndi momwe Chikominisi chikanati chidzatenge zonse chi Fascism ndi zonse izi; ndi momwe—Mzere wa Siegfried ukanati udzamangidwire, ndi momwe kuti Amereka akanati adzakamenyeredwere kumeneko (ndipo iwo sakanati avomereze konse izo mpaka pafupi zaka ziwiri zapitazo, ndipo iwo anatenga zithunzi za ku German za kuzingidwa kumeneko; ndipo iwo analandira kumenyedwa kwenikwenidi. Iwo monga...Iwo anakataya ankondo awo pafupifupi kumeneko); ndi zinthu zonse izo zimene zinachitidwa.

¹⁷ Ndipo tsopano, izo zinanenedwa aponso, “Ndipo zidzafika pochitika, kuti asanafike mathero a nthawi, kuti magalimoto adzatenga maumbidwe a dzira, kukhala mochuluka ngati dzira.” Ndipo ine ndinawona banja la Chimereka likuyendetsa mu msewu mu galimoto imene...Iwo anali atakhala akuyang'anizana wina ndi mzake, ndipo iwo anali ndi gome, ndipo anali, ankawoneka ngati, akusewera njuga kapena makhadi. Ndipo iwo analibe chiwongolero chirichonse mu galimotoyo. Ndipo iyo inali kulamulidwa ndi mphamvu inayake popanda chiwongolero. Ndi angati akukumbukira ine ndikunenera izo (mwaona?), izo zakhala ziri kuno?

¹⁸ Tsopano, pa Chiwonetsero cha Padziko iwo ali nayo kale galimotoyo pa msika. Apa pali...Iyo ikugulitsidwa tsopano; kampani yaikulu inayake yatenga ambiri a iwo. Ndipo galimoto iyi, ndi iyi apa. Paul Boyd anakumbukira uneneriwo, anakayang'ana mu bukhu lake zimene ine ndinanena, ndipo anatengera chithunzicho mmenemo. Ndipo ndi iyo apo, ndendende mwa maumbidwe a dzira, ili ndi mipando iwiri itayikidwa mbali *iyoyi*, ndi iwiri itayikidwa mbali *iyi*, ndi gome litayikidwa pakati kuti azisewera makhadi ndi zinthu, ndendende basi.

¹⁹ Mawu a Ambuye ndi olondola mwangwiro. Izo zinali mu 1933. Izo zingakhale ziri...Tiyeni tiwone, kodi zimenezo zingakhale chiani? Zaka sate-thuu zapitapo, si choncho izo? Ichi ndi 1964. Eya, sate...Eya, zaka sate-wani zapitapo. Zaka sate-wani zapitapo Ambuye anandiiza ine zimenezo, ndipo ndi iyi pano. Ndipo kampaniyo ili kuno imene yawaodetsa kale iwo; n—ndipo makampani a magalimoto akatundu ndi zinthu akugula magalimoto akatundu opangidwa monga amenewo. Iwo akhoza kumawalamulira iwo kuchokera ku malikulu

awo monga choncho, sakusowa ngakhale kuti azikhala ndi woyendetsa mmenemo. Ndipo pano iyo yapangidwa kale, ndipo apo ziri ndi magalimoto. Tsopano, izo ziri pa bolodi la zolengeza kumbuyoko, ndipo inu mukhoza kuwerenga uneneriwo ndipo mungawone kulondola kwake Mulungu wathu aliri, momwe Mawu Ake. . .Iye anati, “Miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Mawu Anga sadzalephera konse.”

20 Tangoyang’anani, zaka sate-firii zapitapo. Inu mukudziwa chomwe—chomwe ya 1931, kapena chirichonse chomwe chinali, mtundu wa galimotozo momwe zinkawonekera; iyo inkawoneka ngati chidina. Iwo anati, “Iyo izidzawoneka monga ngati dzira, idzakhala ngati dzira.” Ndithudi, palibe wina muno, ine ndikupeneka, amene ali moyo lero kapena pakati pathu amene anandimva ine ndikunena zimenezo. Ndi. . .Inu mwandimvapo ine ndikuneza zimenezi kudutsa mmibadwo, koma. . .Eya, apo pali mkazi ali pano. Bwanji, Akazi a Wilson, ine sindimakuwonani inu pamenepo. Inu mukukumbukira pamene izo zinkachitika. Apo ndi pamene iye anachiritsidwa, akufa ndi TB (mayiyo, mwamuna wake ndi mwana wake wamkazi anabwera nandiitana ine kuti ndipite ndikamupempherere iye) mpaka iye ankawukha magazi mpaka—pangodya panali patadzaza n—ndi mapilo ndi zinthu zomwe iye ankawukhizirapo. Ndipo adokotala anati, “Palibe njira yoti iye angafike pakuti akhale moyo konse,” ndipo ngakhale. . .Iye anali kuyesera kuti anene chinachake kwa ine asanafe, ndipo magazi ankakhoza kukhavukira pa mabulangeti ndi nsalu zofunda pamene iye anali pamenepo, pamene iye ankayesera kuti akhosomole. Ndipo ine ndinamuchotsa iye pa kama ameneyo, ndipo ndinamutengera iye ku mtsinje wozizira kuno, ndi madzi achisanu, ndipo ndinamubatiza iye mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo izo zakhala ziri zaka sate-firii zapitapo, ndipo ndi uyu wakhala apayu lero, akadali ndi moyobe, pamene ana aakulu, athanzi, ambiri a iwo apita kale. Ndi inu apo. “Chisomo chododometsa, kukoma kwake kuchimva, chimene chinapulumsa wopanda pake ngati ine!” Izo zikungosonyeza momwe zimakhallira zangwiro pamene zifika pochitika ndi PAKUTI ATERO AMBUYE.

21 [Mkazi ayankhula kwa M’bale Branham kuchokera mwa osonkhana—Mkonzi.] Inde, uko nkulondola, Mlongo. Inde, bwana! Akazi. . .Ine ndinati akazi adzakhala opanda makhalidwe kwambiri mu. . .Tsopano, inu mukudziwa zaka sate zapitazo momwe iwo ankavalira. Ndinati iwo akukhala opanda makhalidwe kwambiri, mpaka iwo akumayenda mu msewu atangovala chokhala ngati zovala zawo zamkati. Ndipo ine ndinati, “Ndiye zidzafika pochitika, kuti iwo adzakhala ngakhalenso ochititsa manyazi kwambiri, mpaka iwo azidzavala chinachake chinkawoneka ngati tsamba la nkhuu.” Ine ndinaziwona izo, ndipo iwo ali nazo izo; ndipo iwo akuzivala

izo. Basi—kupanda makhalidwe kwa akazi kudzafika potsika kwambiri ndi mopanda ulemu! Ife sitingathe kutsika kuposa apo tsopano; inu simungathe kupita moipirapo. Iye ali pa mapeto! Mukuona, iwo sadzakhala ali kwathunthu amaliseche. Ayi, iwo...

²² Ine ndalalikirapo kwa anthu, akazi mwa makumi a zikwi amene amakhala alibe chidutswa chimodzi cha zovala pa iwo (mwaona?), amuna aang'ono, ndi akazi aang'ono, ndi onse, koma iwo asakudziwa kuti ali maliseche. Mwaona? Iwo samadziwa izo. Ndipo momwe akazi akuchitira lero...

²³ Ine ndinali kuyankhula usiku wina kwa amzanga ena a ine pamene ife tinali kutali komwe uko mmapiri, ndipo m—mkazi wachichepere...ine ndinali nditamupempherera kumene mwana wake; iye anali ndi khunyu; ndipo mwanayo ali bwino. Ndipo banja laling'ono, losawuka, kutali komwe uko ku phompho, kamunda kakang'ono ka fodya kachikale mozungulira nyumbayo—ndi pafupi zipinda ziwiri mmenemo—ndi ana seveni kapena eyiti... Mkazi ameneyo amagwira ntchito (o, mai!)—ali ndi nkhwangwa yaikulu kunjira uko, akuwaza nkhuhi ndi zinthu, n—ndi kumalima mminda, ndi kumalongoza zinthu. Ndipo ine ndinayang'ana pa mkazi wosawukayo—diresi yomweyo imene iye wakhala akuvala kwa chaka kapena ziwiri, ndipo yonse itagawanika ndi chirichonse...Ndipo ine ndinali kuyesera kuti ndipeze ena mwa madiresi a Meda kuti ndiwatengere uko kwa iye sabata yotsatira.

²⁴ N—ndipo ife tinazindikira titaima pamenepo, abale angapo ndi ine, donayo akumuyamwitsa mwana wake. Iye anangotulutsa bere lake k—k—kuchokera mu diresi lake ndi kuyamba kumamuyamwitsa mwanayo; ndipo izo zinakhala ngati zododometsa kwa miniti; umo ndi momwe amayi anga ankandiyamwitsira ine! Ndizo kulondola ndendende.

²⁵ Ine ndiri nawo ulemu kwa mkazi ngati ameneyo kuposa momwe ine ndimachitira kwa akazi enawa amene amaika kachingwe kakang'ono panso pawo kuti azidziponyera okha kunjira. Samawoneka nkomwe ngati anthu okhalapo. Iwo ali nacho cholinga pa kuchita zimenezo; izo ndi zachigololo, kupanda umulungu. Mkazi amayala zovala nthawizonse zambiri ndi kuyesera kuti adzipange yekha kumawoneka ngati chinachake chimene iye asali...ine...Bwanji, akazi s—sali kwenikweni mwanjira imeneyo; uwo ndi mtundu winawake wa zinthu zaku Hollywood. Ndipo mzimu wa mdierekezi umafika pa akazi amenewo kuti uziwapangitsa iwo kuti aziyesa kukopa tcheru cha amuna kudzera mu kugonana. Mabere a mkazi anapatsidwa kwa iye kuti aziyamwitsira mwana. Ndiko kulondola ndendende. Mkaziyo ali mu mzere wakusatukuka, koma iye wadzifoletsa molondola. Ine ndiri nako kulemekeza kochuluka kwa izo, kwa mkazi ameneyo monga choncho, chifukwa iye...Umo ndi momwe amayi ake

anamulerera iye; umo ndi momwe. . . I—iwo—samapereka chidwi chirichonse kwa izo. Mwanayo anayamwitsidwa apo pomwe monga chithunzi cha Madonna chimene inu mungachiwone. Ndipo ngati anthu atangokhazikitsa malingaliro awo monga choncho, izo zikanakhala zosiyana.

²⁶ Koma pamene inu mufika popita kunja ndipo mwinamwake kuvala zosachuluka ngati bulauzi kapena zina zotero, ndiyeno nkuzinyamulira mmwamba nokha kunja uko ndi ngolekera ndi zinthu, zimene zimawoneka zopanda umulungu ndi zopangitsa amuna. . . Kodi inu mukuzindikira kuti umenewo ndi mzimu wa mdierekezi uli pa inu? Kotero inu simukufuna kuti muzichita zimenezo, mlongo. Musati inu muzichita zimenezo; zimenezo ndi zopangitsidwa ndi Hollywood ndi msampha wa mdierekezi! Pamene inu muchita zimenezo, inu mumawapangitsa amuna kuganizira chinthu cholakwika pa inu; ndipo pamene inu muchita izo, ndiye inu muli wolakwa pa kuchita chigololo ndi mwamuna ameneyo, chifukwa inu munadziwonetsera nokha mwanjira imeneyo kwa iye. Inu simungachitire mwina momwe inu munawumbidwira, koma zingopitani ndi kumakakhala momwe Mulungu anakupangirani inu. Mukuona? Musati muzidziyesera kudzipanga nokha chinachake chimene inu simuli. Zingokhalani anthu anthu. Izo si zoipa? Chabwino mwinamwake izo zayankha mafunso ena a winawake aponso.

²⁷ Atate athu, ife tikukuthokoza Inu lero chifukwa cha Yesu Khristu ndi chifukwa cha kuwongoka kwa Mawu uku. Monga ine ndikukuwonerani Inu mwanjira kwambiri mukuwapangitsa mawu amenewo kufika pokwaniritsidwa, izo zikundipangitsa ine kukhala wotsimikiza mochuluka kuti ndikhalabe ndi Choonadi ndi mawu aliwonse a Choonadi. Kotero ine ndikupemphera, Atate, kuti Inu mutidalitse ife mmawa uno, anthu okondeka awa. Ndipo podziwa kuti tepi iyi ikupita mu malo osiyana kumene ati akaimve iyo ngakhale ndemanga imene yangopangidwa kumene ija. . . ine sindinati—izo sindinazichite mokonzekera; Inu mukudziwa mtima wanga. Izo zinangobwera apo mu malingaliro anga, ndipo ine ndikukhulupirira Inu mumafuna kuti ine ndinene izo. Ndipo ine ndazinena izo, ndipo izo zatha tsopano. N—ndipo izo ziri ndendende kukhudzidwa kwanga ndi zimene ine ndikukhulupirira kuti Inu mwandipangitsa ine kuzinena.

²⁸ Mulole mkazi aliyense amene adzamva izo kudutsa mu maiko ndi kuzungulira fukoli ndi padziko; iye atakadzichitira yekha manyazi ndi kuwona zimene zachitika, ndi kumakaziveka yekha ngati dona ndiye, kuti iye asakhale ndi mlandu wa chigololo. Cholengedwa chokongola, chokondeka monga Inu mwachipereka, gawo la mwamuna, kuti akhale mwanjira imeneyo k—k—kuti azikakopera tcheru cha mwamunayo kwa iye, awiriwo azikhala mmodzi, chifukwa iye anachokera mwa mwamunayo. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti mkazi

azindikire kuti kukongola kwake ndi chimene iye ali, kuli kongoperekedwa kwa mwamuna wake yekha. Perekani izi, Atate.

²⁹ Ife tikupempha kuti Inu mutithandize ife tsopano pamene ife tikuyesera kuti tiwafotokoze mafunso awa. Ndife osakwanira pa zinthu izi, koma mulole Mzimu Wanu wawukulu ubwere, Ambuye, umene uli chotikwaniritsa chathu; ndipo Iwo utayankha funso mu mitima yambiri. Ife tikukuthokozani Inu pa zimene Inu mwatipatsa ife: *Mibadwo ya Mpingo*, ndi *Zisindikizo*, ndi. . . O, momwe Inu mwachitira nafe mu zinthu zazikulu zamphamvu zomwe zakhala zazikulu kwa ife, Ambuye, chifukwa ife tikuwona nthawi yamapeto ikuyandikira.

³⁰ Tsopano, n—ndimaganiza kuti zinali zopindulitsa kapena zikanakhala zopindulitsa kwa Ufumu Wanu ngati ine ndikanafufuza pa anthu. Nthawi zambiri pansu pa kuzindikira za mmitima ndi kuwona zinthu zambiri zosiyana, ndipo iwe sungathe kusamalira pa chimodzi cha izo; koteru poganiza—ine ndinangowalola iwo kuti alembapo zimene iwo amaganiza pa mtima wawo. Ndiyeno ine ndikhoza kulongosola malingaliro awo kuchokera pa chidutswa cha pepala chimene iwo alembapo, ndiyeno Inu mutipatsa ife yankho loyenera. Ife tonse tikudikirira, Ambuye. Bwerani mu kukhalapo kwathu, Ambuye, ndipo yendani chokwera ndi chotsika mu mipita, ndi kuchita naye aliyense molingana ndi chifuniro Chanu. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu. Amenii.

[Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Terry, kodi ine. . . Kodi izo zikubwerabe, kumeneko pa m'bale. . . ine ndinakhudza. . . Kodi ichi chikuzimitsa izo, kapena chirichonse? Icho sichikuvutitsa. Ine ndinakhudza icho ndi dzanja langa. Ine sindimadziwa.

³¹ Tsopano, pamene ine ndikunena mobwereza tsopano, pamene ife tikuyamba, kwa—atumiki awo kapena anthu mu magawo osiyana a dziko, kapena amene ati adzamvere tepiye, i—inu ndi (ngati tepiye ili bwino bwino)—awa ndi mafunso a pa mitima ya anthu amene ali akuno pa kachisi uyu, kumene ife tiribe chipembedzo, timangokhala ndi chiyanjano wina ndi mzake. Ndipo ine ndikudalira kuti izo zikhala ziri z—zichotsa maganizo athu, kuti ife tidziwa zoti tizichita ndi kudziwa momwe tingamakhalire bwinoko mafunso athu akayankhidwa. Ine ndikudziwa, pa kungowawerenga iwo, iwo anali mdalitso kwa ine.

³² Tsopano, ine ndangowawunjika iwo apa mu mulu, ndipo ine ndiziyang'ana ndipo pafupi maminiti faifi kuti ikwane 12, ine ndibalalitsa. Ndiyeno, nkubwereranso madzulo ano pa hafu pasiti sikisi.

Funso loyamba limene ine ndiri nalo, ine ndikukhulupirira kuti ndi mafunso asanu mondondana, olembedwa motaipa pa kachidutswa ka pepala kachikasu.

236. Kodi izi zikutanthauza chiani? Mateyu 24:19: “Tsoka kwa iwo amene ali ndi mwana, ndi kwa iwo amene azidzayamwitsa mu masiku amenewo!”

Mwachilendo, posadziwa kuti, ine ndinena izi pokhudza mkazi, ndipo ndi izi mu nthawi ino, funso loyamba.

³³ Tsopano, Mateyu 24:19. Yesu anali atafunsidwa mafunso atatu. Mu mafunso amenewa munali zakuti: Ndi liti pomwe iti idzakhale nthawiyo pamene sipadzakhala mwala umodzi utasiyidwa pa umzake? ndi, Nchiani chiti chidzakhale chizindikiro cha kutha kwa dziko? n—ndi mafunso atatu osiyana Iye anali—Iye anafunsidwa. Ndipo Iye akuyankha izo mwa njira zitatu zosiyana, akuyankha funso lirilonse. Kodi zidzakhala liti pamene sipadzakhala mwana umodzi pa umzake? Ndipo chidzakhala chiani chizindikiro cha kudza Kwanu? Ndipo ndi chiani chomwe chiri chizindikiro cha kutha kwa dziko? Ndipo Iye akuyankha izo mwa njira zitatu zosiyana. Iye akuwauza iwo pamene nthawi iti idzafike pamene sipadzakhala mwala umodzi pa umzake; chomwe chiti chidzakhale chizindikiro cha kudza Kwake; ndiyeno, pa kutha kwa dziko. Ndipo nthawi zambiri, ngati inu simungati muyang’anitsitse mwatcheru, tsopano, momwe Iye akuyankhira (mwaona?), inu mungatenge izo mosokonezedwa ndi kuziponyera izo zonse mu nthawi imodzi; ndiye inu mwasokonezeka yense.

³⁴ Tsopano, mopanda kunyozetsa kwathu—kwa abale athu achi Adventist amene amazitenga izi momwe ziriri kuti ndi za mtsogolo. Polowa mu phunziro ilo la tsiku lachisanu ndi chiwiri: “Pempherani ndiponso kuti kuthawa kwanu kusadzakhale mu nthawi yachisanu kapena pa tsiku la Sabata,” anati (mwaona?), iwo adzakhala akusunga apobe Sabata. Si kuwaponyera kumbali abale amenewo, izo sizikanakhala monga-Mkhristu kuti ndichite zimenezo, koma pongolinga kuti ndiziwongole izo apo. Mukuona?

³⁵ Zingatheke bwanji kuti dziko lonse la Chikhristu lidzasonkhane mkati mwa khoma, ndipo makomawo sali kutsegulidwa ndi kutsekedwa monga iwo ankachitira apo. Mwaona? Ndi kusiyanana kwanji komwe izo zikanati zidzapange, kuti kaya itakhala nthawi ya chisanu kapena nthawi ya chirimwe kwa anthu amene amakhala mudera lotentha. Mukuona? Izo zinali basi kwa Israeli yekha. Ndizo pansi pa nthawi pamene sipakanadzakhala mwala umodzi utasiyidwa pa umzake. “Tsoka kwa iwo amene ali ndi mwana, ndi kwa iwo amene adzakhala akuyamwitsa mu masiku amenewo,” chifukwa mayi amene ali ndi mwana (mukuona?), zikanakhala ziri zovuta kuti iye athamange, ndi kwa iwo amene ali kuyamwitsa kwa ana

awo kuti awanyamule iwo, chifukwa iwo akanati achokere ku Yerusalemu kutuluka mu mzinda kupita mu—mpaka mu mapiri a Yudea.

³⁶ Ndipo tsopano, ine ndikhoza kungokhala mmawa wonse pa chinthu chimodzi icho pamenepo, kungoti ndichipange icho kumveka; koma ine ndingoyesera kuti ndigunde malo apamwamba amene ine ndingathe, mpaka izo zifike kwa anthu, ndiyeno nkupita ku funso lotsatira.

³⁷ Tsopano, Yesu anali atawauza iwo kuti iwo a . . . “Pamene inu mudzawona Yerusalemu atazingidwa ndi ankhondo, ndiye siyani iye amene ali mmunda, asati abwererenso mu mzinda kuti adzatenge chikhotho chake, kukatenga china chirichonse kuchokera mnyumba mwake; asati abwererenso mu mzindawo konse, koma athawire mu Yudea, pakuti iyo idzakhala ili nthawi yavuto siinakhalepo chiyambireni cha dziko.” Ndipo zonse izo zinafika pochitika mu masiku pamene mkulu wankhondo wa Chiroma, Tito, anazinga Yerusalemu, anawutentha mzindawo, ndipo uko kunali kokha—ndipo anawapha anthuwo mpaka magazi anataikira pa zipata ndi kuyenderera k—kupita mmisewu. Iye anawuzinga iwo. Ine sindikudziwa basi zaka zingati zomwe zinali, zomwe iye anangowatenga ankhondo ake ndipo anabwera uko ndi kudzangomanga msasa kuzungulira mzindawo. Ndipo ngakhale anthuwo, akazi, ankawawiritisa ana awo omwe ndi kumawadya iwo, kudya makungwa natha pa mitengo, maudzu nkutha pa nthaka. Izo zinali chifukwa cha kuwakana Mawu. Ndi zimene zinachititsa izo. Ndiyeno . . .

³⁸ Tsopano, awo amene anali atawalandira Mawu, monga Josephus, wazambiriyakale wamkulu akulembera . . . Iye anawatcha iwo okudya nyama ya anthu, anati iwo ankadya thupi la Mwamuna wotchewa Yesu waku Nazareti, amene Pilato anamupachika; ndipo iwo anabwera usiku ndipo anadalibamo thupi Lake, ndipo anthu awa analitengera ilo kwina ndipo ankalidula ilo mziidutswa ndi kumalidya ilo. (Iwo anali kutenga Mgonero, inu mukuona. Iwo sanali kudziwa.) Izo zinangokhala zoyankhulidwa zinkapita mozungulira, momwe iwo aliri nazo lero za ife ndi Akhristu ena onse. Inu mukuona? Iwo amanena zinthu zimenezo, koma . . .

³⁹ Tsopano, anthu awo amene anali . . . Chifukwa, “Pempheerani kuti kuthawa kwanu kusadzakhale mu nthawi ya chisanu,” Yudea anali kuchita chisanu. Mukuona, Khrisimasi? Tsopano, Yesu anabadwa chotani kumeneko ndiye mu mapiri ochita chisanu awo? “Pempheerani kuti kuthawa kwanu kusadzakhale mu nthawi ya chisanu, ngakhalenso pa tsiku la Sabata,” mwaona, chifukwa pa tsiku la Sabata zipata zinali kutsekedwa, ndipo iwo akanati adzagwidwe mu msampha wawo womwe. Ngati Tito anakafika uko l—l—Lachisanu madzulo, iwo akanati azingidwe mkati umo chifukwa cha Sabata, chifukwa zitseko zinali kutsekedwa. Zipata zinali kutsekedwa pa Sabata ndipo

sanali kuzitsegula. Uko kunalibe kulowa umo ndi kupita kunja kwa mzindawo pa tsiku la Sabata.

⁴⁰ Ndipo tsopano, inu mukuona zimene zinachitika? Ndiye Iye anati, “Tsoka kwa iwo amene ali oyembekezera, ndi kwa iwo amene adzakhala akuyamwitsa mu masiku amenewo,” (mukuona?) chifukwa kuthawa ndi kuthamanga... Ndipo malingana ndi mbiriyakale, uko kunalibe mmodzi wa iwo amene ankakhulupirira mwa Yesu nawakhulupirira Mawu koma amene anali kuyang’anira kuti izo zichitike. Ndipo iwo anathawa, ndipo anapita kuchokera ku Yerusalemu kupita ku Yudea, n—ndipo anathawitsa miyoyo yawo, ndipo palibe mmodzi wa iwo... chifukwa iwo anachenjezedwa ndi M’busa wawo ndipo anali kuyang’anira ora limenelo kuti libwere. Pamene iwo anamva kuti Tito anali kubwera iwo anachokako, anathawitsa miyoyo yawo, ndipo anatulukamo mu mzindawo.

Tsopano, funso lina likutsatiralo.

237. Mateyu 24:24: “Ndipo pamenepo adzawuka aneneri abodza—ndi akhristu abodza, ndi aneneri abodza, ndipo azidzawonetsa zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa.” Kodi ife tidzawazindikira bwanji iwo?

⁴¹ “Pamenepo adzauka...” Mmenemo tsopano inu mukubwera mpaka mu m’badwo wina. Mwaona? “. . . padzauka akhristu abodza ndi aneneri abodza.” Khristu wabodza ndi wodzozedwa mwabodza, chifukwa Khristu ndi Wodzozedwayo. Ndi angati akudziwa kuti *Khristu* amatanthauza “Wodzozedwa uyo”? Padzakhala pali odzozedwa mwabodzawo, ndipo iwo azidzadzitcha okha aneneri. Koma kodi inu muzidzawazindikira chotani iwo? Mwa Mawu; ndi momwe inu mumawaziwira iwo, mwa Mawu, ngati iwo akulondola. Kodi ife tidzawazindikira chotani iwo? Zidzakhala mwa Mawu. Ngati iwo ali... Ngati iwo akunena kuti iwo ali nawo Mawu, ndiyeno nkumawakana Mawu, ndiye kulibe chirichonse kwa izo, ziribe kanthu zomwe iwo akuchita. Iwo akhoza kumachiza odwala; iwo akhoza kumatsegula maso a akhungu; ndipo nkumawakana Mawu, khalani kutali kwa izo. Musasamale chomwe izo ziri, khalani ndi Mawu amenewo mosasamala zina (mwaona?), chifukwa nthawi zambiri ine ndawonapo vuduu ndi mitundu yonse ya zinthu zikuchitika pansi—pansi pa machiritso.

⁴² Apa pali M’bale Sidney Jackson, Mlongo Jackson mmawa uno ochokera ku South Africa. Iye akhoza kuima pano ndi kutenga phunziro limenelo ndi kukuuzani inu kwenikweni zinthu zina za zimenezo kumeneko. Bwanji zedi, anthu amabwera kwa mafano ndipo amachiritsidwa. Mukuona, chifukwa chiani?

⁴³ Monga momwe Dr. Hegre anandinenera ine nthawi ijayi, zakuti ine ndimanena kuti mdierekezi sangathe kuchiza. Ndipo iye anati, “Munthu amene umaima pamaso pa anthu ochuluka

momwe iwe umachitira, ndi fioloje yoperewera choncho,” anati, “kumanena kuti mdierekezi sangathe kuchiza.” Anati, “Ife tiri naye mkazi mwa oyandikana naye momwe amavala apuroni pa iye, ndipo amapita kumeneko; ndipo anthu amabwera momuzungulira iye ndipo amayenera kuti aziponyera ndalama mu apuroni iyo; ndiyeno iye amawasisita iwo ndi kuthothola tsitsi pa mutu wake ndi magazi kuchokera mu misempha yawo n—ndi kuziika izo pa tsitsi ndipo amaziponyera izo kumbuyo kwake; ndipo iye akakakamizidwa kuti atembukire mmbuyo, matendawo amabwereranso kwa anthuwo. Ndipo,” anati, “sate pa zana a iwo amakhala bwino. Ndiyeno iwe ukuti mdierekezi sangathe kuchiza?”

44 Ndipo ine ndinaganiza, “O, mai!” Ine ndinamulemba iye momuyankha, ndipo ine ndinati, “Wokonedwa bwana.” Ine ndinati, “Ndi chinthu chachirendo kwa ine kuti mphunzitsi wa sukulu yaukachenjeda ya Chilutera angakhazikitse fioloje yake pa chomuchitikira mmalo mwa Mawu a Mulungu.” Mwaona? “Mawu a Mulungu amanena kuti Satana sangathe kutulutsa Satana. Izo zikukhazikitsa izo; Yesu ananena chomwecho.” Ngati Satana. . . Ndinati, “Ndiye inu mukhoza kudabwa momwe anthu awa amachiritsidwira podzera mzimenezo, mfiti imeneyo, ndi chifukwa chakuti anthuwo eniakewo amaganiza kuti iwo akufikira kwa Mulungu podzera mwa mfiti imeneyo. Ndipo machiritso amakhazikitsidwira pa chikhulupiriro, osati pa momwe iwe uliri wolungama, momwe uliri wabwino, kuchuluka kwa momwe iwe umasungira malamulo, kapena chirichonse chimene chiri, iwo amakhazikitsidwira kwathunthu pa chikhulupiriro. ‘Zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira!’ Mwaona? Izo siziri pamaziko a momwe iwe uliri wabwino. Ine ndawawonapo achiwerewere akubwera pa guwa ndi kuchiritsidwa nthawi yomweyo ndipo mkazi woyera kudutsa pa nsanjayo nkuwaphonya iwo. Zedi, iwo ali pa maziko a chikhulupiriro, ‘Ngati inu mungati mukhulupirire,’ osati pa kulungama.”

45 Yang’anani kumusi uku mu France kumene iwo amapita ku guwa lija la mkazi uja, amapita mmenemo ali mu zikulu ndipo amatulukako akuyenda, osati pa chinachake koma zamatsenga mwangwiro, ngati chiri chirichonse, zamizimu—pa kupembedza munthu wakufa. Mwaona? Ndipo komabe iwo amachiritsidwa, chifukwa iwo amaganiza kuti iwo akufikira kwa Mulungu. Tsopano, sikuti ndikuwanyozetsa anthu Achikatolika, ine ndikunyozetsa kachitidwe ka Chikatolika, monga momwe ine ndikuchitira ndi kachitidwe ka Chiprotestanti (mwaona?), zinthu zonse izi.

46 Tsopano, atumiki, ine ndikudziwa kuti izi ziyamba kukung’ambani inu, koma ine ndikuyankha mafunso; ndipo ine ndiku—ine ndikufuna kuti inu mumvetse kuti (mwaona?) ine ndikungo—ndikungokuuzani inu Choonadi kuchokera

mu mtima wanga; Khristu patsogolo panga mwakukhoza kwa kudziwa kwanga. Mwaona? Ndi kachitidwe konseko, ndipo kachitidwe kameneko kawapiringiza anthu ngati... Anthu amapita ndi kukajowina Chimethodisti, Chibaptisti, Chiprebateria, Chipentekoste, Chikatolika; ndipo iwo amaganiza kuti iwo akufikira kwa Mulungu pamene iwo akungopita kudutsa mu kachitidwe. Mulungu amalemekeza izo nthawizina ndipo amawachotsera—matenda awo kuwachotsa kwa iwo kudzera mu mafano. Chabwino, uko komwe kwa Akafula aku Afrika iwo analandira machiritso ndi mafano ndi zina zotero (mwaona?), koma iwo amaganiza kuti akufikira kwa Mulungu.

⁴⁷ Inu mukuganiza kuti nani wa Chikatolika amapita ndi kukajowina—unani wa Chikatolika chifukwa kuti iye akufuna kuti akhale mkazi woipa? Iye amakajowina unani umenewo chifukwa kuti iye akufuna kuti akhale mkazi wabwino. Mwamuna samapita kukajowina mpingo wa Katolika basi kuti akhale mwamuna woipa; iye amapita kumeneko kukajowina kuti akhale mwamuna wabwino. Inu simuma... Kutu, “Chabwino, ndi chiani ichocho?” Ngakhalenso awo—ngakhalenso Amwenye aku India, kapena Achihindu samajowina Chihindu kuti akhale munthu woipa.

⁴⁸ Pamene ine ndinapita mu kachisi w—wa Chijaini, kumene ine ndinafunsidwa kumeneko ndi wansembe—wonga papa atakhala pa pilo wamkulu, mapazi ake atapiringizidwira pansu pake, atagwira zala zake za kuphazi—ndi kupenya koteroko mwakuti iye amalemba chofanizitsa ndi Lemba la Masalmo 23 ndi maso ake akuyang’ana apoyera pa chidutswa cha chitsulo chimene chinali chochepera kuposa—chosakula kuposa kotala la inchi. Tsopano, ndipo izo ndi zopitirira kulingalira kwa umunthu kulikonse kuti alembe zimenezo, ndipo iye anazizokota izo pamenepo ndi maso ake achibadwa; ndipo iye anali mwamuna wa usinkhu wa zaka forte kapena kupitirira. Mwaona?

⁴⁹ Bwanji zedi, i—inu mumangokhala mozungulira apa, mumangomvera za Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria; inu mukuyenera kuti muzituluka ndi kupita ku minda ya umishoni nthawi ina. Kukawona zinthu zoti zikutseguleni maso anu! Mwaona?

⁵⁰ Tsopano, inu mukuganiza kuti masisitere onse aja atakhala uko; iwo samati nkomwe—iwo samaphika; iwo samadya; iwo amachita kupempha chirichonse chimene iwo amalandira. Iwo sangati—iwo amakonza zikolopa zazing’ono ndi manja awo kuti azikolopera nyererere ndi zinthu kuzichotsa pa msewu, chifukwa iwo amakhulupirira kusintha kwa cholengedwa; iwo akhoza kukhala akuponda pa wachibale wawo. Samaponda pa nyererere, samapha ntchentche, kapena kalikonse; samatenthetsa nkomwe mpeni kuti achite opareshoni pa chala. Amamusiya munthuyo

kuti afe, chifukwa iwo akapha jeremu; iyo ikhoza kukhala ili w—wachibale wawo wina atabwereranso. Mwaona? Iwe umapitirira kukhala bwinoko, ndi bwinoko, bwinoko; potsiriza iwe umadzakhala munthu wokhalapo, munthu wokhalapo wabwinoko, ndipo popitirira pitirira monga, mpaka iwe umadzakhala kamulungu. Kumangopitirira pitirira pitirira, ndi, kumasintha, kumakhala wabwinoko ndi bwinoko.

⁵¹ Tsopano, iwo samachita zimenezo kuti akakhale anthu oyipa. Iwo amachita zimenezo ndi kuonamtima, koma inu mukuona, “Pali njira imene imawoneka yolondola kwa munthu.” Pali chinthu chimodzi chokha, anthu, chimene ine ndikudziwa kuti ndikuuzeni inu ng—ngati kalasi mmawa uno pa mafunso amenewa, ndicho Mawu, Mawu a Mulungu. Ndiye inu muzikhulupirira kuti Yesu Khristu ali Mawu amenewo, ndipo Mawu amenewo apangidwa thupi pakali pano pakati pathu, kukwaniritsa ndendende zimene Iye anati Iye akanadzachita mu m’badwo uno. Chabwino.

Tsopano, umo ndi momwe inu mumawadziwira iwo, osati mwa mpingo wawo, osati mwa kachikhulupiro kawo, osati mwa chizindikiro chawo, osati mwa zipembedzo zawo, osati mwa machiritso aliwonse, osati mwa chirichonse, koma mwa Mawu. Mwaona?

238. Mateyu 24:26 (lotsatira) akuyankhula za “chipinda chinachake” ndi “mu malo a mchipululu.” Kodi izi zikutanthauza chiani?

⁵² Izo zikutanthauza kuti kudzakhala kuli wotsutsakhristu, wotsutsa-kudzozza, zina zotero. Ndipo kodi *anti* ndi chiani? *Anti*-ndi “kutsutsa.” Zidzakhala zolengedwa izi zomwe zikuwatsutsa Mawu. Ndipo izo zidzakakhala ziri ku chipululu ndi mu zipinda zobisika.” Ndiye Iye anati, “Musati muzipita mozidzatsatira izo. Zikhalani kutali ndi izo.” Mwaona?

Tsopano, funso lachinai:

239. Mateyu 24:28: (Munthuyo akubwera nazo ndithu mmusi. Iwo sanalembeo dzina apo; inde iwo atero. Ine ndikhululukireni. Ine sinditchula maina amenewa, chifukwa si zofunikira. Mukuona?) Mateyu 24:28: “Pakuti kulikonse kumene kwafa nyama, kumeneko mphungu zimadzasonkhana palimodzi.” Kodi nyamayo ndi ndani ndipo mphunguzo ndi ndani?

⁵³ Tsopano, limenelo ndi funso labwino, palibe cholakwika ndi zimenezo! Kodi nyamayo ndi chiani? Nyama ndi chomwe mphungu zimadyapo. Tsopano, mphungu imatengedwa mu Baibulo, mneneri. Mneneri ndi mphungu. Mulungu—Mulungu amadzitcha Iyemwini mphungu, ndipo ife ndi “timphungu” ndiye, o—okhulupirira. Inu mukuona? Ndipo kodi nyama ndi chiani imene iwo amadyapoyo? Iyo ndi Mawu. Kulikonse kumene kuli Mawu, chikhalidwe choona cha mbalame

chimadziwonetserako chokha. Mwaona? Mphungu, imene imafuna nyama yatsopano, iye amayenera kukhala ndi nyama yake yatsopano. Iye si k—khungubwe (mwaona?), iye ndi mphungu. Inu simungatengere zinthu zachipembedzo kwa iye; iye amayenera kukhala ndi chakudya cha mphungu; imeneyo ndiyo nyama yatsopano kwambiri, osati zimene Mose anazichita, osati zimene winawakenso anachita, osati zimene Sankey, Finney, Knox, Calvin, koma pakali pano, Nyama imene yaphedwera kwa tsiku lino. Ndipo limenelo ndilo gawo la Khristu amene anafera kuti awapangitse Mawu awa kuti atsimikizidwire. Ndi chimene iwo amadya pa icho. Mukumvetsa zimenezo? Onani, mwaona?

⁵⁴ Osati zimene Nowa anachita, zimene Mose anachita, izo zinali zitsanzo; ife timawona ndi kuweringa zimene iwo anachita, koma ndi zimene Iye analonjeza kuti azichita tsopano. Iye anali Mawu kumbuyo uko; imeneyo inali Nyama ya tsiku limenelo. Tsiku l—la Wesile panali nyama ya tsiku limenelo; tsiku la Lutera panali nyama ya tsiku limenelo; koma iwo sabwerera mmbuyo kwa iyo. Imeneyo yavunda kale. Zimene zinasiyidwa ziyenera kuti ziziwotchedwa, monga za Mgonero ngakhalenso; musati muzisiyira izo kwakam’badwo kotsatira. Baibulo linati pamene inu mutenga Mgonero, zimene zatsalira za iwo, musati ngakhale muzisiye izo mpaka mmawa; muziziwotcha izo. Koterotizilozera mmbuyo kwa izo? Ayi, bwana! Ife tiri ndi Chakudya chatsopano lero; amenewo ndi Mawu amene alonjezedwera kwa ora lino, akhale akuwonetseredwa mu ora lino. Ndiko kumene mphungu ziri—kumene kuli nyama. Ife tikanakhoza kukhala nthawi yaitali pa zimenezo, koma ine ndikutsimikiza inu mukumvetsa zimene ine ndikutanthauza.

Chabwino, funso lachisanu:

240. Kodi Mkwatibwi adzasonkhanitsidwa palimodzi mu malo amodzi pa mkwatulo, ndipo kodi izo zidzakakhala Kumadzulo?

⁵⁵ Ayi, sizikusowa kuchita kukakhala kumeneko. Eya, Mkwatibwi adzasonkhana palimodzi mu malo amodzi. Izo ndi zoon, koma osati chisanachitike chiukitsiro. Mwaona? “Pakuti ife amene tiri amoyo ndipo titatsalira mpaka ku kudza kwa Ambuye. . .” Aefeso—II Atesalonika mutu wa 5, ine ndikukhulupirira ndi pamene pali. “Ife amene tiri amoyo ndipo titatsalira mpaka pa kudza kwa Ambuye sitidzawalepheretsa (kapena kuwatchinga) iwo amene akugona (konsekonse); pakuti lipenga la Mulungu lidzawombedwa, ndipo akufa mwa Khristu adzauka, ndipo ife tidzakwatulidwira mmwamba palimodzi ndi iwo kukakomana nawo Ambuye mu mlengalenga.” Chotero, Mkwatibwi yense adzakhala palimodzi pamene Iye akupita kukakomana nawo Ambuye. Mwaona? Iye adzakhala palimodzi, koma izo sizikutanthauza kwenikweni kuti ife—iwo onse adzakhala ali mu malo amodzi monga chonchi; chifukwa

Mkwatibwi akugona mu fumbi la dziko lapansi kuzungulira mdziko, kuchokera kozizira mpaka kotentha, ndiponso k—kuchokera kummawa mpaka kumadzulo, kuchokera kumpoto mpaka kummwera.

⁵⁶ Yesu anati, “Pamene Mwana wa munthu ati adzawonekere,” pakuti anati, “izo zidzakhala monga kuwala kumene kumawala kuchokera kummawa ngakhale mpaka kumadzulo.” Chinthu chonsecho, apo padzakhala pali chiukitsiro, mkwatulo, ndipo kutali Iye adzapita. Ndipo Iye asanapite konse mmwamba kukakomana naye Iye . . .

⁵⁷ Tapenyani nzeru ya Ambuye. Tsopano, tiyeni tinene, mwa chitsanzo, poyankhula izi . . . ine ndikunena izi kudzera mu malingaliro a chisomo ndi chikhulupiriro mu Mawu, pamene ine ndikuti “ife.” Ine ndikudziponyera ndekha mmenemo ndi inu nonse ndipo ine—ndi Thupi lonse la Khristu, konsekonse. I—ine ndikukhulupirira zimenezo. Pamene ine ndikuti “ife” ndiye, ine ndikutanthauza, mwa chisomo i—ine ndikuzikhulupirira zimenezo. Mwa chikhulupiriro ine ndikukhulupirira izo mwa chisomo Chake, kuti ife tidzakhala tiri pakati pa anthu amenewo amene ati adzakwatulidwire mmwamba.

⁵⁸ Tsopano, chinthu choyamba chimene chikuchitika pamene ife taukitsidwa . . . Iwo amene ali amoyo adzakhala basi alipobe . . . Chiukitsiro chidzakhala uwo poyamba, chiukitsiro cha iwo amene akugona. Padzakhala pali nthawi yogalamuka, ndipo iwo amene ali kugona mu fumbi tsopano, osati iwo amene akugona mu tchimo, chifukwa iwo azidzagona mopitirirabe. Iwo sakuuka mpaka zaka chikwi zina. Koma iwo amene ali—amene akugona mu fumbi adzazutsidwa poyamba, ndipo iwo adza—matupi achivundi awa adzavala chisavundi mu chisomo chokwatulitsa cha Ambuye. Ndiyeno ife tonse tidzabwera palimodzi. Ndipo pamene iwo adzayamba kubwera palimodzi, ndiye ife amene tiri amoyo ndipo titatsalira tidzasinthidwa. Matupi achivundi awa sadzawona imfa, koma basi mwadzidzidzi, padzangokhala ngati kusesa kwapita pa ife, ndipo inu mudzasintha. Inu mudzasintha nkubwerera monga Abrahamu anachitira, kuchokera ku mwamuna wachikulire kukhala mwamuna wamng’ono, kuchoka ku mkazi wachikulire kukhala mkazi wamng’ono. Nchiani kusintha kwadzidzidzi uku? Ndipo pakapita kanthawi i—inu mukuyenda ngati lingaliro, ndipo inu mukutha kuwawona awo ndiye iwo awukitsidwa kale. O, ora lakelo! Ndiye ife tidzasonkhana limodzi nawo ndiyeno nkukhala titakwatulidwira mmwamba limodzi nawo kukakomana nawo Ambuye mu mlengalenga.

⁵⁹ Si zofunikira ayi, ngati amalume ako anaikidwa uko kummwera kwa Kentucky, ngati iwo ali woti abweretsedwe mu Indiana, kapena ataikidwa mu Indiana kuchita kutengedwera kummwera kwa Kentucky. Ziribe kanthu kumene iwo ali . . . Iwo amene anafera mnyanja adzauka kuchokera mu nyanja. Iwo

amene anawonongedwa mu bwalo lija nadyedwa kwathunthu ndi mikango, iwo amene anaponyedwera mu ng'anjo ya moto ndipo palibe ngakhale mafupa adzakhale atasiyidwa kapena fumbi, iwo adzawuka apobe! Kaya iwo anali ku Roma, kapena bwalo la ku Roma, kapena kaya iwo anali ku nkhalango zotentha za Kummwera, kapena mu zigawo zachisanu za Kumpoto, iwo adzawuka kuchokera kwa akufa ndi kusinthidwa ndi kukuwitsidwa; ndipo amoyo adzasinthidwa mu kamphindi, mkutwanima kwa diso ndi kukwatulidwira mmwamba palimodzi.

⁶⁰ Tayang'anani pa amishonare amene anafera uko mu minda ya ku Afrika. Tayang'anani pa iwo amene anafera uko m—mu—zigawo zachisanu za Kumpoto. Tayang'anani pa iwo amene anafera mu bwalo, konsekonse mdziko monse, ku Congo, ndi konse kuzungulira dziko. Iwo anafera kulikonse, China, Japan, kuzungulira dziko; ndipo kudza kwa Ambuye kudzakhala kwa konsekonse, mkwatulo uwu udzatero.

⁶¹ Penyani kusinthako. “Adzakhala ali awiri mu kama; ine ndidzatengapo mmodzi ndi kusiyapo mmodzi,” mphindi yomweyo, “Adzakhala ali awiri mmunda; ine ndidzatenga mmodzi ndi kusiya mmodzi,” mmodzi kumbali yamdima ya dziko ndi wina ku mbali yowala ya dziko. Mwaona? Iwo udzakhala mkwatulo wa konsekonse. Inde, Mpingo wonse udzakhala uli palimodzi, koma chitachitika, chitachitika chiukitsiro ndipo mkwatulo utalowamo.

⁶² Tsopano, ngati umo si momwe inu mukuziwonera izo, bwanji, zonse ziri bwino tsopano. Ine sindiri kuyankhula ndendende pamene ine ndikunena izo; ife tikujambula izi. Inu mukuona? Ndipo pakhoza kukhala atumiki ena amene akutsutsana nazo izo. Zonse ziri bwino.

241. Wokonedwa M'bale Branham, funso langa liri pa ubatizo. Ndi liti pamene munthu amapulumsidwa? Ine ndamvapo kuti ndi pamene munthuyo akhulupirira. Ena amanena kuti pamene iwe walandira Mzimu Woyera iwe wapulumutsidwa, ngakhale kuti iwe usanabatizidwe mu madzi, monga momwe zinaliri ndi Korneliyo pa Machitidwe 10:47. Ena amanena kuti Paulo anapulumsidwa pa njira yaku Damasiko, koma mu Machitidwe 22:16, amanena kuti iye anali akadali nawo machimo ake masiku atatu pambuyo pake. Kodi munthu angabatizidwe mwa Mzimu Woyera momwe Korneliyo anachitira, ndi kukhala nawobe machimo ake, pakuti iye anali asanalandire ubatizo wa madzi, pa—kapena kodi munthu samakhala ndi njira yopitira Kumwamba mpaka iye atalandira ubatizo wa madzi, ngakhale kuti iye ali nawo Mzimu Woyera?

⁶³ Tsopano, mzanga wofunika... Tsopano, m'bale uyu walemwapo dzina lake; ine sindikumudziwa iye, koma iye walemwapo dzina lake. Koma i—ine sinditchula maina ake, chifukwa izo si zofunikira; chifukwa anthu ena azifika kwa iwo nkumati, “Chabwino, i—ine sindikugwirizana nanu pa *izi* ndi *izo*.” Mukuona? Ndipo ine sindimatchula basi maina ayi. Zambiri za izi ziri nawo maina, koma i—ndi za kwa ine basi. Mwaona? Ine ndikuzibwezera izi mkati umu, kuti ine nditthe kuzisunga izo. Kotero ndi zolemba za buluu chotero; zina za izo ndi zotaipidwa ndi njira zosiyana.

⁶⁴ Tsopano, funso pano poyamba linali: “Ndi liti pamene iwe umapululumutsidwa?” Ndipo lotsa—lotsatira ili, “Kodi machimo angachotsedwe kunjira kwa ubatizo wa madzi, pakuti Kornelio analandira Mzimu Woyera—iye ndi apa banja ake—ndipo anali asanabatizidwe apobe mu madzi.” Ndipo Paulo anali asana—iye atakomana nacho chomuchitikira chake p—pa njira yaku Damasiko, iye, nayenso, anali akadali nawo machimo ake pa iye mpaka iye atabatizidwa; chifukwa iwo amati (ine ndawawerenga Malemba onsewa modutsa aponso kuti ndikhale wotsimikiza)... Ndipo kotero izo zinali... Iye anati, “Uka ndipo pita pomwepa molunjika ndi kukabatizidwa, kumatchula pa Dzina la Ambuye—ukabatizidwe, ukhale kuti machimo ako akhululukidwe (achotsedwe), n—ndi kumapita ukutchula pa Dzina la Ambuye.”

⁶⁵ Ndiyeno, “Kodi ubatizo wa Mzimu Woyera...munthu akhoza kubatizidwa ndi Iwo ndi kukhala uli nawobe machimo awo ndipo kusa—ndi kusabatizidwa mu madzi.”

⁶⁶ “Kodi njira ya munthu yotsimikizika kuti akupita Kumwamba pamene wabatizidwa, ngakhale iwo atakhala ali nawo Mzimu Woyera; komabe iwo ayenera kuti abatizidwe mu madzi, njira yawo isanakhale yotsimikizika kupita Kumwamba?” Tsopano, ine ndikukhulupirira... Tsopano, ine sindi—ine sindikumudziwa m'bale uyu, ndipo ilo ndi labwino kwambiri ndi funso la luntha. Ndipo ilo liyenera kuchitidwa nalo motalika, chifukwa ndi zofunikira kuti ife tizidziwa zinthu zimenezi. Mwaona?

⁶⁷ Tsopano, ine ndikukhala ngati ndikukhulupirira kuti m'baleyu mwina akunena kwa ine kapena akundipangitsa ine kuti ndinene izo (kapena mwinamwake iyeyo amakhulupirira mu zimenezo, ine sindikudziwa) ndi—za chinachake chimene ine ndiri kuganiza kuti chiri basi—pang'ono pokha mosiyana kwa chenicheni, chikhulupiriro choona mu Mawu. I...Izi zikumveka ngati kuti m'baleyu akuti... Tsopano, zomwe ziri zabwino bwino, M'bale; mukhoza kukhala muli pano; ndipo zimenezo ndi zabwino. I—ine ndikuganiza zimenezo ndi zabwino... Ine ndikukondwa kwambiri kuti inu munaziyika izo pamenepo. Tsopano, mwaona? Koma ine sindimakhulupirira mu kubatizidwa mmadzi kuti usinthike (mwaona?), chifukwa

pamene iwe utero, izo zimawadumpha Magazi. Mwaona? Iwe umabatizidwa mu madzi kuti uwonetsera kuti kusinthika kwachitika. Mwaona? Izo ndi zakunja chabe—chiphiphiritso cha kusinthika. Chinthu chonsecho chimakhazikika mwaulemu pa kukonzedweratu. Mwaona? Koma ife sitimadziwa amene ali ndi amene asali; chotero, ife timalalikira Uthenga. Mwa chikhulupiriro ife timangopita tikulalikira.

⁶⁸ Koma pa kusinthika tsopano, apo ndi pamene ine ndimasiyana ndi abale aumodzi. Ndipo inu abale aumodzi amene mukumvetsera tepi iyi ya mafunso, ngati iyo ingadzagwere mu ofesi yanu, kapena mu nyumba mwanu, kapena pakati pa inu anthu amene muli anthu aumodzi, musati mundimvetse molakwika ine, tsopano, kuti i—i—basi chifukwa chakuti ife sitigwirizana.

⁶⁹ Ine ndi mkazi wanga sitigwirizana; zedi ife timatero. Ine ndimamuza iye kuti ine ndimamukonda iye, ndipo iye amati sakukhulupirira kuti ine ndiri. Kotero nd—kotero ndiye ife ndithudi sitimagwirizana, koma ine ndikukuuzani inu, ife ndithudi timapitirira limodzi bwino bwino.

⁷⁰ Tsopano zindikirani. Mwinamwake ine sindimasonyeza zizindikiro zokwanira kwa iye, zimene ine ndimachita. Koma ine ndimakhala kunja ndikulalikira, ndiye ndikabwera kunyumba ndipo ndimatenga ndodo yanga yowezera ndi kupita kukawedza. Mukuona? Koma pansu mu mtima mwanga ine ndimamukonda iye; ine ndimangoyenera kuti ndikakhale kutali ndi iye, ndizo zonse.

⁷¹ Tsopano, zindikirani mu izi... Tsopano, ngati ife sitigwirizana, zonse ziri bwino; koma inu mukuona, madzi samachotsa machimo; ndi kuyankhira kwa ku chikumbumtima chako chabwino.

⁷² Tsopano, ine ndikukhulupirira chifukwa chimene Paulo anayenera kuti abatizidwe pamenepo, chifukwa ziri movomerezeka ndi zofunikira mu Baibulo kuti ife tizibatizidwa. Chifukwa ine nditenge mobwerera mmbuyo momwe kwa ichi ndiye: pamene wakuba anali atapachikidwa pa mtanda... Ndipo iye anafa wopanda kubatizidwa konse, ndipo komabe ali ndi lonjezo kuti Yesu akanati akakomane naye iye mu Paradiso tsiku limenelo—mu Paradiso, osati mu Madera a otaika, chifukwa inali nthawi yoyamba yomwe mwayiwo unaperekedwa kwa iye.

⁷³ Ndipo ine ndikukhulupirira zikhalidwe zomwezo zinali ndi mitima imeneyo ya aku nyumba ya Kornelio pamene iwo anali atalandira Mawu a Mulungu ndi kukondwera. Ndipo Mzimu Woyera ndiwo Mawu amenewo akapatsidwa moyo, ndipo Iwo anali atapatsidwira moyo kwa iwo. Ndicho chifukwa Mzimu Woyera unayamba kuyankhula mu malirime ena ndi

kumalosera. Inali mitima yolandira ya anthu imene Mawu anagweramo, powona zauzimu zonsezo.

⁷⁴ Ndi zimene zimandidodometsa ine lero mu ora ili limene ife tiri kukhalamo. Pambuyo pakuti gulu lija la Aroma linali lita—ndi Agriki, monga iwo anali, anali atangowona kuwonetseredwa kwa masomphenya kukutsimikiziridwa, Mzimu Woyera unadzidzimutsa kwambiri mitima imeneyo mpaka pamene Petro anali chiyankhulire mawu awa, Mzimu Woyera unagwera pa iwo. Mwaona?

⁷⁵ Monga ngati... Onani, Kornelio anati, “Pita ukamuitane...” Iye anali kenturio, ndipo izo zikuchokera ku “sentare” ndi zochokera ku zana. Iye anali woyang’anira amuna zana. Iye ndi senturio wa Chiroma; ndipo iye i—iye anawona masomphenya pamene iye anali akupemphera, ndipo Mngelo anabwera kwa iye. Iye anali mwamuna wabwino. Iye anati, “Pita uko ku Yopa. Simoni wina, wofufuta zikopa, ndipo kuli wina wotchedwa Simoni Petro. Iye ali pamwamba... Iwe ukamupeza iye kumeneko, ndipo iye abwera adzakuuze iwe Mawu.”

⁷⁶ Chabwino, iye anaganiza kuti masomphenya awo anali owoneka enieni kwambiri. “Ine sikuti ndinali ndikugona; ine ndinali ndikuyang’ana kumene pa—Mngelo.” Kotero iye anawatumiza asilikari ake ena okhulupirika kumeneko.

⁷⁷ Ndipo ali kumeneko, Mulungu anali akumukonzekeretsa mtumwiyo ku mapeto ena a mzere awo. Ndipo Iye anati, “Tsopano, dzuka.” Iye anati... Powona kuti iye anali pamwamba pa nyumba apo akuyembekezera—Mayi Simoni kuti akonze chakudya. Ndipo pamene iye anali pamenepo... Iye anali wa njala, mwinamwake pakuyenda, atumwi, kudutsa—mu zipululu. N—ndipo anali atagona pamwamba apo panyumba chisanafike chakudyacho, pamwamba pa nyumba, monga chinali chizolowezi. Akumachitabe chinthu chomwecho, amagona pamwamba pa denga apo, ndipo iwo amapita pansi ndi makwerero ndipo nthawizina masitepe ndi zinthu, kuchokera pa dengalo—kukhala pamwamba apo mu chisisira cha madzulo.

⁷⁸ Koma mtumwiyo anagona tulo, ndipo pamene iye anali akugona, iye anapita mopyola kugonako nalowa mu chizimbwizimbwi; ndiyeno iye anawona chinsalu chikubwera pansi chiri ndi zodetsedwa zonse ndi zinthu mmenemo, ndipo iye anamva Liwu likuti, “Dzuka, ipha ndi kuzidya.”

Iye anati, “Si choncho, Ambuye, palibe kanthu kanayamba kalowa mkamwa mwanga kali kodetsedwa.”

⁷⁹ Tsopano, onani, awo ndi masomphenya. Tsopano, penyani! Zimenezo zikuyenera kuti zitanthauziridwe. Tsopano, izo zikuwoneka ngati Petro apita paulendo wokasaka ndipo akapeza mtundu wina wa nyama imene iye sanayambe wadyapo kale ndi kudzayesera kuti ayidye iyo. Iye anati, “Si choncho,

Ambuye, i—ine sindinayambe ndakhala ndi chirichonse chosayera chinabwera mu milomo yanga.”

⁸⁰ Iye anati, “Usati uzitche izo zoyera zimene ine ndazipanga—zosayera zimene ine ndazipanga kuyera.” Anati, “Dzuka, kuli amuna akukudikirira iwe pa chipata. Pita, usati ukaikire kalikonse.” Nthawi yomweyo iwo anali akugogoda pa chitseko. [M’bale Branham agogoda pa guwa—Mkonzi.]

⁸¹ Tsopano, mwaona? Ndiyeno pamene iye anamupeza mwamuna uyu pamenepo, asilikari okhulupirika awa, basi mogwirizana ndi masomphenya. . . Ndipo apa iwo anabwerera ndi mwamuna yemweyo amene Mulungu anali atamunena mu masomphenya—munthu wosadziwika, nsodzi wamng’ono basi wosadziwika. Koma pakati pa gulu laling’ono ilo, izo zinali zodziwika kwambiri kuti iye anamupeza nsodzi wamng’ono uyu. Ndipo ndi uyu apa akubwera kuno kudzalowa mu nyumbayi tsopano, malo omwewo amene iye anawona masomphenya. Kornelio anawasonkhanitsa anthu onse palimodzi nati, “Pakuti, ziri ndendende basi momwe ine ndinaziwonera izo.” Ndiyeno Petro anaimirira apo ndipo anayamba kuyankhula momwe iwo analandirira Mzimu Woyera, ndipo pamene iye anali chiyankhulire. . . ! Iwo anawona chirichonse mwangwiro kwambiri mu dongosolo la masomphenya amodzi. Gulu la anthu amene anali Amitundu, amene anawaona masomphenya amodzi akuwonetseredwa, ndipo iwo anamva Mawu a Choonadi a momwe iwo akanati alandirire Moyo; ndipo Mzimu Woyera unagwa pa iwo asanabatizidwe nkomwe.

⁸² Kodi izo zikuyenera kuchita chiani kwa kachisi uyu mmawa uno? Odwala, osautsika, akhungu, ogontha, osayankhula, w—wochimwa, chirichonse. . . Tangoganizani, kuchokera mwa zinthu zikwi khumi, palibe nthawi imodzi zinayamba zalepherapo dontho limodzi! Bwanji, izo zikuyenera kuyatsa mitima yathu lawilawi!

⁸³ Tsopano, tsopano, iye apobe, pamene anali chiyankhulire mawu awa, Mzimu Woyera unagwa. Ndiye Petro anati, “Kodi ife tingaletse madi, powona kuti awa alandira Mzimu Woyera monga ife tinachitira.” Ine ndikukhulupirira machimo awo anali atapita kale, pakuti Mzimu Woyera sukanati ubwere mkatimo; ndipo Iye sakanati abwere umu kupatula ngati chikanakhala chotengera chokonzedweratu. Iye ankadziwa kuti iwo akanati atsature. Iye ankadziwa. . .

⁸⁴ Ine ndikukhulupirira Paulo, chifukwa chimene iye ankayenera kuti abatizidwe kachiwiri chinali, iye anali atawazunza Akhristu. Ndiko kulondola. Ndipo Iye, Mulungu ankadziwa, chifukwa Iye anati, “Ine ndamusankha iye,” Iye anatero kwa Anania, mneneri. Pamene Iye anadziwa kuti Saulo anali kumeneko mu chipinda, nkhope itadetsedwa ndi maso atadetsedwa, ndipo i—iye anali atapemphera molimba kwambiri

ndi fumbi paliponse pa iye, ndipo iye anachititsidwa khungu kuchokera ku Lawi la Moto limene linawonekera kwa iye pa njira wa kumeneko; ndipo Iye anati, “Ine ndamusankha iye chida cha kwa Amitundu.” Mulungu ankadziwa zimenezo—kuti Anania akanati akhoze kumubatiza iye mu Dzina la Yesu Khristu mu Mtsinje wa Damasiko masiku atatu patsogolo pake. Koma ine ndikukhulupirira kuti machimo ake anali atakhulukidwa kale, koma iye ankayenera kuti achite izi kuti asonyezere kwa dziko. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti icho ndi chifukwa chake ife timayenera kuti tizibatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti mbewu yokonzedweratu idzatha kuziwona zimenezo, ndipo ndi iwo okha ati adzaziwone izo.

⁸⁵ Tsopano, abale a chikhulupiriro chautatu, ine sindiri kuponyera izi kumbali kwa inu, m’bale wanga wokonedwa, ine ndikungoyankha mafunso. Ine ndikungopereka malingaliro anga owona a izo. Tepi iyi ikhoza nthawi ina kukathera mu Afrika. Ine ndikukhulupirira kuti ife tiri mu mithunzi ya kudza Kwake. Ife tonse tikukhulupirira zimenezo.

Ine ndiri nawo abwenzi ofunika, a DuPlessis ndi a Schoeman, ndi onse, Yeager, ndipo iwo abale abwino m—mu South Afrika. Koma nthawizonse pali winawake amene amangoima bwino bwino mu moyo wa munthu. Ndipo mwa anthu onse amene—ndipo ine ndimawakonda iwo mokondeka basi momwe ine ndimamukondera m’bale uyu, mofunikira basi, koma M’bale Jackson ndi mkazi wake nthawizonse ankaima bwino mu moyo wanga. Ine sindimatha basi kumvetisa zimenezo; i—iye ankaima bwino. Tsopano, kumeneko kuli Justus DuPlessis, mzanga wapachifuwa, ndipo o, ochuluka kwambiri a amenewo abwino, abale abwino Achiafrikani ndi alongo.

⁸⁶ Chabwino, chifukwa chiani M’bale Jackson ndi mkazi wake anali kundimira bwino ine? Chifukwa iye anali msaki? Ayi! Chifukwa ine ndiri nawo abwenzi ambiri abwino osaka kumeneko. Koma nchifukwa chiani iye amaima bwino? Ndipo bwanji? Ngati inu mukanati mungodziwa chinsinsi cha kuseri kwa zonse izi. Koma ine sindimawauza anthu zinsinsi zonse zimene ine ndimazidziwa. Pakuti, chifukwa chiani izo zinali kuti pa ora lomwelo limene Ambuye anati, “Uyankhulane ndi Sidney Jackson ku South Afrika,” Ambuye anayankhula kwa Sidney Jackson kuti abwere kuno? Lamlungu lapitalo iye anabatizidwa, iye ndi mkazi wake, mu Dzina la Yesu Khristu, komwe kuno mu nthawi ya mwamthunziyi. Onani, okonzedweratu ku cholingacho. Mwaona?

⁸⁷ Tsopano, ine ndikukhulupirira kuti iwe—uma—pulumutsidwa pa kumulandira Yesu Khristu. Ndipo ubatizo wa madzi ndi kuwonetsera kwa kunja koti usonyeze kuti chinachake mkatimo chachitika, chifukwa madzi alibe ukoma;

ndi choyimira chabe. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti iwe umapulumsidwa pamene iwe. . .

⁸⁸ Tsopano, pali anthu ambiri (ndiroleni ine ndiziwongole izi kwa m'baleyu). . . Pali anthu ambiri amene ali—amati iwo anapulumsidwa; ambiri amabatizidwa mu Dzina la Yesu; ambiri amayankhula mu malirime, ndipo ali ndi mitundu yonse ya zisonyezo za Mzimu Woyera, ndipo apobe asali atapulumsidwa nkomwe. Uko nkulondola. “Ambiri adzadza kwa Ine mu tsiku limenelo nati, ‘Ambuye, kodi ine sindinakhale ndikulosera mu Dzina Lanu?’—mlaliki—‘Kodi ine sindinali mu Dzina Lanu kutulutsa ziwanda ndi kuchita ntchito zambiri zamphamvu.’” Iye adzati, “Chokani kwa Ine, inu ochita mwa kusaweruzika; Ine sindinali kukudziwani nkomwe inu.” Mwaona? Kotero zinthu zonse izo, komabe i—i—izo ndi Mulungu; izo ziri mmanja Mwake. Koma pamene ine ndiwona izo. . .

⁸⁹ Inu mukuti, “Chabwino ndiye, nchifukwa chiani inu mumawaitaniranso anthu kuti adzabatizidwenso?” Ndi chifukwa chakuti ine ndikutsatira ndondomeko ya pachiyambi. Ife sitingathe kutaya ndondomeko imeneyo.

⁹⁰ Tsopano, ife timutenge mtumwi Paulo pamene iye anawapeza ophunzira ena ake amene anali anthu odabwitsa. Ine ndikukhulupirira iwo anali opulumutsidwa, ndipo komabe iwo anali asanabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu, ngakhale iwo anali atabatizidwa (Machitidwe 19). Paulo podutsa ku maiko a gombe la kumtunda kwa Aefeso; iye anawapeza ophunzira ena. Ndipo iye anati kwa iwo, “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni chanu?”

Ndipo iwo anati kwa iye, “Ife sitikudziwa za Mzimu Woyera, ngati kuli Mzimu Woyera uliwonse.”

Iye anati, “Ndiye inu munabatizidwira ku chiani?”

Iwo anati, “Ife tinabatizidwa kale. Yohane anatibatiza ife, mwamuna yemweyo amene anamubatiza Yesu.” Umenewo ndi ubatizo wabwino ndithu.

⁹¹ Mupenyeni mtumwi wolimba uyu. Iye anati, “Koma Yohane ankangobatiza kuloza ku kulapa,” osati kwa kukhululukidwa kwa machimo, chifukwa Nsembe inali isanaphedwe apo, kubatizidwira kwa iko. . . Ndipo pamene iwo anamva ichi, iwo anabatizidwanso mu Dzina la Yesu Khristu, ndipo Mzimu Woyera unabwera pa iwo.

⁹² Tsopano, kodi ichi chinachita chiani? Zinasonyeza kuti anthu awa amene anali okonzedweratu ku Moyo, mwamsanga pamene iwo anawona Choonadi cha Mwamalemba, iwo anayenda mu Choonadi ndipo analandira mphoto ya wokhulupirira: Mzimu Woyera unabwera pa iwo, ndipo iwo anayankhula mu malirime, analosera, anamukuza Mulungu. Inu mukumvetsa zimenezo tsopano? Mwaona? Iwo anachita

zimenezo iwo atakhala nacho kale chisangalalo chachikulu, kufuula, ndi kumutamanda Mulungu.

⁹³ Mu Baibulo iwo anali naye mlaliki wa Chibaptisti kumeneke; iye anabatizidwa nayenso. Koma iye anali, ndipo iye anali—ankatsimikizira n—ndi Baibulo kuti Yesu anali Khristu. Ndipo anthu anali ndi chisangalalo chachikulu, ndipo iwo anali okondwa kwambiri basi pa chimenecho; ndipo apobe iwo anali opanda Mzimu Woyera! Iwo anachita kubatizidwanso kachiwiri. Ndipo Paulo ananena mu Agalatia 1:8, “Ngati Mngelo wochokera Kumwamba angabwere nadzalalikira uthenga wina uliwonse wosiyana ndi uwu umene ine ndaulalikira kwa inu, musiyeni iye akhale wotembereredwa.” Sanali kusamala chimene icho chikanakhala chiri.

⁹⁴ Chotero, podziwa zinthu izi...Mwinamwake inu simukuzidziwa izo, abale anga; koma podziwa zinthu izi, ndiye ine ndiri wokakamizidwa ndi kumangikira pa ntchito kwa Mulungu kuti ndizichita dongosolo la maziko oyambirira, chifukwa palibe munthu wina amene angaike maziko ena aliwonse kuposa awo amene anaikidwa kale; amenewo ndiwo atumwi ndi aneneri. Aneneri ananeneratu izo, ndipo atumwi ankazichita izo; ndipo ife tikuyenera kuti tizipitirira kumazichita izo mpaka chimangochi chitsirizidwe.

⁹⁵ Tsopano, ine ndikukhulupirira ndiye, kuti munthu amapulumsidwa pamene iye akhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu ndi mtima wake wonse, ndipo kuchokera mu mtima mwake, osati kuchokera ku chikumbumtima chake chakunja tsopano... .

⁹⁶ Onani, inu—ndinu munthu wapawiri—anthu atatu mwa mmodzi, solo, thupi, ndi mzimu. Tsopano, ine ndikukhulupirira mphamvu zanu zakunja, s—solo yanu kuchokera-osati solo yanu, koma chikumbumtima chanu chakunja, mphamvu zanu... Pamene inu muli maso, mwa kuyankhula kwina, i—inu mumagwiritsidwa ntchito ndi mphamvu zisanu: kuwona, kulawa, kukhudza, kununkhiza, ndi kumva. Zimenezo zinangopatsidwa kwa inu kuti muzikhudzira kwanu kwapani pano; ndipo i—izo sizinapatsidwe kwa inu kuti muzikhudzira kwanu kwa kumwamba. Pali mochtika mphamvu zisanu ndi imodzi mu thupi laumunthu, chifukwa iye ndi wa chiwerengero cha chisanu ndi chimodzi mu Baibulo. Iye analengedwa pa tsiku lachisanu ndi chimodzi, ndipo iye ndi wa chiwerengero cha chisanu ndi chimodzi—munthu ali. Ndipo iye ali nako kuwona, kulawa, kukhudza, kununkhiza, kumvera, ndi chikhulupiriro. Chikhulupiriro chake chimakhazikitsa kumene iye akupita, kumene iye walunjikako.

⁹⁷ Tsopano, chikhulupiriro ndi thunthu la zinthu zoyembekezedwa, umboni wa zinthu zimene inu simukuziwona, kulawa, kuzikhudza, kununkhiza, kapena

kuzimva. Koma mwa chikhulupiriro, pamene iye awagwira Mawu, Iwo amamutumiza iye mu dera (mwaona?) izo zimawapangitsa Iwo kukhala enieni kwambiri kwa iye, mpaka iye amangokhala basi ngati kuti iye ali nazo izo mu dzanja lake. Iye amadziwa kuti izo zichitika.

⁹⁸ Tsopano, apo pali chinthu chomwecho pa funso ili pano pa ubatizo wa madzi. Mwaona? Mulungu ankadziwa kuti anthu awa akanati abatizidwense mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo Paulo, iye anaika neno lakuti palibe munthu, ngakhale Mngelo wochokera Kumwamba, asamaphunzitse chiphunzitso china chirichonse chosiyana ndi chimene iye anali ataphunzitsa; koteru choncho, ngati ine ndibwera ngati mlaliki; ngati mtumiki, ngati mneneri, kapena chirichonse chimene ine ndingakhale ndiri, kapena ngakhale Mngelo kutsika pansu, ndi kuphunzitsa chinachake chosiyana kwa chimene mtumwi uyu anachita, ndipo ine ndikapanda kuwalamulira anthu kuti azibatizidwanso mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikanadzapezeka mwa Baibulo mboni yabodza ya chinthu chimene ine ndikudzinenera kuti ndikuchikhulupirira.

⁹⁹ Koteru ine ndikukhulupirira kuti ndondomeko yayalidwa kale. Munthu aliyense mu Baibulo anali kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Panalibe nthawi imodzi pamene aliyense anayamba wabatizidwapo mu dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera. Mwaona? Panalibe aliyense anayamba wakonkedwapo; iwo onse ankamizidwa.

¹⁰⁰ Koteru ine ndikukhulupirira kuti pamene iwe mochitika . . . Kwa funso lanu, m'bale wofunika, ine ndikukhulupirira kuti pamene Mulungu adziwa mtima wako . . . Padzakhala zikwi uko amene anabatizidwa mu Dzina la Yesu. Iwe umangopita pansu wochimwa wowuma ndi kutulukamo uli wonyowa. Mukuona, mwaona? Koma monga wokhulupirira weniweni, wooka, amene iwe ukuyenera kuti uziyenda mu chikhulupiriro chonse ndi chikumbumtima chabwino kwa Mulungu, pamene iwe uziwona izo, iwe umabatizidwa! Koma ine ndikukhulupirira kuti izo zimangokhala kuwonetsera kwakunja kusonyezera kuti ntchito yamkati ya chisomo yachitidwa.

¹⁰¹ Chimodzimidzi basi momwe Mulungu anamangira chombo. Anati, “Nowa, kalowe mu icho, iwe ndi banja lako ndi apanyumba ako.” Ndipo iwo anakalowa mmenemo. Tsopano, ine ndikukhulupirira kuti ngati apo pakanati pasakhale chombo, Mulungu akanamulola Nowa kuti akhale pa chipika kapena kuyenda pa madzi. Mwaona? Koma Iye anapanga chombo kuti iye alowemo, ndipo iyo inali njira yochitira zimenezo; imeneyo inali njira yoperekedwa ndi Mulungu. Ine ndikukhulupirira kuti Mulungu amamupulumutsa munthu mwa chisomo. Mu Dzina la Yesu Khristu kudzera mu kuwonetsera kwa kunja ndiyo njira ya Mulungu yoperekedwa yoti ulowere mu zimenezo, pakuti iwo onse ankabatizidwa mwanjira imeneyo.

¹⁰² Ine sindiri kumuweruza munthu winayo, koma izo ndi basi...ine ndikuganiza kuti ndi chimene izo ziri. Madzi samamupulumutsa munthu, iwo amangosonyeza kuti iye wapulumutsidwa; icho ndi chofotokozera mwakunja. Tsopano, izo zikhoza kusakhala zolondola, m'bale. Ngati izo siziri, chabwino, ife tidzazitenga izo nthawi inayake kapena... Chabwino.

242. Mu Genesis 6:4, chitachitika chigumula, kodi zimphona zinachokera kuti?

¹⁰³ Limenelo ndi labwino, labwino kwambiri. Limenelo ndi funso lanzeru. Kodi zimphona izi zinachokera kuti? Adamu sanali chimphona monga momwe ife tikudziwira, chifukwa ngati izo zikanakhala, Baibulo likanakhala litanena chomwecho. Iye anali munthu wamba chabe. Kodi iwo anachokera kuti? T—tsopano, uwu ndi mtsutso wawukulu, ndipo ichi changoperekedwa kwa ine. Izo ziri pa pepala lalikulu, lakuda, ndipo izo ndi—kapena zilembo zazikulu, zakuda pa chidutswa cha pepala loyera.

¹⁰⁴ Tsopano, zimphona izi...ine ndikukhulupirira anali wina—winawake kuno osati kale...Iye ayenera kuti anali Josephus. Ine si—ine sindikunena izo tsopano, abale otumikira, kuti anali Josephus. Koma izo zikuwoneka kwa ine kuti akhoza kukhala kuti anali iyeyo, kapena Dr, Scofield, kapena ena a iwo, amene ananena kuti zimphona izi zimene zinali mu dzikolo zinali makamaka mizimu yokugwa ya Mulungu imene inamvera k—ku nthano za Satana, pamene iye anazinena ku—cha Kumwambako...Ndipo anali Mikaeli...Ankayesera kuti ayambitse nkhondo ndi Mikaeli Kumwamba...anaponyedwera pansu...Kuti ana amuna a Mulungu awa anawaona ana aakazi a anthu, ndi kuti zimphona izi zinali mu dzikolo pa nthawi imeneyo, kuti iyo inadzikunikizira yokha mu thupi laumunthu. Ngati inu muchita zimenezo, inu mumupanga Satana kukhala mlengi. Inu simungati muchite zimenezo.

¹⁰⁵ Mosachuluka kuposa Dr. Smith, ku Seventh Day Adventist pa mbuzi yansembe. Iye anati mbuzi imodzi imene inali... Iwo ankapha mbuzi ziwiri pa—tsiku la nsembe—Tsiku la Chitetezero, ndipo mbuzi imodzi inkaphedwa ndipo inayo inkamasulidwa ipite. Ndiyeno iye anati mbuzi imene inkaphedwa inkaimira Yesu, wonyamula machimo athu amene anafa; koma mbuzi imene inkamasulidwa inkaimira mdierekezi, amene amanyamula machimo athu ndipo amapita kutali ku muyaya ndi iwo. Tsopano, inu mukuona, aliyense...Kwa lingaliro langa...Ngati izi ziti zidzakafikenso konse kwa m'bale wa Adventisti, ine sindikunena kanthu pa munthu wamkulu uyo, Dr. Smith. O, iye anali munthu wophunzira, waluntha, wabwino, Mkristu wotukuka, wokhulupirira; koma kwa ine, inu mukuona, izo sizikupanga nzeru. Pamene inu muchita zimenezo, inu mukupereka nsembe kwa mdierekezi ndiye. Izo

zonse zinkaimira Khristu kufa, kuikidwa, ndi chiukitsiro. Iye aponso anafera machimo athu ndipo anawanyamulira machimo athu kotalitali; zonse izo zinali Khristu.

¹⁰⁶ Kotero zimphona sizinabwere pa kudzikanikezira yokha mmenemo. Zimphona izi zinali ana a Kaini, amene bambo wawo anali serpenti, amene ankawoneka mwa mawonekedwe aliwonse ndendende monga munthu, koma anali munthu wamkulu, kwambiri, wamkulupo kuposa munthu. Ndipo uko ndi kumene ana amenewo anachokera, chifukwa iwo anali ana a Kaini, nchifukwa iwo anali Akanani mu dziko la Kanani, kumene iwo anachokerako; ndipo uko nndi kumene Kaini anapitako. Ndipo izo zinali. . . Mukuona, izonso zikutsimikizira mbewu ya serpenti. Iwo unali mtundu wa anthu wosiyana mwapalimodzi. Zimenezo zinali mbewu za serpenti. Mwaona?

¹⁰⁷ Tsopano, f—funso la mbewu ya serpenti ilo liri mkati umu, kotero i—ife tifika kwa ilo, ndipo ine ndikufuna kuti inu mukhale nazo izi mu malingaliro. Mwaona? Tsopano, kuti ndingopereka maziko awa.

¹⁰⁸ Mukuona, iwo anali—iwo anali Akanani, zimphona izi; ndipo iwo anali ana a Kaini, amene anali mwana wa serpenti. Ndipo serpenti anali chimphona cha munthu, munthu wamkulu, wokhala ngati mwachinyama, osati chokwawa konse, wokongola. Iye anali wochenjera kwambiri mwa zinyama zonse za kuthengo. Ndipo iye anali yekhayo. . .

¹⁰⁹ Onani, m—majini ochokera kwa chinyama kupita mwa akazi sangabale konse. Iwo aziyesera izo mobwereza bwereza; ndi zosabereka kwa ukazi wa mkazi. Ndipo tsopano, iwo akulephera kuti achipeze icho. Kutenga chimpanzi, iye ndi chinthu chapafupi kwambiri chimene iwo angathe kuchipeza kwa munthu, kapena gorila, kapena zina za izo zoyandikirapo kwa munthu. Monga Mulungu mu kusintha kwake kwa chirengedwe kwakukulu anayamba kupanga nsomba; ndiyeno Iye anapanga mbalame; ndipo kenako Iye anapanga zinthu zinazo, zinyama, ndipo izo zinakhala zikubwerabe chokwera, mpaka china chinabwerapo mpaka kwa chimpanzi, ndi kwa nyani, ndi kumapitirira mpaka kwa gorila, ndiyeno mpaka ku mawonekedwe a serpenti, ndiyeno kuchokera kwa serpenti kufika kwa munthu.

¹¹⁰ Ndipo mtundu wa anthu wayesera kuti afufuze, sayansi, kuyesera kuti apeze mafupa, chimene chinyama ichi chinali chomwe chinali chapafupi kwa umunthu. Ndipo umunthu ndi chinyama. Munthu, gawo la mnofulo ndi mnofu wa chinyama; ife tikudziwa zimenezo. Ife ndife zinyama, chimene chiri chinyama cha magazi ofunda; ife tikudziwa zimenezo! Koma nchiani chimapangitsa kusiyanako? Chinyama sichimakhala nayo solo yamkati iyo, koma umunthu uli nayo. Icho sichimadziwa chabwino kusiyantsa ndi choipa.

¹¹¹ Galu wamng'ono wamkazi iye samadziwa kuti akuyenera kumavala diresi, ndipo ine sindikukhulupirira kuti iye angavale akabudula ngati iye akanati—akanamvetsa. Ngakhalenso nkhumba siikanatero, koma ndi mtundu wokugwa wa umunthu. Mwaona?

¹¹² Tsopano, u—uko ndi kumene izo zinachokera. Uko ndi kumene zimphona izi zinachokera. Iwo anali ana a serpenti.

¹¹³ Ndipo onani, pamene iye anamuwona Eva ali mu chikhalidwe ichi, i—Satana analowa mwa iye ndipo anamupangitsa iye kuti... Mukuona, Adamu anali asanazindikire izo apobe. I—ine sindikudziwa momwe ndingagwiritsire ntchito mawu awa. Izo zikhala zabwino bwino nanu inu nonse pano, koma winawake amazitsutsa kwambiri zimenezo. Inu mukudziwa, iwo nthawizonse amayesera kuti atole chinachake. Koma onani, Adamu anali asanamudziwe konse Eva, mkazi wake. Iye anali asanafike konse pa malo amenewo, ndipo Satana anamutsogolera iye pamenepo. Mwaona? Ndiyeno pamene iye anakhala ndi pakati, ndiye iye anamudziwa iye. Ife tifika kwa izo pa funso lotsatira ili kapena limodzi la mafunso awa. Ine sindikudziwa kuti liri pati; ife—ine ndinangoliwona ilo mkati umu. Tsopano, koma uko ndi kumene zimphona zinachokera.

243. Wokonedwa M'bale Branham, kodi ana onse aamuna ndi aakazi a okhulupirira owona, obadwa mwatsopano adzapulumutsidwa?

¹¹⁴ Ayi, m'bale; ayi, iwo ndithudi sadzati. Onani, monga ine—monga ine ndinamutengera David DuPlessis pa ndemanga iyi, “Mulungu alibe zidzukululu (mwaona?), ana aamuna ndi aakazi okha.” Mukuona, iwo adzayenera kuti adzabadwe chimodzimodzi basi monga abambo awo ndi amayi anabadwira nao Mzimu. Mwaona? Icho ndi chimene chimamupanga munthu kukhala munthu watsopano, ndi chifukwa chakuti iye wabadwa kachiwiri, kubadwanso. Kubadwa kwake koyamba kumamubweretsa iye munthu wachibadwa pa dziko lapansi; kubadwa kwake kwachiwiri kumamubweretsa iye munthu wauzimu wa Kumwamba. Mwaona? Izo zimamusintha iye, solo yake, osati chikumbumtima chake chakunja, mapangidwe ake akunja, mphamvu zake; iye amamverera apobe, ndi kununkhizabe, kulawa, ndi kumva; koma magawo ake amkati, zokhumba zake, zimene zimamupangitsa iye, zasinthidwira kwa Mulungu. Mwaona?

¹¹⁵ Tsopano, kumbukirani, njira yokha yomwe izi zingachitikire ingati ikhale iyi: monga momwe izo zinaliri mu nthawi ya kenturio wa Chiroma. Paulo anamuza wa Chiromayo, iye ndi Sila, pamene iye ankafuna kuti asolole lupanga lake ndi kudzipha yekha, chifukwa Mulungu anali ataigwedezera ndendeyo pansu ndi chivomezi; iye anati, “Usati udzipweteke

wekha, powona kuti ife tonse tiri muno. Dzuka!” Ndipo ankafuna kuti adziwe chimene iye akanati achite. Iye anati, “Dzuka ndi kukabatizidwa, ukutchula p—pa Dzina la Ambuye, ndipo iwe ndi a pa nyumba yako mupulumutsidwa.” Mwaona? Mwa kuyankhula kwina, “Khulupirira pa Ambuye Yesu Khristu, iwe ndi nyumba yako mupulumutsidwa.”

116 Tsopano, motani? Ngati nyumba yako ikhulupirira mwa njira yomweyo imene iwe ukukhulupirira. Mwaona? Inu pempherani ndi kumawapereka ana anu kwa Mulungu ndi kugwiritsitsabe kwa Mulungu, mukukhulupirira kuti iwo adzapulumutsidwa.

117 Ine ndangodutsa kumene mu chondichitikira ndi Rebekah wanga. Mwaona? Kungozipereka izo kwa Mulungu. Pamene iye anafika pokhala “wa mmateni,” ndipo iye anali kuyenda ndi mtsikana wina pamene ife tinapita koyamba kumeneko, amapita—kuthamangira ku nyumba ya mtsikana winawake kumakatenga maphunziro a zoyimba . . . Ndipo mtsikana uyu . . . Ine ndinadzera uko tsiku lina, ndipo apa mtsikana uyu anali atakhala pa limba akusewera roko ndi rolo. Chabwino, zimenezo zinali zokwanira basi kwa ine! Kotero ine ndinamuuza iye kuti asadzapitenso kumeneko. Mwaona? Ndiyeno iye anati, “Chabwino, awo ndi malo okha kumene ine ndikuyenera kuti ndingamapite kukaphunzira zazoyimbira.” (Inu mukudziwa momwe “a mzaka za mmateni” amachitira.)

118 Ndipo ine ndinati. . . Mwana aliyense amayenera kudutsa mu zimenezo. Mwakuchitika aliyense amadutsa mu usinkhu umenewo. Inu munatero; ine ndinatero. Ndipo ife tikuyenera kumaganiza maganizo awo.

119 Kotero ndiye, masiku angapo zitachitika zimenezo amayi ake anamutsatira iye chifukwa cha chinachake, ndipo iye anawazazira iwo. Tsopano, ameneyo si Rebekah konse. Anachokapo ndipo anamenyetsa chitseko, ndi pafupifupi kuti akanagwetsa zinthu zinali pakhoma, napita ku sukulu.

120 Tsopano, ine ndimayenera kuti, zimawoneka choncho, ndingovula lamba wanga, ndi kumamutsatira iye mu bwalo, ndi ndikumubweza iye ndi zikwapu zikumukulunga iye. Mwaona? Koma ine ndinaganiza, “Dikira miniti, ine ndinayamba kuganiza malingaliro a wausinkhu wa zaka eyitini.” Mwaona? “Tsopano,” ine ndinati, “Mayi, ine ndikudziwa izo. . .” Iye anayamba kulira, Meda. Ine ndinati, “Ine ndikudziwa kuti iwe wachita zonse zomwe iwe ukanatha kuzichita; ine ndachita zonse zimene ine ndikanatha kuchita. Tsopano, ngati izo zatipulumuka mmanja athu, ife tiyenera kuti titenge sitepe yotsatira.”

121 Monga dona wina mokoma analemba tsiku lina (ziri mu limodzi la mafunso awa pano), anati, “M’bale Branham, inu si Mesiya, kodi muli?”

Ine ndinati, “Ayi, mayi.”

Iye anati, “Ife timakukhulupirirani inu kuti ndinu m’busa wathu, koma inu nthawizonse mumatilozera ife kwa M’busa Wamkulu.”

Ine ndinati, “Uko ndiye kulondola; uko ndiye kulondola.” Mwaona?

122 Ine ndinati, “Chabwino penya, Wokonedwa, tsopano, iwe ukuyenera kuti umvetsere kwa ine. Ndi zovuta kuti iwe ungachite izi; ine ndine mwamuna wako. Koma anthu amayenda kudutsa mafuko ndi kozungulira kuti adzangopeza mawu ochepa a malangizo. Tsopano, ngati iwe. . . Ine ndinayankhula kwa iye tsiku lina, ndipo iye anangochokapo kwa ine.”

123 Tsopano, Becky sanachitepo konse zimenezo kwa ine. Mwaona? Ndipo pamene amayi ake ananena chinachake pa izo, iye anamenyetsa chitseko ndi kuti, “Inu mukuyembekeza kuti ine ndizingokhala pano ndi kungokhala maluwa a pakhoma moyo wanga wonse?” Ndi kupsyonya! Iye anamenyetsa chitseko ndipo anapita kunjja. Ameneyo anali mdierekezi.

124 Ine ndikukumbukira, zaka ziwiri zoyambirira za moyo wake iye ankalira. Ife tikapita ku malo odyera ndi kumadya; ine ndimamuyendetsa iye mu msewu pamene Meda akudya, ndiyeno iye amayenda naye iye mu msewu pamene ine ndimadya. Ankangolira lira. Ndipo tsiku lina tiri uko ku Canada, analira usiku wonse, ndipo ine sindinathe kupuma ndi chirichonse; ine nditaima pamenepo. . . Tsopano. Ndipo Chinachake chinanena kwa ine, “Ndi mdierekezi akulowa mu utumiki wako.”

125 Ine ndinati, “Ndipatse ine mwana ameneyo.” Ine ndinati, “Satana, mu Dzina la Yesu Khristu, iwe chotsa manja ako pa iye.” Iye anatonthola apo pomwe ndipo sanalire konse moonjezera. Iye ndi mwana wa bata kwambiri amene ine ndiri naye. Kuchokera pa ora ilo lomwe izo zinachoka. Iwe umayenera kuti uchipeze icho. . . Iwe umayenera kuti ukhale uli nacho chimenecho mwa iwe basibe, iwe usanachichite icho!

Ndiyeno pamene iye—ndiyeno izo—iye anayamba zimenezo. Ndipo ine ndinamutenga Meda pafupi ora. Ine ndinati, “Meda, chotsapo manja ako.”

“Ine? Ameneyo ndi mwana wanga!”

126 Ine ndinati, “Kodi iye si wanganso?” Chabwino. Ine ndinati, “Ngati iye akanakhala akufa mmawa uno, iwe ukanati umupereke iye kwa Mulungu pofuna kopita kwake kwamuyaya. Bwanji ife sitikumupereka iye kwa Mulungu tsopano pofuna za ulendo wake wa pansipa?”

Ndipo iye anati, “Chabwino, ameneyo ndi mwana wanga!”

Ine ndinati, “Ameneyo ndi wanga inenso.”

Ine ndinati, “Tsopano, kodi iwe ungatege ako. . .”

“Ine osanena kanthu kwa iye?”

¹²⁷ Ine ndinati, “Ine sindinanene konse zimenezo. Ife tisiye kumuzazira iye, tizingomulangiza iye. Iye akusowa mzake, ndipo iwe ndi amene ukuyenera kukhala uli mzake, iwe ndi ine. Ife ndi makolo ake.”

¹²⁸ Ana awa lero akusowa mzawo. Ngati iwo akanakhala nawo amayi ndi abambo amene akanamakhala panyumba ndi kumawasamalira iwo, mmalo mopita kunja uku mu chipinda chogulitsira mowa kuthamangathamanga usiku wonse ndi zinthu monga izo, sitikanati—sitikanati tikhale ndi kupanda makhalidwe kwa ana. Mwaona?

¹²⁹ Iwo achoka ku Baibulo; iwo onse amapita ku tchalitchi ndi kumakapanga masewero a banko ndi zinthu monga izo ndi. . . Mwaona? Inu mukuyesera kuzipukuta izo momwe Satana wakhazikitsira uko mu Hollywood. Inu simungati konse muibweretse Hollywood mu mpingo, inu muyenera k—ine ndikutantha za kuwubweretsa mpingo mu Hollywood, inu mukuyenera kumubweretsa Hollywood ku mabwalo anu. Mwaona? Osati kupita mu mabwalo awo, asiye iwo azibwera kunoko. Ife tiri nacho chinachake chimene iwo sakudziwa kanthu za icho.

¹³⁰ Kotero ife pamenepo ife tinagwada pa mawondo athu ndipo tinazipereka izo kwa Mulungu. Ine ndinati, “Ine ndikudziwa iye ali usinkhu wa zaka eyitini—akhala mu masiku pang’ono, ndipo iye—ndipo msungwana wa usinkhu umenewo amaganiza za amzake achimuna, ndipo ife timamusunga iye mkati.” Ine ndinati, “I—ine sindimafuna konse kuti ndidzamuwone iye akukwatiwa. Ine ndikufuna kuti ndimuike iye mu ofesi kuno, azichita ntchitoyo. Ine ndikufuna ndidzamuwone iye atadzazidwa ndi Mzimu n—n—ndi kumakhala moyo monga choncho.”

Ndipo i. . . Chabwino, ife tonse tinkafuna zimenezo. Iye anati, “Chabwino, ife sitingathe kuzichita izo.” Anati, “Iye basi samvera kwa zimenezo.”

¹³¹ Ine ndinati, “Dikira miniti! Ife tamulera iye monse momwe ife tingathere, tsopano timuike iye mmanja a Mulungu—timupereke iye.” Ndipo ine ndinati, “Ndiye iye akamachita chirichonse tiziti, ‘Becky, wokonedwa, amayi, sakufuna kuti iwe uzichita zimenezo, koma ine ndi bambo wako; ine ndikhalabe pafupi nawe.’ Mwaona? Kumulola Iye adziwe kuti iwe ukumukonda iye. Iye ayenera kupeza wina woti azimukonda iye, ndipo uyo akhoza kukhala mkazi wolakwika.” Mwaona? Ine ndinati, “Iwe ukhale mkaziyo amene azichita kukondako.” Ine ndinati, “Wokonedwa, zimenezo zikumveka ngati zopanda pake, koma anthu amabwera kulikonse, ndipo amakhala pa zokambirana za payekha, ndi zinthu.” Ine ndinati, “Ndine wawamba kwambiri; ndife awamba wina kwa mzake,

chifukwa ndife mwamuna ndi mkazake, koma tisamalole izo kuti zizichitika. Iwe uyenera kuti uzikumbukira, izi ziri mu Dzina la Ambuye!”

Kotero iye anati, “Chabwino.”

Ife tinagwada pa maondo athu ndipo tinamupereka iye kwa Mulungu. Tinati ife tikuchotsa manja athu pa icho.

Madzulo amenewo iye anabwera umo; iye anati, “Chabwino, ine ndikulingalira inu panobe mukuti ine ndisamapite kumeneko!”

¹³² Meda anati, “Ayi, ine sindinanene kanthu za izo.” Anati, “Iwe ukudziwa, Amayi sakufuna kuti iwe uzichita zimenezo; ndipo iwe ukudziwa kuti zinakhala ngati ziwaphe abambo ako pamene iwo anakumva iwe ukusewera nyimbo za bugi wugi zija, chirichonse chimene izo zinali, ndi msungwana ujayu.” Anati, “Tsopano, iwo sakufuna kuti iwe uzichita zimenezo, ndipo ife sitikufuna kuti iwe uzichita zimenezo, Becky, koma ife tinangozipereka izo kwa Ambuye. Ine ndikufuna iwe udziwe kuti ife tikukukonda iwe. Chirichonse chimene iwe uti uchite, ife tikukukondabe iwe.”

Iye anafuula, nati, “Ine ndikupitabe mulimonse!”

Anati, “Chabwino, Wokonedwa.” Kotero anapitirira nazo. Anati, “Chabwino, ine ndikonzeratu chakudya pamene iwe uzibwerera.” Iye sanapite konse! Ayi, iye sanapitenso kuyambira pamenepo. Mwaona?

¹³³ Si motalika zitachitika zimenezo iye anakomana ndi George; George ndi Mkhristu. I—izo zinakhazikitsa icho ndiye.

¹³⁴ Iye anali kuyesera kuwauza Akazi a Wood za izo tsiku lina. Iye anati, “O, ine ndinafika polusa moyipa.” Anati, “Adadi ndi Amayi anandipereka ine kwa Ambuye.” Anati, “Ndinalusa moyipa.” Koma i—izo zinali kulusa kwa ife; ife sitikufuna kukhala ndi kulusa kulikonse koposa kumeneko. Mwaona? Kungozisiya izo kuti zipite monga choncho. Chabwino.

244. M'bale Branham, kodi inu mukuganiza chiani za athu . . .
(O, o! Ine ndikukumbukira ndinaliwerenga ili. Ine sindinali . . . Ine ndinati ndilisunge ilo mmbuyo mochedwa, koma ine ndikuganiza ine ndikhoza kungoliwerenga ilo. Zolemba za mkazi wina. Iye ayenera kukhala wochokera ku Kentucky, chifukwa ali ndi—tikiti ya Kosmos Portland Cement apa.) M'bale Branham, kodi inu mukuganiza chiani za alongo athu mu mpingo akuvala madiresi aafupi choterowa? Kodi izo sizikuipitsa umboni wathu ndi kuika chitsanzo cholakwika kwa anthu athu aang'ono mu mpingo wathu uno? Izo zikuwoneka mwakuti-. . . kumuwona wamng'ono—kumuwona mkazi wachikulire atavala diresi lalifupi kwambiri mpaka ilo limawonetsa mawondo ake pamene iye akuyenda.

¹³⁵ Aliyense yemwe inu muli, Mulongo kapena M'bale, aliyense amene muli, ine ndikugwirizana nanu zana pa zana. Ndi chamanyazi, koma ndiuzeni ine choti ndichite nazo izo! Ine ndalalikira izo molimba basi momwe ine ndikudziwira kulalikira kwake kwa izo; iwo akumachita izo chomwechobe. Kotero ndi chiweruzo chawo, chifukwa Mawu apitapo. Inde, ine ndithudi ndimatsutsana nato timadiresi tating'ono togwira thupi timene timawoneka ngati... Ine mowirikiza ndimawakalipira ana anga, Becky ndi Sarah. Ine sindikusamala momwe iwo aliri aang'ono, i...izo...ine ndimangowakalipira iwo nthawi zonse. Ine ndikuganiza iwo amavala ngakhale madiresi aja... Meda amamutengera Becky pambali tsiku lililonse pa izo. Mwaona? Madiresi olekezera kupitirira... Ndithudi ana, inu mukhoza kuyembekezera zimenezo mwa ana, ndipo inu mumayenera kuti muziwakonza iwo; koma zikafika kwa mzimayi, pali chinachake cholakwika pamenepo. Mwaona?

¹³⁶ Ndisati ndipweteke kumverera tsopano, ine ndikungoyankha mafunso. Inu mwandifunsa ine kuchokera mu mtima mwanu; ine ndikukuzani inu kuchokera mu mtima wanga. Ngati inu mwapeza kukonza kwake, c—chonde bwerani mudzandiuze ine, ine ndithudi ndichita zimenezo, ngati ine ndingathe kuchita chirichonse pa izo.

¹³⁷ Monga winawake ananena tsiku lina, iye anati, “Chabwino, ine ndikuuzeni inu, M'bale Branham,” anati, “Ine ndikuuzani inu zimene Adamu ndi Eva...” Anati, “Izo zinali ndendende basi; iwo anali ndi apulo!” Ndipo ine ndazindikira kuti iwo asintha zimenezo tsopano; iwo akuti iwo anali ndi chiani? Ine ndikukhulupirira icho chinali kutchedwa *chinachake*? [Mwamuna mwa osonkhana ayankha, “Apurikoti”—Mkonzi.] Apurikoti, eya, inali apurikoti imene iwo anadya. Chabwino, ndi nthawi yoti tigawenso maapurikoti ngati iwo angawapangitse iwo kumazindikira kuti iwo ali maliseche. Mwaona?

245. M'bale Branham, ine ndawulandira Uthenga wa Mulungu wa lero, ndiponso mwana wathu wamwamuna. Ndipo ife tonse tinabatizidwa mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Mwamuna wanga—mwamuna wanga sanaulandire Uthengawu ndipo akumenyana nawo Uthenga uwu. Ndipo iye wamukopa mwana wathu wamwamuna ndipo akumamutengera iye ku mpingo wa Methodisti. Iye akufuna kuti ine ndizipita naye ku mpingowo pamene ife sitiri mu utumiki kuno ku kachisi. Kodi izo zingakhale zoyenera kuti ine ndizipita naye iye kapena kodi izo zingakhale bwinoko kuti ndizikhala kunja kwa chipembedzo chimenecho?

¹³⁸ Chabwino tsopano, Mlango wokondedwa... Iye sanalembepo dzina ayi, koma mwinamwake inu mukumvetsera kwa funso lanu; ngati inu simukumvetsera, inu mudzalimva ilo pa tepi. Zipitani ndi mwamuna wanu, koma musati

mukhale ochita nawo a—a zimene iwo akuchita. Mukuona, inu mukuyenera kuti muziwakonda amuna anuwo, ndipo chikondi ndi chimene chimachititsa izo. Inu mungokhala muli wamchere kwenikweni; iye ayamba ludzu ngati muli chirichonse mwa iye.

¹³⁹ Musati mujowine chipembedzo chakecho. Iye anati, “Inu mukhale kutali ndi chipembedzo chimenecho.” Musati muchijowine icho; zipitani kumeneko. Ngati inu simungapeze mkate wamphumphu, zipezani watheka; mukapanda kupeza watheka, ingopezani kachidutswa. Mukuona, mwaona? Koma umo ndi momwe inu muti muwapindulire amuna anu, pakuchita zimenezo. Musati mukhale amwano, ndiye iye adziwa kuti iye ali nazonso zochuluka momwe inu muliri nazo. Mwaona? Koma pamene inu muzisonyeza chinachake chimene inu muli nacho chimene iye alibe, zimenezo zimupangitsa iye kukhala waludzu kuti akhale monga inu. Mkazi woyeretsedwa amamuyeretsa mwamuna wake.

¹⁴⁰ Limenelo linali langizo chabe. Kotero i—ine ndingati nditaye nthawi yaitali pa zimenezo, koma ife tikungofuna kuti tidutse mu ochuluka momwe ife tingathere, chifukwa ine ndikuwona kuti ine ndangotsala ndi pafupi maminiti twente-thuu ndiye. Chabwino.

246. M’bale Branham, ine ndikukhulupirira Uthenga umene inu mukuphunzitsawu ndi mtima wanga wonse. Iwo umakondoweza moyo wanga; komabe, mkazi wanga ndi mwana wanga wamwamuna samasangalala mu Mawu. Iwo sali kukhumba kuti adzilekanitse okha ku zina za zizolowezi zawo zachidziko. Inu munanena kuti ife tizidzitengera athu—tizidzitengera mabanja athu. Ine ndikupeza izo zikundivuta kuti ndizichite, zikuwoneka kuti iwo sakukhalira moyo Mawu kapena mu Mawu. Kodi njira yanga ndi iti, bwana? Kodi ine ndidzitengere iwo ndi kumakhulupirira, kapena kodi ine ndizipemphera, “Atate, chifuniro Chanu chizichitidwa,” ndi kumakhutitsidwa mu chikhalidwe chimene ine ndadzipeza ndekha ndirimomu? Ine ndikanayamikira kundilondolera kwanu, M’bale Branham.

¹⁴¹ Mulungu akudalitseni inu, M’bale wanga kapena Mlongo, aliyense yemwe inu mungakhale muli. I—ine ndikanangowapereka iwo kwa Ambuye. I . . . Mukuona, chifukwa, “Onse amene Atate anandipatsa Ine adzadza kwa Ine.” Mwaona? Tsopano, chinthu chokha choti inu anthu muzichita . . .

¹⁴² Izo zinapangitsa mtima wanga kufufuma ndi chisangalalo tsiku lina ndikupita kutunda ndi kumusi ndikuwawona amuna a mamotelo awo. I . . . ine ndinapita uko kwa Bambo Becker. Iye anati, “Billy, iwe ukudziwa chiani? Ine ndimadyetsa osonkhana anu onse Lamlungu lililonse”—pamene Blue Boar imadyetsa

mazana atatu pafupifupi Lamlungu lirilonse! Mwaona? Ndipo ine ndinatuluka panja ndipo mnyamata uyu kumeneko, njonda iyi kumeneku—ku Ranch House, munthu wabwino kwambiri. Ine ndinakomana naye; iye anati . . .

Ine ndinati, “Chabwino, izo zinali zabwino kwenikweni.” Ine ndinati, “Ine ndikuyamikira inu pochotsa zinthu zonse zija kunja kuja—kuchita mopitiriza konse kunja kuja.”

Iye anati, “Inde, bwana, M’bale Branham.”

Ine ndinati, “Iye wandidziwa bwanji ine?” Mwaona? Ine ndinati, “Inu mwandidziwa bwanji ine?”

Iye anati, “Ine ndikukudziwani inu,” Anati, “Ine ndimadyetsa osonkhana anu onse Lamlungu lirilonse pa . . . Chabwino,” iye anati, “ndipo ine ndikufuna kuti ndikuuzeni inu chinachake: iwo ndi anthu abwino. Iwo ndi anthu abwino!”

¹⁴³ Tsopano onani, izo zinandipanga ine kumverera bwino. Inu ndi ana anga. Mwaona? Pamene ine ndimva kuti ana anga akuchita bwino ndi kukhala abwino, izo zimawapanga Ababa kumverera bwino kwenikweni. Mwaona? Kotero inu mukumvetsa.

¹⁴⁴ Tsopano, tsopano, Amayi, pamene . . . Mlongo Wangwa, ngati amuna anu akufuna kuti inu muzipita ku mpingo wa Methodisti, inu zipitani nawo. Inu mwina simukapezako mtanda wonse wa mkate, koma ngati iwo ngakhale atati iwo amakhulupirira kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu, inu mukakhulupirire zimenezo, chifukwa ife timatero nafenso. Tsopano, ngati iwo apambukira pa zolunditsa zina ndi zinthu, basi—zingowasiyani iwo kuti azipitirira nazo, koma inu muzidya mkate wochulukira choterowo. Mwaona? Ndipo mmenemo, inu muzingosonyeza mwa kukoma kwa moyo wanu ndi kulingalira bwino kwanu pa ena . . . Ndipo ngati inu mulibe izo, wokonedwa Mlongo, pempherani mpaka izo zibwere kwa inu, kuti inu musamachite kudzipangitsa chirichonse chongopeka, chifukwa pamene inu muchita zimenezo, izo si zenizeni. Mwamuna wanu akhoza kudziwa zimenezo. Koma inu—pamene inu mwapemphera zenizeni mpaka pa malo pamene moyo wanu uli wodzaza ndi mchere wa Mpulumutsi, izo zipanga kukhudzako. “Ngati ine nditi ndikwezedwe mmwamba, ine ndikokera anthu onse kwa Ine.” Ine ndikanamapita; zikhalani osamala kwenikweni. Musati mukajowine mpingowo apobe! Chonde musati mukachite zimenezo; inu musati mukajowine mpingo wawo, koma zipitani nawo!

247. M’bale Branham, apa pali funso limene lakhala ngati lododometsa kwa angapo a ife pano. Mmodzi—p—pa (pepani ine)—pa matepi ena inu mumayankhula za Ayuda okha kukhala akupulumutsidwa Mkwatibwi atakwatulidwa kaye. (Ndipo padutsa mzere.) Chonde fotokozani kwathunthu za Amitundu amene sati apite

mu mkwatulo. Ine ndimaganiza inu munanena kuti Amitundu amene anasiyidwa anadutsa mu chisautso ndipo anapereka miyoyo yawo mwa umboni wa Yesu. Pamene Iye akubwerera kuchokera kwa Amitundu kupita kwa Ayuda—pamene Iye akupotoloka nachoka kwa Amitundu kupita kwa Ayuda, ndiye apo palibe mwayi wina uliwonse kuti Amitundu apulumutsidwe, Amitundu okha amene anapulumutsidwa kale, koma amene sanalandire Choonadi cha tsiku lawo lotsiriza adzapita mu nthawi ya chisautso ndiyeno nkudzapulumutsidwa pa mapeto. Kodi uku nkulondola? Chonde longosolani, chifukwa inu munanena kuti uko kudzangokhala chiwerengero chaching'ono chokha chopita mu mkwatulo. Nanga bwanji anthu amene anakhulupirira pa Ambuye—akukhulupirira pa Ambuye tsopano ndi momwe—ndipo sakukhulupirira momwe inu mumalikirira Athenga wa tsiku la nthawi yotsiriza uwu? Kodi iwo adzapulumutsidwa? Ndiyeno mlongoyo walembe dzina lake.

145 Tsopano, funso labwino kwambiri. Tsopano, malo oyamba, kusokoneza kwake kuli, kuli zimene ine ndanenapo za masiku a Amitundu kuti adzatha pamene chisautso—mu chisautso. Tsopano, ine sindimawawona Amitundu mu Baibulo... Mkwatibwi wa Amitundu, Mkwatibwi, osati mpingo wa Amitundu tsopano, mpingo wa Amitundu udzadutsa mu nthawi ya chisautso (mwaona?), koma osati kwa... Mukuona, Mkwatibwi ndi Wosankhidwa; Iwo sali kudutsa mu chirichonse koma mkwatulo. Iwo adzangosinthidwa ndi kuchotsedwa mu dziko. Mwaona? Tsopano, ine ndifotokoza zimenezo mu funso lamtsogolo pano, ndizibweretsa izo kuchokera kwa Lutera mmwamba, ndipo inu muwona ndiye chimene izo zikutanthauza; uko ndi kukhwima kwa Thupilo. Mwaona?

146 Tsopano zindikirani. Tsopano, Ayuda amene akutsala ndi amene ati adzalalikidwire ndi aneneri awiri, Eliya ndi Mose.

147 Tsopano, awa ndi malingaliro anga anga, abale otumikira, njira yanga yanga yomwe ine ndikumverera kuti Mzimu Woyera waziwululira kwa ine.

148 Tsopano, chinthu chotsatira choti chichitike ndi Achiyuda—kapena Mkwatibwi wosankhidwa wa Amitundu kuti akwatulidwe palimodzi ndi Mkwatibwi wina yense wosankhidwa wa Amitundu amene wakhala ali mmusimo kudutsa mmibadwo—adzakwatulidwira mmwamba mu Kukhalapo kwa Khristu mmiyamba. Akufa akuuka; amene ali amoyo ndipo atatsalira akusinthidwa; ndipo iwo akukwatulidwira mmwamba palimodzi mu mlengalenga kukakomana nawo Ambuye. Ndiye, chifukwa...

149 Pambuyo pa mwambo wa Chikwati mu Ulemerero, Yesu—iwo akadzati akwatulidwira mmwamba kupita mu mlengalenga,

Yesu akubwerera pa dziko lapansi ndi kudzadzidziwitsa Yekha kwa anthu Ake, mwa choimira monga Yosefe anadzidziwitsa yekha kwa abale ake. Ndipo mkazi wake, palibe Wamitundu amene analipo, palibe wina aliyense koma Yosefe yekha, pamene iye anakadzidziwitsa yekha kwa abale ake. Nonse mukumvetsa zimenezo tsopano?

¹⁵⁰ Iye anatomiza...Ngakhale mkazi wake anali ali mu nyumba yachifumu, choimira kuti Mkwatibwi adzakakhala ali mu nyumba yachifumu mu Ulemerero pa nthawi imeneyo. Ndiye Yesu akudzidziwitsa Yekha kwa Ayuda (mwaona?) ukadzachitika mwambo wa Chikwati, zaka 3½, n—n—ndi vuto la Yakobo, zaka 3½ zija, kutha kwa sabata lachisevente la Daniele. Mesiya ndi woti adulidwe mkati mwa...Ndipo Iye ananenera zaka 3½ ndipo anadulidwa nachotsedwapo. Ndiye pali zaka 3½ zatsalirabe kwa aneneri awo, Mose ndi Eliya, ndiyeno pa kutha pa masiku sevente awo monga zinawerengedwera pa anthuwo, momwe Daniele ananenera; ndiye pa kutha kwa masiku sevente amenewo, Yesu ali woti akadziwitsa Yekha kwa iwo. Iye ndiye Kalonga uyo amene akuyenera kuti abwere kwa Ayuda. Mwaona?

¹⁵¹ Tsopano, ndiyeno pa nthawi imeneyo...Onani, Mkwatibwi wa Amitundu ali Kumwamba, ndipo anamwali opusa, namwali wa Amitundu, si woti adzapulumutsidwe pa nthawi imeneyo; iye ali wopulumutsidwa kale, koma wakanidwa mwa Mkwatibwi. Ndipo iye akungodutsa mu nthawi ya chisautso kwa nthawi ya chiyeretso, chifukwa iye wamukana Khristu, Mawu, oti iye ayeretse nayo. Ndiye iye ayenera kumva kuwawa chifukwa cha zochita zake, koma Mkwatibwi amene wasandulika Mawu, chitetezero chathunthu chinapangidwa ndi Khristu, chifukwa Iye ali Mawu. Thupi limenelo linang'ambidwa, ndipo pamene thupi limenelo linang'ambidwa, Mkwatibwi anali mu thupi limenelo, chifukwa ilo Lonse liri Mawu! Ameni! Inu mukuziwona zimenezo?

¹⁵² Pamene Yesu anamva kuwawa mu thupi limenelo, Iye anamva kuwawa...Chifukwa mwamuna ndi mkazi ali munthu mmodzi. Eva anatengedwa kuchokera kwa Adamu, Mpingo... Nchiani chinachitika? Mulungu anatsegula mbali y—ya Adamu ndipo anatenga kuchokera mmenemo womuthandizira, mkwatibwi. Ndipo Mulungu anatsegula mbali ya Yesu pa Kalvare ndipo anamutulutsamo Mkwatibwi. Mwaona? Ndipo pamene Yesu ankafa pa Kalvare...Kumbukirani, Mkwatibwi sanatengedwe kuchokera mu thupi mpakana thupilo litafa. Iye anali atafa kale, ndipo iwo ankati athyole miyendo Yake. Ndipo mneneri anati, “Sipadzakhala fupa limodzi liti lidzaswedwe.” Koteriwo anali atakokela mmbuyo kale nyundo kuti athyole miyendoyo, ndipo mwamuna anapita apo ndi nthungo ndipo anaithimbiriza iyo kupyozza mtima Wake; ndipo madzi ndi magazi zinatulukamo; Iye anali atafa kale. Mkwatibwi anali

atawomboledwa kale mu thupi mwa imfa Yakeyo, kotero palibenso kuvutika mu nthawi ya chisautso kwa Mkwatibwi. Mwaona? Iye akupita kukalowa. Koma mpingo wa Amitundu umene unangokhulupirira pa Iye ndi kumatenga tizikhulupiriro tachipembedzo ndi zina zotero ndipo apobe . . .

¹⁵³ Monga munthu wosauka uyu anati: “Mwamuna wanga ndi mwana wamwamuna, iwo akukondabe zinthu za mdziko ndi zinthu monga choncho” . . . Mukuona, iwo sanakuvomereze kuwombola kumeneko, pakuti pamene iwe utero, izo zimakutsuka iwe mwazokha. “Iye amene wabadwa mwa Mulungu samachita tchimo.” Sipamakhalanso chikhumbo, mulibe kanthu mwa iye ka zinthu za mdziko.

¹⁵⁴ Yesu anati, “Iye amene akonda dziko (*Kosmos* tsopano), kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri nkome mwa iye.” Iye sali mu chikondi ndi Mkwati. Mwaona? Choncho, iye ayenera kuti adzalipire chilango chimenecho, ndipo osati . . . Iye sali kudzapulumutsidwa mu nthawi imeneyo; iye ali kupulumutsidwa tsopano kuchokera ku imfa yamuyaya; koma iye adzayenera kuti adzadutse mu nthawi ya chisautso kuti adzayeretsedwe. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Tsopano, tsopano, izo—ine ndikukhulupirira izo zikukhazikitsa funso limenelo. Tiyeni tiwone, pali chinachakenso apa.

¹⁵⁵ “Chonde tafotokozani, chifukwa inu munanena kuti padzakhala pali chiwerengero chapang’ono chokha chidzapite mu mkwatulo.” Amene ali awa pa dziko lapansi amene ati adzasinthidwe. Yesu anati, “Khwalala ndiro chipata ndipo njirayo ndi yopapatiza, koma apang’ono adzakhalapo amene ati adzaipeze iyo.”

¹⁵⁶ “Nanga bwanji anthu amene akukhulupirira mwa Ambuye tsopano ndipo sali—ndipo osati momwe inu mukulalikirira?” Iwo sakuwona kuti akhulupirire izi. Iwo sakuwona kuti achite kukhulupirira momwe ine ndimalalikirira izo. Mwaona? Sakuwona kuti achite kukhulupirira izo. “. . . kwa Uthenga wa tsiku lotsiriza. Kodi iwo adzapulumutsidwa?” Inde, ngati iwo akhulupirira Ambuye. Mwaona? Ndipo ngati iwo—ngati iwo azitsutsa ndi kumati, “Ine sindikukhulupirira kuti Iye ali Mawu. Ine sindikukhulupirira kuti izi ndi zolondola. Ine sindikukhulupirira mu ubatizo wa Mzimu Woyera,” izo zikusonyeza kumene iwo ali nkupita, nthawi ya chisautso. Koma iwo amene angawalandire Mawu mu chidzalo Chake, osati ine ndikuwalalikira Iwo, chifukwa Liri Baibulo likunena choncholo. Awo amene akuvomereza izo ali mfulu, chifukwa iwo—Mawu anaweruzidwa kale.

¹⁵⁷ Tsopano, kodi Woweruza wolungama angamuweruze munthu kawiri pa chinthu chirichonse ngati chilangocho chinalipiridwa? Ngati ine ndikanakhala ndiri mu sitolo ya pinyolo, ndipo inu nkubwera uko ndipo mukanati, “Ine

ndikuti ndimuwombole iye”; ndipo inu mukanalowa umo ndipo mukanalipira mtengo wa kuwomboledwa kwanga (ndipo icho ndi chilango changa cha kukhala ndiri mu sitolo ya pinyoloyo), ndipo inu munalipira chiwombolo changa, ndiye wopinyolitsayo anganditengenso ine kachiwiri chotani? Kupatula ine nditagulitsidwanso kachiwiri. Ndi inu pamene. Pamene ine ndinakana Chidzalo cha Mawu, ndiye ine ndinabwereranso mu sitolo ya pinyolo kachiwiri. Mukuona, mwaona? Ndiye ndimenyeretu njira yanga yotulukira mmenemo ndiye, ngati ine ndingathe. Koma Iye anandiwombola ine. Chabwino. Ine ndikuyembekeza kuti izo...ine—ndangokhala nazo zochuluka kwambiri pano ine ndikufuna kuti ndizitenge izi zimene... [Kutha kwa mbali yoyamba ya tepi. Mbali yachiwiri ikuyamba ndi gawo la funso likusowapo zina—Mkonzi.]

248. ...Chikoka Chachitatu ichi ndipo chiri kuyankhula Mawu. Izo zikuwoneka kwathunthu zotheka kwa iwe kuti uyankhule mawu ndipo wina akhoza kubwezeretsedwa kwathunthu ndi modzaza, nkuikidwa mwamphumphu mokonzekera mkwatulo mu chiukitsiro, Mwana wa munthu. Izi ziri chomwecho, kapena kodi izo siziri choncho? Ndipo iwe ungachite izi ngati iwe utapsyinjika bwino bwino, kodi iwe “Sungathawe ayi zinthu zonsezi (pali kubwereza pamene) — kuthawa zinthu zonse izi ndi kukaima pamaso pa Mwana wa munthu”? (Luka 21:36)

¹⁵⁸ Tsopano, m—mzanga wokondedwa. Mwaona? Tsopano, ine ndikuganiza apa kuti i—i—inu muli—inu muli ndi maneno abwino. Inde, bwana! Inde, bwana! Tsopano, izo zingakhale chomwecho. Inu munati, “M’bale Branham...” Mwakuyankhula kwina, ndi ichi chimene ine ndiri...Ine sindikuganiza izo ziri...ine ndingati...ine ndikukhulupirira i...Sikuti ndikupukuta zimene inu munanena, koma ine ndikukhulupirira ine nditha kuzipangitsa izo kuti zimvekepo bwino pang’ono kwa anthu. Mwaona? Inu mukukhulupirira, chifukwa cha Mawu Oyankhulidwa ndi zinthu zonga izo zimene Iye anazikamba. Ndipo nonse inu pano munachitirapo umboni agologolo ndi zinthu zina zonse izi zimene zachitidwa. Koma kodi inu munazindikira, kuti zimenezo zinaperekedwa mwa Kuchitakwayekha! Ine sindinamupemphe konse Iye, “Ambuye, ndiroleni ine kuti ndichite izi, ndiyankhule zinthu izi monga choncho, ndichite zinthu izi pamene.” Ine sindinamupemphe konse Iye zimenezo. Iye mwa chifuniro Chake cha Umulungu anabwera kwa ine ndipo anati, “Iwe pita ukachite *izi*.” Mwaona? Ine sindinali kupempha chinthu chimodzi cha izo. Mose sanapemphe konse kuti apite mu Igupto kuja, koma anali Mulungu amene anamutumiza iye ku Igupto kuja. Mwaona?

¹⁵⁹ Tsopano, ine ndikukhulupirira kuti Mzimu Woyera ungangwere kwa ine ndi kunena mu masomphenya, “Pita ukamuuze munthu *wakuti*, *wakuti* kuti iwo sali—iwo akuyesera

kuti agonjetse chinthu *chinachake*, ndipo iwo sangathe kuchita icho. (Ndipo iwo akusuta; iwo akumwa; iwo akunama, akuba, kapena akuchita chigololo, chirichonse chimene chingakhale chiri; kapena iwo ali ndi mzimu wachisiliro.) Ndipo iwe ungowopita kulikonse kumene iwo ali ndi kukati, ‘Iwe mzimu, tuluka mmenemo; ine ndikumumasula wamumsinga uyu paufulu.’” Kodi izo zingachitike? Mwamtheradi! Inde, ndithudi, izo mwamtheradi zingatero; izo zingachitike. Koma tsopano, pa kupenekera kwanga kwanga... Tsopano, *kupenekera* ndipo—kumatanthauza “kuchitapo wopanda ulamuliro.” Mwaona? Ine ndingapite kumeneko kuti ndikamuthandize munthu ameneyu; ine ndikungopenekera kuti izo zikhala ziri bwino bwino. Mwaona? Ndiye ine sindikudziwa; ine ndikhoza kutchulira Dzina la Ambuye pa iwo; ine ndikhoza kuwapempherera iwo, kuchita chirichonse chimene ine ndikukhumba kuchichita.

¹⁶⁰ Ngati ine ndikanakhala nayo njira yanga yanga mmawa uno...i—ine ndinangokhala ndi kuyankhulana ndi dona wamng’ono uyu amene wakhala mu chikuku ichi. Kuti abwere ku msonkhano uno lero, iwo anachita kubweretsa ozimitsa moto kuti akamuchotse iye mu nyumba yake ku Chicago; ndipo anthu amakhala patsidya la msewuwu ndipo samabwera ku misonkhano. Mwaona?

¹⁶¹ Kodi ine ndikanachita chiani? Ngati izo zikanakhala mu mphamvu yanga...Izo ziri mu...Ine ndiri nawo ulamuliro woti ndichitire izo, koma ine ndimayenera kuti ndizidikirira kulamuliridwa kuti ndichite zimenezo. Mwaona? Ine ndiri nawo ulamuliro wochokera kwa Mulungu kuti ndizichita izo; koma tsopano, pamene Iye ati apereke kulamulirako, iye akhoza kubwerera kwawo ali bwino. Mwaona? Ine ndikudziwa kuti izo ndi zoono. Mwaona? Ine ndikanangokhala wololera kuti ndife mmawa uno pa izo momwe i—ine ndikanakhalira pa chirichonse. Mwaona? Zimenezo ndi zoono.

¹⁶² Koma poyamba, inu mukuona, ndi zonse zimenezo...Palibe mmodzi, ngakhale Yesu Mwiniwake ankati, “Mwana sangathe kuchita kanthu mwa Iyeyekha, koma zimene Iye awaona Atate akuchita, zimenezo Mwana amazichita chimodzimidzi.” Ife tikudziwa zimenezo. Yohane Woyera 5:19. Chabwino. “Mwana samachita kanthu mwa Iyeyekha, koma zimene Iye awawona Atate akuchita, zimenezo Mwana azichita chimodzimidzi.” Chabwino.

249. Kodi masomphenya amene munali nawo zaka zapitazo a chozizwitsa chachikulu choti chidzachitike pafupi ndi Corydon, Indiana, anafika pochitika konse?

¹⁶³ Ine ndinayang’ana mu bukhu langa pamene ine ndinapeza ili ndipo ndinaikapo chizindikiro chofunsira. Tsopano, panali pokuti padzakhale nthawi imene ine ndinali—ndimayenera kumadzayang’ana kumene mitengo ya mikunguza iyo...

Basi pamene iwe uyamba kutsika phirilo kumeneko, kumbali inayo, kupita mmusi chaku Corydon, utachoka pamwamba pa phirilo ku New Albany, ine ndinali woti ndisamale mitengo ya mikunguza chifukwa cha ngozi yowopsya imene ine ndikanadzakhala nayo. Ndipo mwa chisomo cha Mulungu, ine ndinapuluma kwa iyo pamene msungwana wamng'ono, akumwa botolo la mowa, anaphedwa—khosi lake linadulidwa apo pomwe ndi botolo limene iye anali nalo mkamwa mwake, msungwana wa usinkhu wa zaka sikisitini, ndipo ine ndikanakhala ndiri apo pomwe pa nthawi imeneyo. Mwaona? Tsopano, izo mwina zikhoza kukhala zimene inu mumazinena. Ine ndinaziwerenga zimenezo.

¹⁶⁴ Ndiyeno aponso, pamene ine ndinali ndi msonkhano uwu mwa M'bale Beanblossom. . . Izo zikhoza kukhala ziri zimenezo. Izo zikhoza kukhala kuti anali Georgie Carter. Mwaona? Iyo inali ina imene inachitika kumeneko. Ndiyeno pali anai kapena asanu a iwo pamenepo. . . ine sindinawone kalikonse koma kamene kanachitika. Ng—ngati munthu amene analemba izi angalembe izo kachiwiri ndi kundiuza ine zimene ine ndinanena pa nthawi imeneyo, ndiye ine ndikaziyang'ana izo. Mwaona? Ngati inu mutangondiuza ine zimene ine ndinanena, masomphenyawo. . . Chifukwa ine ndinazindikira mu masomphenyawo uko zinthu zimene ine ndinaika mu bukhu, ndipo ndi izi apa pamene izo zinachitika monga chonchi. Ine ndinalibe kalikonse kataikidwamo, kamene ine ndinkadziwa, chinthu chotsimikizika chirichonse kunjya kwa icho.

¹⁶⁵ Ndiyeno apo panali chinthu china; icho chinali kutembenuka kwa Omar Price kumusi uko panthawi imeneyo pamene iye anali wotsutsa kwambiri kwa ine. Ndipo inu mukudziwa, iye anabwera ku kachisi ndipo anadzabatizidwa mu Dzina la Ambuye Yesu. O, iye ankamenyana nane molimba kwambiri pa zimenezo; ndipo ine ndinakhala limodzi naye pa nthawi ya usiku. Ine ndinangopitirira kumukonda iye, ndinangokhala pomwepo chimodzimodzi basi; koma potsiriza iye anabwera, chifukwa Ambuye anandiuza ine kuti iye akanati abwere, ndipo kotero i—ine ndinangokhala nazo izo. Mwaona?

¹⁶⁶ Chinthu chofanana ndi mlaliki wamng'ono wakhala kumbuyo kwangu pano. Ine ndinapita uko ku Clarksville kuti ndikayankhule naye iye nthawi ina, kukamuyankhulira iye mu mpingo wa Methodisti, ndipo iye anali wa Methodisti mwathunthu ndi mwathunthu—chimene ine ndikutanthauza. Ine ndinabwerera kuno; ine ndinati, “Tsiku lina ine ndidzambatiza iye mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu.” Ndipo ine ndinatero; ameneyo ndi M'bale Neville!

250. Ngati kuli kolakwika kuti ine kuti—kodi ndi zolakwika kuti ine ndiziyendetsa—sitolo ya zokongoletsa? Ine ndine wokongoletsa ndipo ine sindimakhulupirira kuti Akhristu azidula tsitsi lawo, koma ine ndimawadula ena ndipo

(ine ndikulingalira kuti ndi k-u-l-o-c-h-a, kulocha, izo zikutanthauza mitundu, ine ndikuganiza, sichoncho izo?)

Kuika mitundu naponso.

167 Mlongo wokonedwa, ine ndikanati—ine sindikanadziwa choti ndikuuzeni inu. Mvetserani, ine sindingathe kunena kwa akazi za zimenezo, kuika mtundu mu tsitsi lawo. Ine ndiribe Lemba lotsutsa zimenezo; ine ndingathe kumangokhala ndi Lemba. Mwaona? Lemba silimanena kuti iwo asamachite izo. Lemba limanena kuti iye azikhala ndi tsitsi lalitali, ndipo pambuyo pa izo, ine sindikudziwa koti ndipite. Mwaona? I—ine sindikudziwa kanthu kena za zimenezo.

168 Tsopano, mlaliki wamng'ono amene ali pano penapake ine ndikudziwa, bwenzi wokondeka wa ine, ife tinali kuyankhulana palimodzi tsiku lina ku Blue Boar pamene ife tinali kulandira chakudya. Iye anati, “Mkazi wanga akukhala ngati akuchita manyazi kuti abwere pamaso panu.” Mkazi wachiyero kwambiri, waumalungu, wachichepere, ndipo iye ndi—dona wamng'ono wokongola, gogowamkazi, ndi... Koma iye ndi wabwino, waukhondo, kwenikweni. . . Mkazi wanga amatengeka naye basi mkazi uyu, n—ndipo ine ndikuganiza iye ndi mkazi weniweni, mwenimweni. Iye. . . Ine sindikudziwa ngati iye ali muno; ine ndikulingalira iye ali muno. Ine ndikuganiza mwamuna wake ali muno. Ndipo iye anati kwa ine; iye anati, “Iye analisiya tsitsi lake kuti lizikula pambuyo pa kukumvani inu mukulalikira ndipo iye akuwona kuti izo zinali zoonza, koma,” anati, “iye wakhala akugwiritsa ntchito mitundu ina mu tsitsi lake; ndipo iye akuyesera mwakukhoza kwake kuti apangitse mitundu yonse ichokemo kuti likule iyeyo asanabwere pamene inu muli.”

169 Tsopano penyani, Mlongo wokondeka, ine ndikulemekeza mwapamwamba zimenezo. Ine ndiri nako kulemekeza kwa mkazi amene angachite zimenezo. Kutu mkazi wina kuti angobwera apo ndi kulikonza tsitsi lake mulimonse, kapena kulavulira pa mapazi ako ndi kumayendayenda apo mwamwano ndi mopanda kulemekeza konse, kumbukirani, Yesu anati, “Zimene inu muchitira kwa awa, inu mukuchitira izo kwa Ine.” Mwaona? Ndipo ine ndikulemekeza zimenezo mwa inu, ndipo Mulungu akudalitsani inu chifukwa cha izo.

170 Koma, Mlongo, za mtundu wa tsitsi kapena chinachake chonga izo, i—ine sindikudziwa. I—ine sindingathe kuziikira kumbuyo izo ndi Lemba, kotero i—izo ziri basi kwa inu. Inu mukuona? Inu, ngati inu mukufuna kuti muzichita izo, zimenezo ziri zangwiro bwino bwino ndi ine. Momwe ine ndikudziwira, mpingo ulibe mwambo woterowo. Ngati inu mukufuna. . . Chirichonse chimene mulibe mu Baibulo ili, chabwino, inu basi. . . Zimenezo ziri kwa inu. Inu mukuona? Koma ine ndingangokupatsani inu langizo langa, inu mukuona, ndi momwe ine ndikanadziwira. . . Inu mukudziwa, basi ndi

chibadwa cha mkazi kuti aziwoneka wokongola; iye amayenera kuti azikhala mwanjira imeneyo.

¹⁷¹ Inu mukudziwa, mu moyo uliwonse umene ulipo, champhongo ndicho chokongoletsetsa, kupatula mtundu wa umunthu. Mukatenga mbalame iliyonse, ng'ombe. Kutenga gulu la ng'ombe. Nditi iti yokongoletsetsa, ng'ombe yokalamba ya nyanga-zokwinyika kapena nkhuzi yaikulu? Tengani gwape; ndi uti, wathazi kapena tonde? Tengani gulu la mbawala; yokongoletsetsa ndi iti, yatonde kapena yathazi? Insa, chirichonse chimene inu mukufuna kuti muchite. Tengani i—tengani izo mwa mbalame; tengani izo mwa nkukhu, tambala kapena nsoti? Tengani izo mwa mbalame, yaing'ono—yamphongo yaikulu yokongolayo kapena nsoti wawung'ono wamangamangawo, utakhala pa chisa chake ndi kumautamira mazira ake? Mwaona? Chirichonse mu mtundu wonse, nthawizonse—champhongo ndicho chokongoletsetsa, koma wamkazi kwa umunthu. Bwanji? Iye anayambitsa kugwa. Satana anamusankha iye apo pomwe, ndipo kukongola ndi kwa mdierekezi. Mwaona?

¹⁷² Satana anali mngelo wokongola kwambiri. Iye anali mkerubi amene ankaphimba. Penyani kusiyana kwake momwe akazi akukhalira. Ndi angati akumukumbukira Pearl—anawerenga za Pearl O'Brien? Tiyeni tiwone manja anu, ena a inu anthu achikulire. Zedi. Mwaona? Akuyenera kuti anali mkazi wokongola kwambiri mu Amereka. Msungwana wa mu zaka khumi aliyense wonyang'ama pa msewu angakhale wokongola pawiri mwa momwe iye aliri tsopano. Bwanji? Ndizo ndendende basi zimene Baibulo linanena: “Pamene ana a Mulungu anawawona ana aakazi a anthu kuti anali okongola...” Limenelo linali gulu la zigawenga limene linapangitsa chigumula pamwamba pa dziko lapansi, kuti Mulungu anawononga mtundu wonse wa umunthu. Mwaona? Ndizo ndendende. Ndipo lero chirichonse maziko ake ndi Hollywood n—ndipo kukongola ndi zinthu munga zimenezo, pamene kukongola chiri chinthu chachinsinsi cha mtima (mwaona?) ndipo osati mawonekedwe akunja. Asiyeni iwo azidzikongoletsa okha, osati ndi mawonekedwe akunja, koma amkati, a kufatsa, mzimu woleza. Uyo—ameneyo ndiye Mkhristu.

Kotero tsopano, pa funso lanu, Mlongo, ine sindikudziwa basi zoti ndikuuzeni inu.

Tsopano, ine ndikhoza kuima panali pano kapena kutenga maminiti ena sate ndiye, ndiyeno...Kodi maminiti sate angati...? Ndi angati angakhale alipobe maminiti ena sate, ndiyeno zimenezo zitipatsa ife kanthawi kowonjezera pang'ono usikuuno. Chabwino, ine ndithamanga mofulumira ndiye.

251. M'bale Branham, kodi l Timoteo uyu 2:9 akutanthauza kuti mkazi sangathe kuluka tsitsi lake? Kodi tsitsi “lotiwidwa” limatanthauza tsitsi “lolukidwa?”

¹⁷³ Tsopano penyani, Mlongo, tsopano izi...I—ine ndikukondwa kuti ilo latsatira ili. Ine sindinachite kuliika ilo pamenepo, koma basi i—ilo latsatira mwabwino chotero.

Zindikirani, tsitsi lolukidwa mu tsiku limenelo linali chisonyezo cha mkazi wamumsewu; izo ndi zimene iye ankachita, ankaliluka tsitsi lake. Ndipo Paulo ananena kwa Akhristu, “Tsopano, kakongoletsedwe, kasakhale ka kuluka...” (kapena ‘kutiwa’ ndi ‘kuluka’ ndi chinthu chofanana)—kuluka tsitsi lawo, chifukwa izo zinkawoneka ngati dziko lina lonse.

¹⁷⁴ Tsopano, inu simukuyenera kuti muziwoneka monga dziko kapena kumachita monga dziko! Mwaona? Akazi akuyenera kuti azikhala osiyana pamenepo. Mwaona? Ayi, tsopano, kuluka tsitsi... Tsopano, lero tsitsi lolukidwa ndi lokongola, ndipo liri ulendo wautali kuchokera ku fashoni ya mdziko. Tsopano, inu mumawawona akazi, momwe iwo akuchitira ndi tsitsi lawo lero... Muzingolisunga tsitsi lanu mu njira iliyonse; kungoti musamawoneke ngati dziko! Mwaona? Musati muziwoneka kapena kuvala monga ilo! Ngati iwo akuvala akabudula, inu muzivala diresi. Ngati i—ngati iwo akuchita tsitsi lawo lonse—kulimeta ilo lonse ndi kulidula ilo, ndi kumachita izo konse... I—i—inu mungolisya lanu lokha. Mwaona?

¹⁷⁵ Ndipo kuluka—koma lolukidwa...Funso linali: Kodi “lolukidwa” limatanthauza—“lotiwidwa” kutanthauza “lolukidwa”? Inde, uko nkulondola. Ndipo tsopano, pa msewu...

¹⁷⁶ Tsopano, ine ndinaziyang’ana izo bwino kuti ndipezepo zaka zapitazo chimene tsitsi “lolukidwa” linkatanthauza. Mwaona? Mkazi, mwakuchita, akazi akale, iwo ankangolikokera tsitsi lawo mmbuyo ndipo ankalamanga ilo, mochuluka ngati nhira wa kavalo lero. Ndipo iwo ankayendayenda... Iwo ankakhala atavala mikanjo monga choncho, koma akazi apa msewu ankatenga tsitsi lawo ndipo ankaliluka ilo pa mitu yawo ponse, ndi kulimanga ilo mozunguza monga choncho, ndi kuika maluwa mu ulo ndi zinthu monga choncho, ndipo izo zinali ngati—wodzigwedeza pa msewu; monga momwe ife tingamuwone wodzigwedeza lero, momwe iye amavalira. Ine ndikuti *wodzigwedeza*, chifukwa inu mukudziwa ndine bambo wachikulire; kotero icho ndi chimene iwo ankawatcha iwo mu masiku amenewo. Kodi iwo akuwatcha iwo chiani lero? I... Mai, ine sindikudziwa. *Anapiye* kapena chinachake kapena chimzake. Kotero... Chirichonse chimene icho chiri. Apatseni iwo dzina la mtundu uliwonse, iwo amalikonda ilo.

252. M'bale Branham, inu munanena pa imodzi ya matepi kuti Nowa anapulumutsa apanyumba ake. Kodi izi zikutanthauza mayi akhoza kukhala ndi chikhulupiriro chofanana kwa apanyumba ake? Ndipo kodi izo zikutanthauza kuti aliyense wa pa banjapo adzapulumutsidwa ngati ife titakhulupirira izo?

¹⁷⁷ Tsopano, izo ndi—eya, izo ndi zokhala ngati . . . Inu muyenera kusamala momwe ine nditi ndiyankhire ili tsopano. Mwaona? Choyamba, “Inu munati . . . (Tsopano, ndiloleni ine ndiwone bwino.) Inu munanena pa imodzi ya matepi anu kuti Nowa anawapulumutsa apanyumba ake.” Bwanji? Chifukwa iwo anakhulupirira. Ndi zimenezo, chifukwa iwo anakhulupirira uthenga wake.

¹⁷⁸ “Kodi izi zikutanthauza kuti mayi akhoza kukhala ndi chikhulupiriro chofanana kwa apanyumba ake?” Inde, Mlongo! Ine ndikutha kuwona mtima wa mayi wamng’ono ukulirira anthu ake. “Ndipo kodi izi zikutanthauza kuti aliyense wa m’banjamo adzapulumutsidwa ngati ife tikhulupirira izo?” Inde, ngati iwo ati azivomereze izo. Ndiko kulondola.

¹⁷⁹ Kumbukirani wamndende waku Filipi. Khulupirira pakuti inu nonse . . . Ngati iwe uli nacho chikhulupiriro chokwanira kwa chipulumutso chako chako, kodi iwe sungathe kukhala nacho chikhulupiriro icho chomwe chimene chidzagwire ntchito pa anthu anu? Kodi chikhulupiriro ndi chiani? Ndi mphamvu yosawoneka. Mwaona? Ndi chiani—ndi chiani—ndi Mzimu. Mzimu Woyera umabweretsa chikhulupiriro. Mwaona? Ndi mphamvu yosawoneka.

¹⁸⁰ Chifukwa chiani ine ndingamaike manja pa odwala? Mwaona? Ngati ine ndingathe kukhala ndi kukhudzana nao kwandekha ndi mzimu umene uli mwa munthu ameneyo pamenepo, chinachake chingachitike. Mwaona? Apa pamaima Mzimu Woyera; Iye amawulula zinsinsi za mu mtima. Iye achita ndendende basi zimene Iye ananena kuti Iye adzachita mu tsiku lotsiriza. Anthu amakhulupirira zimenezo; iwo amayang’ana pa izo, “Inde, bwana, ine ndikuzikhulupirira izo.”

¹⁸¹ Tsopano, ngati ine sindingati ndingokhala wawamba kwambiri kwa inu (mwaona?)—kumakhala chinthu chawamba chabe. Inu muzingothamanga kudutsapo tsiku lina ndi kungothamanga kudutsapo tsiku lotsatiranso. Mwaona? U—uko ndiko kungotengerapo mwayi. Inu simuli kuzikhulupirira izo pa kuyamba pomwe (mwaona?), chifukwa mwamsanga basi pamene inu mukhulupirira kwenikweni izo . . . Mkazi uja anati, “Ngati ine ndingathe kukhudza chovala Chake, ine ndipangidwa kukhala wamphumphu pa chidutswa chirichonse,” ndipo iye anachita izo. Mwaona? Iye sananene kuti, “Siyani ine ndiyesere izo kachiwiri.” Mwaona? Iye anakhulupirira izo. Mwaona? Ndizo—ndizo . . .

182 Tsopano, ngati inu mutati mungokhulupirira ndi zonse zimene ziri mwa inu kwa banja lanu. . .

183 Tsopano, monga apa, nchiani chimandipangitsa ine? M—mphamvu iyi ndi chiani mu nkono wanga? Iyo ndithudi si akatumba anga, ndi mzimu wanga. Ndithudi, mukatulutsamo mzimu umenewo, ndiyeno akatumba awa achita chiani? Iwo akhala okufa momwe iwo angakhalire. Mwaona? Iwo avunda, koma ndi. . . Mukuona, ndi mzimu umene umalimbikitsa.

184 Tayang'anani pa Samsoni wamng'ono. Ambiri a iwo ankawona zitseko zinkawoneka ngati pakati pa mizati iwiri iyi apa. Bwanji, mwamuna wamkulu chotero angayambane nawo mkango ndi kuwukhadzula iwo mzidutswa, M'bale Jackson. Mkango utalumphira pa mwamuna wonga ameneyo ndi chitseko—wokhala ndi mapewa onga chitseko cha barani, bwanji zedi, zimenezo sizikanakhala zozizwitsa ayi; koma chozizwitsa chinali, iye anali basi kachiwala kakang'ono kwambiri ka mutu wa tsitsi lotiwidwa, wamng'ono kwambiri, munthu wamkulu, pafupi—wachikazi pang'ono, mnyamata wamng'ono wa amayi, mangongo asanu ndi awiri achikazi akulendewera kumbuyo kwake. Koma inu mukazindikira, iye anali wopanda chomuthandiza monga chirichonse mpaka Mzimu wa Ambuye utabwera pa iye. Ndipo pamene Mzimu wa Ambuye ubwera pa iye, mkango umenewo unathamanga ndipo unabangula, iye anangowukhadzula iwo mzidutswa. Uyo sanali Samsoniyo; Uwo unali Mzimu wa Ambuye.

185 Tsopano, iye angatenge bwanji fupa la chibwanu cha bulu, limene linali liri ku chipululu kuja ndipo chitasuluka kukhala loyera. . . Ndipo zipewa za Afilisti zimenezo zinali pafupi inchi kukandapala kwa mkuwa wolimba. Chabwino, inu mukatenga chibwanu chimenecho ndi kuchimenyetsa icho pa chimodzi cha zipewa zimenezo, icho chingapite mu zidutswa chikwi. Inu mukudziwa zimenezo. Iwo akanamenya, chibwano chakale chowuma icho. . . Koma penyani pamenepo, iye anaima pamenepo ali ndi fupa la chibwano icho mdzanja lake ndipo anawakanthira pansu Afilisti chikwi; ena onse a iwo anathawira ku mathanthwe. Iye anati, “Zibwerani kuno, inu mukufuna zina za izonso?” A—apobe atagwirizira icho! Kodi chinali chiani icho? Mzimu wa Ambuye unadza pa iye. Mwaona?

186 Choncho, Uwo ndi Mzimu wa Ambuye. Ndipo pamene inu muli nawo Mzimu wa Ambuye mwa inu kuti mukukhulupirira kwa chipulumutso chanu chomwe, chiikeni icho pa banja lanu. Kuti, “Ine ndikudzitengera iwo mu Dzina la Yesu Khristu; ine ndikudzitengera ilo! Mulungu, ine sindikudziwa momwe Inu muti mupangire kuti iye achite izo, ndi momwe Inu muti mumupangitsire iye kuti achite izo, koma ine ndikukhulupirira izo. Ine ndikukhulupirira izo, Ambuye! Thandizani kusakhulupirira kwanga.” Dzitengereni izo ndipo penyani zomwe ziti zichitike. Icho chichita izo.

253. Kodi Mkwatibwi—kodi Mkwatibwi asanabwere Yesu, kodi Iye adzakhala nazo mphamvu zonse za Mzimu Woyera kuti azidzachita zozizwitsa, kuwukitsa akufa, ndi zina zotero monga mu mvula ya masika—kapena kodi mvula iyi ya masika ndi ya kwa Ayuda 144,000? Kodi atumiki onse adzakhala nazo izi, kodi ife—kapena kodi ife tikuyembekezera kudzako kokhako?

¹⁸⁷ Inde. Ukuona, mzanga, i—i—ine sindine wafioloje. Ine sindine wafioloje; choncho, ine ndimayenera kuti ndiziphunzitsa zonse zimene ine ndikudziwa za Baibulo kuchokera ku mithunzi ndi zoimira. Inu mumakhala ngati mumanditcha ine wofanizitsa. Koma ngati ine ndingayang’ane pa khoma ilo, ndipo ine ndisanayambe ndadziwonapo ndekha; ndipo ine poyang’ana, ndipo ine ndingathe kuwona kuti ine ndiri nawo mutu, ndi makutu, ndi manja, ndipo—ine ndidziwa chinachake cha momwe ine nditi ndidzawoneke monga ngati ine nditi ndidzaziwone ndekha konse. Mwaona? Ngati ine ndiwona kuwonekera kwanga pa kalilole, ine ndidziwa momwe ine ndikanaonekera ngati ine ndikanatha kuyima pambali ndi kudziyang’ana pa ndekha.

¹⁸⁸ Tsopano, umo ndi momwe ine ndimaganizira za Baibulo. “Zinthu zonse izi,” Aroma 26 anati, “zinachitika kwa zitsanzo zathu.” Ife tikhoza kumayang’ana mmbuyo ndi kuwona zomwe izo zinali, monga mwezi kunyezimiritsa dzuwa. Ife tidziwa chimene dzuwa liti lidzakhale pamene—ngati ife sitinayambe taliwonapo dzuwa; ife tikhoza kuwuwona mwezi, ndi kuwona kuti ilo lidzakhala lopambana kuposa uwo. Chabwino, pamene inu muwona zimene zinkachitika mu Chipangano Chakale, ndi chinyezimiritsa basi cha zimene zikuchitika mu Chatsopano.

¹⁸⁹ Tsopano, mkati umu, ine ndikukhulupirira ndi mtima wanga wonse i—ife tiri, kapena masiku ano. . . Ngati ife sitiri, winawake ali; izo zikuyenera kukhala ziri. Nthawi yatha; ife tiri pa mapeto!

¹⁹⁰ Yense. . . Dziko. . . Mulungu anapanga dziko mu zaka zikwi zisanu ndi chimodzi, ndipo chikwi chachisanu ndi chiwiri Iye anapuma. Iye anati munthu sadzakhala konse moyo nthawi imeneyo nkuitsiriza—c—chaka—kapena—kapena tsiku—“tsiku limene iwe udzadye, tsiku limenelo iwe udzafa.” Adamu—kapena Metusela anali munthu wamkulu kwambiri amene anayamba wakhalapo moyo mu Baibulo, ndipo iye anali wausinkhu wa zaka 969; ndipo iye sanakhale moyo konse zaka Chikwi zija. Koma munthu amene ati adzakhale moyo kupyola mu Zakachikwi, zaka chikwi chimodzi, nkuti asonyeze k—kuti chilango chinalipiridwa kale. . . Munthu akukhala moyo kwanthawizonse; tsiku latha; nthawi yatha; iwo ali mu muyaya.

¹⁹¹ Tiri chiyankhulire, ine ndalandira makalata ochuluka kwambiri pa uthenga wanga wa ma Lamlungu awiri kapena atatu apitawo pa—*Kwawo Kwa Mtsogolo kwa Mkwatibwi ndi*

Mkwati. Zimenezo ndithudi zinawakhudza pamalo ambiri a iwo. I. . . Izo zinatero kwa ine aponso. Ine sindinafike pondithera izo.

¹⁹² Tsopano, zindikirani. Pa izi (mwaona?), Abrahamu anawona. . . Tsopano, monga Iye ankachitira naye Abrahamu, chomwechonso Iye akuchita ndi mbewu yake. Tsopano, limodzi la masiku awa pamene ine ndidzabwerera nthawi ina, ine ndikufuna kuti ndidzatenge izo pafupi mochuluka pang’ono ndi kudzakuwonetsani inu ndendende malo a moyo wa Abrahamu. Zinali ndendende ndi Lutera, Wesile, ndipo mpaka mmusi kufika kuno, ndendende basi momwe Iye anachitira ndi mipingo monga Iye ankachitira ndi Abrahamu; momwe Iye anawonekera; momwe kuti apo pamene Iye anatsimikizira pangano kwa iye pansu pa magari okhetsedwa, uwo unali m’badwo wa Filadefia. Inde, bwana, umenewo unali m’badwo wa magari, Lutera—m’badwo wa Wesile.

¹⁹³ Komano penyani m’badwo wa Chipentekoste. Iye atafika kale kumeneko, Iye anapanga lonjezo la *El Shaddai*, “yamwa kuchokera kwa Ine.” Funso ndi lakuti: Kodi inu mungayamwe? Izo zinabweretsedwa pamaso pa Achipentekoste. Mwaona? Kodi inu mungayamwe? Koma iwo sanachite izo; iwo anambwandira awo—mabere a ku chipembedzo kumene iwo anatulukako. Komano Mbewu, Mbewu yeniyeni, inabwera apo kuti idzayamwe mabere amenewo.

¹⁹⁴ Ndipo kodi chizindikiro chotsiriza chimene iwo anali nacho chinali chiani, asanafike mwana wolonjezedwa uja amene anali atamudikirira zaka zonse izi, pamene Iye anabwerera? Iye anali Mulungu ataima mu mawonekedwe a Munthu ndipo ankakhoza kuzindikira maganizo amene anali mu mtima wa Sarah (Sarah pokhala Mpingo, woimira Mpingo)—kuzindikira maganizo amene ali mu Mpingo umene unali ngakhale kumbuyo kwa Iye. Ndi kulondola uko? Ndipo mwamsanga zitachitika zimenezo, iye anasintha nabwerera ku utsikana ndi iye mnyamata; ndipo Isaki anabweretsedwa powonekera, mwana wolonjezedwayo.

¹⁹⁵ Ine ndikukhulupirira kuti inu mukuwona chinthu chotsiriza chimene chiti chichitike kwa Mpingo usanachitike mkwatulo. Ndizo ndendende. Ine ndikukhulupirira zimenezo. Mvula yatha. Ingowerangani mitu itatu yoyamba ya Chivumbulutso ndipo inu muwona zimene zalonjezedwa kwa Mpingo. Izo ndi zimene zinalonjezedwa, Mpingo, apo pomwe—mibadwo ya mpingo.

¹⁹⁶ Inu munazindikira tsiku lina pamene ife tinayamba malipenga aja, Mzimu Woyera unati, “Zimenezo si za kuno.” Mukuona, mwaona?

¹⁹⁷ Tsopano, mvula ya masiku, Ayuda 144,000, ayi, izo si zimenezo—i—iwo sadzati—izo—ndi pamene Eliya ndi Mose. . . uko ndi kumene zozizwitsa ziti zikachitike. Zinthu zimene anthu akhala akuziyembekezera, Achipentekoste, pofuna zozizwitsa,

uko ndi kumene izo ziti zidzachitikire mmenemo—pansi pa iwo. Mukuona, umenewo ndi wa Eliya ndi Mose. Iwo akukantha dziko lapansi ndi matemberero mowirikiza momwe iwo afunira; iwo akutseka miyamba kuti isavumbe mu masiku a uneneri wawo. Ndipo Mulungu adzaima ndi kumawamenyera iwo monga Iye anachitira, ndipo Iye adzawatulutsamo iwo pansi pa dzanja lamphamvu chimodzimidzi basi monga Iye anachitira ku Igupto (mwaona?), kuwachotsa ku “machitidwe” awa a mdziko. Ndipo Iye adzachita zimenezo, koma zimenezo sindizo . . .

¹⁹⁸ Ife tiri woti tizingodikirira pa kudza kwa Ambuye. Zingodikirirani; sungani nyali zanu zitakonzedwa, zonse zikhale zodzaza mafuta. Zipempherani ora lirilonse, osati tsiku lirilonse, ora lirilonse. Muzingokhala okonzeka; khalani okonzeka, khalani okoma, ndi kuyang’anira . . .

O, tikudikirira kudza kwa tsiku lokondwa la Zakachikwi ilo.

Pamene Ambuye wathu odala ati adzabwere ndi kudzamtengera Mkwatibwi Wake woyembekezera napita.

O, mai—o, mtima wanga wadzadza ndi mkwatulo pamene ine ndikuvutikira, kudikirira, ndi kupemphera,

Pakuti Ambuye wathu akubweranso padziko kachiwiri.

Ndi zimenezotu; ndicho chiyembekezo cha Mpingo ora lino.

254. Kodi Dzina la “Yesu Khristu” ndi labwino kwa ubatizo, kapena kodi izo zimayenera kumakhala mu Dzina la “Ambuye Yesu Khristu”?

¹⁹⁹ Liri lenselo. Ine ndimatenga la *Ambuye Yesu Khristu* (mwaona?), chifukwa ine ndikuganiza Iye ndi Ambuye wathu. Tsopano, *Dzina la Yesu* chabe, monga ena mwa abale athu amabatizira, i—ine ndimasiyana nawo pamenepo (mwaona?), chifukwa ine ndikudziwa ine ndiri nawo abwenzi ambiri dzina lawo Yesu, ochuluka a—ochuluka a amzanga olalikira ku Mexico, n—ndi Italy, ndi ena otero. Iwo amawatcha iwo *Yesu*, ndipo koteru *Yesu* si zokwanira. Iye anabadwa ali Khristu Mpulumutsi, monga Iye anabadwa ali Mpulumutsi, Khristu, wodzozedwayo. Ndipo masiku asanu ndi atatu kenako Iye anapatsidwa dzina la *Yesu*. Mwaona? Ndiye Iye anali Ambuye Yesu Khristu. Ndi chimene Iye anali. Chabwino.

255. M’bale Branham, kodi Ambuye angakulolezeni inu kuti mutilangize ife pa funso la chikwati ndi chilekano pa nthawi ino? Funso: Kodi mwamuna angakwatire mkazi ndi kusudzulidwa ndi iye ndiyeno nkukwatira winanso? Ngati onse a iwo akwatira wina, kodi iwo onse akuchita chigololo? Inu munatchula kuti izo zidzalumikizana mu mbewu ya serpenti. Mmotani izo?

200 Tsopano, pano—pano pali limodzi la mafunso ovutitsitsa kwambiri amene ife tiri nawo mu mulu uwu, ndipo ilo ndi lofunsidwa kwambiri m—m—mu dziko lero. Tsopano, ndimveni ine, ndipo ine ndiri nacho chifukwa cha izi. Ngati ine ndikanabweretsa kwenikweni kwa mpingo uno ndi pa tepi iyi mmawa uno, chinthu cholondola cha pa chikwati ndi chilekano, izo zingaphwasule mpingo uliwonse mu dzikoli, ngati iwo atamvetsera kwa izo. Mwaona? Ndiko kulondola.

201 Tsopano, kotero ndithandizeni ine, apa pali Baibulo patsogolo panga, ine ndiri naye pa funso limenelo, PAKUTI ATERO AMBUYE! Ndipo mbali zonse zimene zikutsutsanazo ziri kulakwitsa. Onse amene amakwatitsanso wokwatiwayo ndi zina zotero, iwo onse akulakwitsa pa zimene iwo akuchita, koma pakati pakepo pali Choonadi, pakati pa msewu. Ine sindikufuna kuti. . . Ine ndipanga tepi kaya ngati chinachake chindichitikira ine, ndiye abale akhoza kumaisewera iyo ine nditapita kale (mwaona?) kwa mipingo. Koma i—ine ndikufuna kuti ndipange tepi pa izo ndi kungokusonyezani inu pamene izo ziri; koma mpaka ine nditi ndimverere kutsogozedwa ndi Ambuye, ine sindinena kalikonse za izo. Koma ine ndikumverera kuti pa zinthu izi kuti ine ndikuyenera kumatsogozedwa ndi Ambuye; ngati ine sinditero, ine ndichita zowononga kwambiri kuposa mmene ndingachitire bwino. Mwaona?

202 Tsopano, ine ndikufuna kuti inu muzindikire ichi. Funso: “Kodi mwamuna angakwatire mkazi ndi kusudzulidwa naye iye ndiyeno mkukwatira wina; ndipo ngati onse a iwo akwatira wina, kodi onsewo akuchita chigololo?” Tsopano, bwenzi wanga, ine sindikufuna kuti ndivulaze kumverera kwanu, koma zimenezo ndi Choonadi. Yesu anati, “Aliyense amene akwatira uyo amene wachotsedwayo achita chigololo.” Mwaona? I—ine sindikufuna basi kuti ndinene zimenezo, koma icho ndi Choonadi.

203 “Inu munanena kuti izi zidzalumikizira mu mbewu ya serpenti.” Mwaona? Ine sindikukumbukira kuti ndinanena zimenezo, koma mwinamwake ine ndinatero penapake, ndinanena chinachake cha izo.

204 Monga tsiku lina, ine ndinasakaniza chinachake, ine ndinapezeka kuti ndinamvetsera izo, ndipo izo. . . ine ndinazigwira izo apo pomwe; ndipo izo ziri pa tepi, ndipo i—ine mwinamwake ndizimva kuchokera pamenepo. Pamene ine ndinali kuyankhula za Malipenga Asanu ndi awiri, ine ndinanena kuti anali malipenga asanu ndi awiri. Ine ndimalozera ku phwando la Chipentekoste. Kuchokera pa phwando la Chipentekoste mpaka asanu ndi awiri—mpaka—Malipenga, apo panali Masabata asanu ndi awiri. Masabata asanu ndi awiri anali pakati pa Phwando la Paskha kukafika pa Pentekoste (inu mukuona?), zimene zinkapanga masiku fifite. Mukuona? Koma chimene ine ndinali kulozera kwa

icho, pokhala kuti, ine ndinati, “Izo zikutanthauza Mibadwo ya Mpingo Isanu ndi iwiri.”

205 Pa tepi imeneyo (ngati inu mudzapezeka mutsaipeza iyo kapena chirichonse)—pa tepi imeneyo ziyenera kukhala, kuti mwezi wachisanu ndi chiwiri zitachitika kuti zimenezo zinkabweretsa umo p—Phwando la Malipenga, limene linkatanthauza Mibadwo ya Mpingo Isanu ndi iwiri—miyezi isanu ndi iwiri, osati Masabata asanu ndi awiri. Masabata asanu ndi awiri anapita kwa . . . Ine ndinafotokoza izo pamenepo. Ine ndinati Masabata asanu ndi awiri, monga choncho, komano ine ndinapitirira nalo lingaliro lomwelo mopitiriza, pamene uli mwezi wachisanu ndi chiwiri litachitika Phwando la Paskha—kapena Phwando l—la Pentekoste, ndiye pamabwera phwandolo, mtolo utabweretsedwa umo, utaweyulidwa. Inu mukuona nd—ndiye . . . Kumbukirani pamenepo, mtolowo ukusandulika kukhala mtanda wa mkate itatha nthawi imeneyo. Mwaona? Pamene—mtolo w—mtolo umodzi, ndiye wonsewo ukupita mu mtanda umodzi. O, ndi kuphunzitsa kwakukulu pamenepo; ine sindinakhudze mphepete mwa zimenezo. Koma ngati zichitika kuti inu mwazigwira izo pa tepi yanu, kumbukirani, kayang’aneni mu Baibulo. Inu mukawona, iyo ndi miyezi isanu ndi iwiri zitatha zimenezo. Kuwerenga miyezi isanu ndi iwiri: Januwale, Feburuwale, Malichi, Epulo, Meyi, Juni, ndi Julayi—angakhale ali Julayi, miyezi isanu ndi iwiri, imene ikuimira Mibadwo ya Mpingo Isanu ndi iwiri yamphumphu. Mtumiki wina akhoza kuzitola zimenezo, ndiye inu mukhoza kukhala nazo izo, inu mukaziwona pamenepo. Chabwino.

206 Tsopano, pa izi apa, t—t—tiyeni tingokhala ngati . . . Inu . . . Izi ndi zimene ine ndikunena. Ndiroleni ine ndinene izi, si Ambuye, ndiroleni ine ndinene izi. Ngati inu muli wokwatira pa nthawi ino, ndipo inu nonse ndinu opulumutsidwa, ndipo ndinu odzazidwa nao Mzimu Woyera, ndipo inu mukukondana wina ndi mzake, ndipo inu muli nao ana aang’ono (tsopano, kumbukirani uyu ndi ine, osati Ambuye. Mwaona?), pitirirani nazo kumakakhala limodzi; khalani okondwa; chifukwa inu simunathe kukhala naye mkazi wanu woyamba kapena inu simukanati mukwatire. Ndiye ngati inu muti mumusiye uyu ndi kubwerera kwa woyamba wanu, inu mukuchita moyipitsa kuposa momwe inu munachitira pamalo oyambawo. Mwaona? Koteru inu mukuwona, inu mwangodzisokoneza yense; apo palibe njira yochokera kwa zimenezo. Pangakhale njira imodzi yokha moonna imene ine ndingainene kuchokera mu Baibulo: nonse inu kukhala mbeta. Mwaona?

207 Tsopano, koma . . . Iyo ndi njira yokha imene ine ndingathe kuinena pakali pano, koma pali chinthu china mmenemo, chimene i—ine sindingathe kukuuzani inu tsopano, ndipo chifukwa chimene ine ndikuti, “Si ine, koma Ambuye, zipitirirani nazo.” Ngati inu mudzazibweretse izo konse kwa

tepi, ndipo tsiku lina, ngati ine ndidzazibweretsa konse izo, inu mudzakumbukire momwe ine ndanenera izo. Ngati inu mukanakhala anzeru, inu mukanatha kuzigwira izo apo (mwaona?), pa momwe ine ndinanenera izo pamenepo, ndiyeno inu mukanadziwa.

256. M'bale Branham kodi ife tizipita ku mipingo ina ngakhale pamene iwo akutsutsana nanu?

²⁰⁸ Zedi, inde! Yesu ankatero pamene iwo ankatsutsana naye Iye. Pitirirani kutero. Ife tikuzindikira apa, akuti, “Kodi ife tizipita ku mpingo wina umene amatsutsana ndi inu?” Zedi, ine sindikuti. . . Ine sindine nsangalabwi yokha pa doko, inu mukudziwa. P—pali amuna ena aumulungu kulikonse; ine ndikuyembekeza ndine mmodzi wa iwo. Mwaona? Koma musati konse muzifika kumusi kuno. . .

²⁰⁹ Ine ndinaitanidwira mu chinachake chonga ichi tsiku lina. G—gulu mu Arizona linaitanira tcheru changa kwa izo. Mwaona? Gulu la atumiki linati, “Chinthu chokha chimene ife tiri nacho motsutsana ndi inu, M'bale Branham, ndi (chimodzi cha zinthu) anthu amene amabwera kuno ndi inu, ife timalephera kuti tiwapangitse iwo kuti azipita ku tchalitchi kulikonse.” Anati, “Iwo ali ndi ana ndi chirichonse; iwo samapita ku tchalitchi.” Ndipo anati, “Chabwino, ife tinawauza iwo kuti iwo anali olandiridwa kuti azibwera—azibwera ku tchalitchi chatu.”

²¹⁰ Tsopano, ine ndikudziwa iwo amaika kupanikiza pa inu ndipo amafuna kuti inu muwajowine, koma inu simukusowa kuti muwajowine; koma ayikeni ana amenewo mu Sande sukulu kwinakwake! Ndipo inu muzipita ku tchalitchi; musati muzikhala kunyumba, kumapita kokawedza, ndi kukasaka, ndi zinthu monga zimenezo Lamlungu.

Inu mukuti, “Chabwino, ine sindine wamwamalamulo.”

Chabwino, inu kulibwino mukhale mu chikhalidwe chimenecho kwa kanthawi, kusalemekeza chiukitsiro cha Khristu. Inu muzipita ku tchalitchi kwinakwake!

²¹¹ Ngati i—ngati ine ndikanapita. . . Ngati ine sindikanatha kupeza. . . Ngati ine ndikanapita ku mpingo *winawake* umene ine ndikudziwa kuti pali chinthu chimodzi chokha chimene anthu amenewo anayamba anenapo chimene ine ndikuchihulupirira—iwo atati iwo amakhulupirira Yesu ndi Mwana wa Mulungu. Iwo atanena zimenezo (ine ndikukaikira izo), koma ine ndingamapite kumeneko kumakawamvera iwo akunena zimenezo. Mwinamwake inu mukuti. . . Umenewo ndi mpingo uwu, mwinamwake mpingo winawo ungakhale chinachake monga wa Baptisti. Iwo amati, “Eya, ine ndikuhulupirira kuti iwe uyenera kukhala ndi chokuchitikira.” Ine ndinga—ine ndingamapite nawo iwo pa izo. Ndiye ine ndikuhulupirira kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu;

ine ndikukhulupirira kuti iwe umayenera kukhala ndi chokuchitikira. Chabwino.

²¹² Ndiye mwinamwake pali a Assemblies of God. Tsopano, iwo amakhulupirira. . . Mwaona, ine—tsopano ine ndikhoza kudya mwina pafupi zidutswa zitatu kapena zinai za mkate ndi iwo (mwaona?), chifukwa iwo akukhoza kukhulupirira. . .

²¹³ Monga tsiku lina, munthu uyu yemwe anaimba ndipo amafuna kuti adziwe za zimenezo, ndipo anati, “Inu munati. . .” (Mtumiki uyu kunjira uko, munthu uyu kumusi uko amene ankafuna kuti tikambirane zimenezo. M’bale wosauka, iye ali mu chisokeletso chotero.) Iye anati, “Chabwino, M’bale Branham,” mukuona, iye anati, “iye akutsutsana ndi inu ku Assemblies of God.” Ndipo ngati mtumiki wa Assembly apezeka atatanga tepi iyi, ine ndikufuna kuti inu mudiuze ine ndi liti pamene ine ndinayamba ndatsutsanapo ndi munthu wa Assembly of God kapena munthu wina aliyense! Nchifukwa chiani kuti, pamene malikulu anu omwe akuvomereza kuti ine ndakutumizirani inu firii kotala ya milioni ya ana anga amene ine ndawabalira kwa Khristu? Ine ndikutsutsana nawo chotani a Assemblies of God? Chifukwa chiani ine ndikutsutsana nawo aumodzi? Ine sindikutsutsana nawo aumodzi, Assemblies of God, Mpingo wa Mulungu, kapena munthu aliyense! Ine ndikutsutsana ndi kachitidwe kalikonse kamene kamawalekanitsa anthu.

²¹⁴ Penyani, ine ndawatumizira a Assemblies, mwa kuwerengera kwawo komwe, firii kotala ya milioni ya ana anga omwe. Ngati iwo ali oyipa chomwecho, bwanji ine ndinachita zimenezo? Bwanji? Ine ndikuganiza kuti ndi opambana omwe alipo mu dziko kuti ndiwatumizeko iwo—kaya aumodzi kapena—ena a chikhulupiriro cha Chipentekoste, chifukwa iwo amakhulupirira mu machiritso Auzimu; iwo amakhulupirira mu zauzimu; iwo amakhulupirira mu ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndizo zopambana. . . I—ine sindingathe kuwabweretsa iwo onse komwe kuno; iwo ali konsekonse mdzikomu. Ine ndiri nawo abwenzi konse konse mdziko, ana amene ndawabalira kwa Khristu. Ine ndimawatumiza iwo kwa opambana. . . Kodi inu munayamba mwandimvapo ine pamene ine ndikupanga kuitanira ku guwa? Ine ndimati. . . Pamene ine ndimawatengera iwo pamwamba apo ndi kuwafikitsa iwo populumatidwa, ine ndimati, “Tsopano, inu muzipita ku mpingo wina wabwino wa Uthenga Wamphumphu ndipo inu mukazipezere mpingo wa kwana.” Ndi angati anayamba andimvapo ine ndikunena zimenezo? Zedi, zedi. Chabwino, nchifukwa chiani ndiye chomwe ine ndimawatumiza iwo kumeneko? Kodi ine ndikanakhala wachinyengo kuti ndiziwatumiza ana anga omwe ku imfa? Izo zikhale kutali kwa ine. Ayi, bwana!

²¹⁵ Ngati inu simungathe kupita. . . Ngati inu simungathe kumabwera kuno ku kachisi, kapezeni mpingo wina

kwinakwake; zipitani kwa iwo. Inu simukusowa kuti mukachite kutengera zonse zimene iwo amachita. Gawo la mkate limene iwo akugawa, inu muzigawa mkatewo. Pamene iwo ali ndi galiki, potero, inu mungozisiya izo zokha. Mukuona? Ndiko kulondola. Ine sindingathe kuwapangitsa iwo kuti azikachita zimenezo, koma ndizo ndendende... Zedi, inu muzipita ku mpingo. Kulikonse kumene chitseko cha mpingo chatsegulidwa, inu muzinyamuka nkupita mwamphamvu momwe inu mungapitire. Ngati iwo samakhulupirira, chabwino... Tsopano, inu simukusowa kuti muzikachita nawo. Musati mukawajowine iwo, musati mukajowine uliwonse wa mipingo imeneyo; koma zipitani kwa iyo; zikayanjanani ndi iwo. Kodi inu mukudziwa bwanji kuti si Ambuye? Iye anati Iye azipangitsa chirichonse kumagwira ntchito palimodzi kwa ubwino! Ndipo mwinamwake kuli moyo kumeneko umene ukuyenera kuti upulumutsidwe, ndipo inu mungati mukaunikire Kuwala kwa iwo. Mukuona? Zipitanibe kumeneko. Musati muzipita mwamwano, zipitani mokoma; ndipo anthu akayamba kumati, “Ameneyo ndi mkazi wa Chikhristu chotero, ndi banja la Chikhristu; uyo ndi mnyamata kapena msungwana wa Chikhristu chotero. Mai, ine ndimakonda izo... Mnyamata, iwo akuchitadi ngati iwo ali ndi chinachake.” Mukuona? Ndi kuti, “Ndi chiani icho?”

“Ndi izi apa.” Ndiye awuze iwo. Koma kangokhalani amchere, ndipo iwowo azikakhala aludzu.

257. Wokonedwa M’bale Branham: Kodi inu mukukhulupirira kuti zizindikiro ziziwatsatira onse amene ali nao Mzimu Woyera?

Yesu ananena choncho, Marko 16.

Ngati ziri choncho, nanga bwanji anthu amene amakhulupirira Uthenga ndi zonse zimene ziri mkati mwawo, komabe iwo alibe zizindikiro izi? Kodi iwo ndi osakhulupirira kapena kodi iwo akusowa Mzimu Woyera? Ngati ziri choncho, chonde tilangizeni ife lero, momwe tingalandirire Mzimu Woyera. Ife tikukhulupirira inu ndinu kamwa ya Mulungu ya tsiku lathu. M’bale wanu.

²¹⁶ Zikomo inu, m’bale wanga, chifukwa chonditenga ine ngati wanu—m’bale wanu, ndipo ine ndikuganiza limenelo ndi funso labwino kwambiri. Abwenzi, inde, ilo ndi lochedwa pang’ono. Ine ndikanafuna kuti ndichite motalika pang’ono pa ilo ngati ine ndikanatha. Mukuona? Ilo lachedwa. Penyani! Ena a inu... Mukuona? Pamene—inu simungathe kulandira ubatizo wa Mzimu Woyera popanda kukhala ndi chokuchitikirani pamene izo zikuchitika... Tsopano, ngati inu mukukhulupirira “chidutswa chirichonse cha Mawu,” inu mukuti... Inu mukuti mumakhulupirira chidutswa chirichonse cha Iwo, ndiye Mawu ali chikhalireni pamenepo kuyembekezera Mzimu Woyera kuti

uwayike Iwo pogwira ntchito; koma izo zimatengera kuyatsa kwa kandulo.

²¹⁷ Apa pali kandulo ndi chingwe mwa iyo, ndipo ndi zonse—mafuta, ndi chirichonse chimene iyo ili nacho choti chikhale mu kandulo iyo; koma mpaka moto ubwere pa iyo, iyo siingawalitse kuwala kulikonse. Ziribe kanthu momwe kanduloyo iliri yangwiro, ndi momwe iyo ingayakire mwangwiro ndi chirichonse, iyo iyenera kuti iyatsidwe, ndiyeno iyo imayaka. Ndipo pamene inu mukhulupirira ndipo mwapangidwa ndi malangizo a chimene Mzimu Woyera uli, chikondi, chimwemwe, mtendere, kupirira motalika, ubwino—zipatso zimene Iwo umabalapo, mpaka Mzimu Woyera ndi chokuchitikirani choyaka tsikani ndi kudzayatsa kandulo imeneyo, ndiye inu—inu—inu simunawulandire Mzimu Woyera. Mukuona? Inu mukuyenera kukhala ndi chokuchitikirani kuti mukhale nao Mzimu Woyera.

258. Ndine wa mgwirizano wa apa ntchito. Kodi izi ndi zolakwika kwa Mkhristu? Mawu amati, “Musamalumbire—musamalumbire.” Ife timayenera kulumbira kuti tizisamalira chikhazikitso cha apa ntchito. Ine sindinatenge gawo lolimbikira kuyambira pamene ndinakhala Mkhristu, koma ine ndimalipira panobe zopereka zanga.

259. Kodi dzina la Yudasi Iskarioti linafufutidwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, kapena kodi ilo linali pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa?

²¹⁸ Chabwino. Zokhudza mgwirizano wa apa ntchito, ine ndikudziwa kuti inu ogwira ntchito...Anthu inu muli ndi migwirizano ya apa ntchito ndi zinthu zimene inu... Ngati iwe ukufuna kuti uzigwira ntchito, iwe umayenera kuti ukhale wa mu zimenezo. Ndiko kulondola ndendende. Iwe umayenera kuti uchite zimenezo. Koma samalani izo (mwaona?), chifukwa izo zidzachokera ku ntchitozo kufika ku chipembedzo limodzi la masiku amenewa. Mukuona? Tsopano, inu muzingomakumbukira, izo ndi zotsogolera kudza kwa chirichonse chodzakhala mwamgwirizano. Iwe sungathe kugwira ntchito; iwo sangakulole iwe kuti ukhale pa ntchito; iwe—ndiwe “wachabe,” kupatula iwe—kapatula iwe ukhale wa mu mgwirizano uwu.

²¹⁹ Tsopano kumbukirani, inu achinyamata, mudzakumbukire zimene M'bale Branham akunena. Ndipo mulole mawu anga azokotedwe ndi cholemba cha chitsulo p—p—pa phiri la chitsulo! PAKUTI ATERO AMBUYE, chinthu chomwecho chidzachitika mu chipembedzo. Inu mudzakhala a chipembedzo cha mtundu wina, kapena inu simungathe kugula kapena kugulitsa. Kotero khalani osamalitsa kwenikweni, M'bale. Siyani izo zizingothera pa za ntchito zokha. Samalirani izo; ilo ndi chenjezo!

220 “Kodi dzina la Yudasi Iskarioti linafufutidwa kuchokera mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, kapena kodi ilo linayamba lakhalapo pa Ilo?” Inde, ilo linali pa Ilo ndipo ilo linafutidwapo. Mukuona? Chifukwa mu Mateyu mutu wa 10, Yesu anamuitana Yudasi ndi onse a iwo, ndipo anawapatsa iwo mphamvu motsutsana ndi mizimu yosayera. Iwo anapita namakatulutsa ziwanda, ndipo Yesu anati, “Ine ndinamuwona ngakhale Satana akugwa kuchokera Kumwamba.” Uko ndi kulondola? Ndipo iwo anabwererako, ophunzira onsewo palimodzi, ndipo iwo anali akusangalala; ndipo Iye anati, “Musati muzisangalala k—kuti ziwanda zimakumverani inu, koma zisangalalani kuti dzina lanu linalembedwa pa Bukhu la Moyo.” Mukuona? Ndiko kulondola. Ndipo Yudasi anali kumene ndi iwo! Mukuona?

221 Kotero kumbukirani, pa chiweruzo, penyani, pa mpando wa chiweruzo, “Chiweruzo chinakhazikitsidwa; mabuku anatssegulidwa; ndipo Bukhu lina linatsegulidwa, limene linali Bukhu la Moyo, ndipo munthu aliyense anaweruzidwa chomwecho.”

222 Tsopano, ndi inu apo, kwa funso la kanthawi kapitako. Mukuona? Pa mpando wa chiweruzo. Yesu, Mpingo, Mkwatibwi, anakwatulidwa, anapita mmwamba ku Ulemerero, ndipo anali kumwamba uko ndipo anakwatiwa, anadzabwereranso pa dziko lapansi, ndipo anadzakhala zaka chikwi. Pa kutha kwa zaka chikwi Satana anamasulidwa ku ndende yake, kumene anamangidwa ndi Mngelo ndi unyolo, osati unyolo wachipika, koma unyolo wa zochitika; omumvera ake onse anali mu hade. Onse amene anaukitsidwa pa dziko lapansi anawomboledwa ndi Yesu limodzi nawo. Iye sakanatha kugwira ntchito pa chirichonse; koma pa mapeto a zaka chikwi, chiukitsiro chachiwiri... “Wodala ndi woyera ali iye amene ali nalo gawo mu chiukitsiro choyamba pa omwe imfa yachiwiri ilibe mphamvu.”

223 Tsopano zindikirani, mu chiukitsiro chachiwiri ichi, pamene iwo akubwera apo, ndiye Satana akumasulidwa kuchokera mu ndende yake kwa kanyengo kakang’ono; ndiye chiweruzo chikuyambika. Tsopano penyani, Yesu ndi Mkwatibwi, monga Mfumu ndi Mfumukazi, atakhala pa mpando wachifumu, Mpandowachifumu Woyera wa chiweruzo; ndipo mabuku anatssegulidwa, mabuku a ochimwa. Ndipo Bukhu lina linatsegulidwa, limene linali Bukhu la Moyo; ndipo munthu aliyense anaweruzidwa chomwecho ndi Mkwatibwi. “Kodi inu simukudziwa (pakutengera nkhani zazing’ono izi pamaso pa alamulo)—kodi inu simukudziwa kuti oyer adzaweruzo dziko lapansi?” Mwaona, mwaona? Chabwino.

260. Kodi chonde inu mungafotokoze omwe gulu la Chivumbulutsu 20:4 ali? Kodi iwo ali gawo la Mkwatibwi wakale kapena mtsogolo?

²²⁴ Iwo ndiwo Mkwatibwi kwathunthu, onse wakale ndi atsopano. Iwo ndiwo Mkwatibwi kwathunthu, chifukwa iwo akukhala mu Zakachikwi. Chabwino.

261. Kodi chonde inu mungafotokoze (Chabwino, ndi ndendende funso lomwelo.)...Chivumbulutso 20:4, kodi iwo ali miyoyo ya odulidwa mitu chifukwa cha umboni wa Khristu amene sanalambire chirombo ngakhale kulandira chilemba chake mu (O, ine ndikuwona kumene iwo akupita tsopano. Ili langopatsidwa kumene kwa ine, langoperekedwa kumene kwa ine)...pakuti akuti anakhala moyo ndipo ankalamulira limodzi ndi Khristu kwa zaka chikwi? Kotero izo ndi zododometsa, chifukwa cha kuzunzidwa kwa Mkwatibwi, koma kodi iwo angakhaleenso ndani ndi kumalamulira ndi Khristu zaka chikwi? Kodi i—i—kodi iwo angakhale 144,000?

Ayi, ayi! Iwo ndiwo Mkwatibwi. Tsopano, kumbukirani, kumbukiranai, iwo...

²²⁵ Inu munati, “Pamene iwo akudulidwa mitu chifukwa cha umboni...” Tsopano, inu mukuti, “Pakuti—sali kulambira chirombo...” Zedi! Inu mukuti, “Chirombo ndi choti chidzabwerabe.”

²²⁶ Chirombo chakhala chiripo nthawi yonse; chirombo chinali chimene chinkawadyetsa iwo ku makola a mikango aja, chikawadyetsanso iwo mmbuyo umu mu mabwalo uko mu Roma. Ameneyo anali wotsutsakhristu; icho chinali chirombo uko komwe, anayambitsa mawonekedwe a chipembedzo. Ndendende basi monga—pafupifupi ndondomekoyo. Mpingo wa Roma unatengedwa kuchokera mu Baibulo, ndiyeno... Chimene iwo anachita pa izo, iwo anapanga bungwe chinthucho ndipo anapanga chikhazikitso ndipo anapanga—mpingo wa konsekonse kuchokera mu zimenezo, ndipo onse amene samagwadira kwa izo anayenera kuti aziwonongedwa. Mukuona? Izo zinali.

²²⁷ Ndipo iwo a mu gawo la Thupi amene linali apo... Tsopano, Thupi lakula chimodzimidzi monga mtengo mpaka Izo zikubwera ku Mutu. Mukuona? Ndipo onse, onse ofera, ndi ozunzidwa, ndi ena otero...

²²⁸ Koma Yesu watipatsa ife mtendere mbali ino ya mtsinje, monga momwe Iye anachitira kwa mafuko amene...uko (mukuona?) sanawolokere kwinko. Tsopano.

262. Kodi ine ndiwachitire chiani iwo? Kodi ine ndipitirize (O!) kuwasamalira Adadi ku munda? Kodi ine ndichite chiani...kuti akhale—nazo moyo...? Ndipo walembapo dzina lake.

Inde, m'bale wanga...Izo—walemba apa. Ine sindikudziwa kuti ndi ndani...Ilo likuti, “M'bale Branham...” Ilo likungoyamba ndi, “Kodi ine ndiwachitire chiani iwo?”

²²⁹ Tsopano, mwinamwake mnyamata wina kwa abambo ake. Penya, M'bale wanga wokondedwa, wodala uli iwe pamene iwe ukuwasamalira abambo ako, chifukwa abambo ako anakusamalira iwe pamene iwe sunkatha kudzisamalira wekha. Ndipo lamulo loyamba lokhala ndi lonjezo, lamulo loyamba lokhala ndi lonjezo: “Lemekezeza abambo ako ndi amai ako chimene chingatalikitse masiku pa dziko lapansi amene Ambuye Mulungu wako anakupatsa iwe.” Mukuona? Eya, zivasamalira abambo ako mwanjira iliyonse yomwe iwe ungather. Uziwona kuti iwo akulandira zopambana kwambiri.

263. Inu munanena kuti Kaini anali wa mbewu ya serpenti. Nchifukwa chiani Eva anati, “Ine ndalandira munthu kuchokera kwa Ambuye”?

Tiyeni nazoni. Ine kulibwino ndidikire mpaka chakudya pa ili. Eya, ine ndiyembekezera mpaka chakudya pa ilo. O, izo zingatenge pafupi kanthawi pang'ono kuti ndifotokoze zimenezo. Chabwino.

264. Wokondedwa M'bale Branham: Kodi inu mungafotokoze ndime iyi kwa ine, Yesaya 2:2: “Ndipo kudzachitika kuti mu masiku otsiriza, kuti phiri la Ambuye—pa phiri la Ambuye nyumba idzakhazikitsidwa pamwamba pa mapiri, ndipo idzakwezedwa pamwamba pa mapiri; ndipo mafuko onse adzakhamakira ku iyo.”

²³⁰ Inde, ine ndinatero, Lamlungu lisanafike lathali. Mukuona? N—nyumba ya Ambuye idzakhazikitsidwa pamwamba pa mapiri, ndipo mafuko onse azidzakhamakira kwa iyo. Lalikulu... Ngati inu mulibe... Ngati inu muli nayo tepi ya *Kwawo Kwa Mtsogolo Kwa Mkwatibwi ndi Mkwati*, iyo ikufotokoza izo ndendende basi mwanjira imeneyo.

O, mai! Ine mwina ndibwino ndingolekeza pakali pano, chifukwa mai, o, mai, m'bale, ife sitingate kutsiriza zonse izi apa. Fyuu!

265. M'bale Branham, ndi... (Tiyeni tiwone chomwe ili liri.) M'bale Branham, zikukhulupiriridwa mwawamba ndi ambiri amene akutsatira Uthenga wanu kuti inu ndinu Mesiya wa tsiku lino. Kodi izo ziri choncho?

²³¹ Ayi, bwana!

Mwapoyera tatiuzani ife, M'bale Branham. Inu mukuwoneka ngati mukudodoma pozidziwitsa nokha, ndipo ife tikudziwa kuti ndi utumiki woterewu wonga womwe Mulungu wakupatsani inu, inu mukuyenera kuzindikiritsidwa mu Malemba penapake.

266. Lachiwiri: Inu munatiuza ife cholinga chanu chopitira ku Arizona nthawi yoyamba. Inu munatiuza ife chifukwa chake, ndipo izo zinafika pochitika, koma inu simunatiuza ife chifukwa chimene inu munabwererakonso kachiwiri.

²³² Malo oyamba, ine sindine Mesiya! Mukuona? *Mesiya* ndi Yesu Khristu, koma ife ndi “Tiamesiya,” mmodzi aliyense wa ife. *Mesiya, Mesiya* amatanthauza “Wodzozedwayo.” Ndipo mwa Iye munkakhala chidzalo cha Umulungu mwathupi; mwa ine mukukhala gawo la Mzimu Wake, womwewo umene umakhala mwa inu. Ine ndinapatsidwa mphatso k—kuti—ndizidziwa zinthu zazing’ono ndi kuwoneratu zinthu. Izo zikundipanga ine kukhalabe m’bale wanu. Mukuona? Ine sindiri—Mesiya ayi; ine ndine m’bale wanu (mukuona?), m’busa basi kwa gulu. Ndipo ngati ine ndikanakuuzani inu kuti ine ndinali Mesiya, ine ndikanakhala wabodza. Mukuona? Ndipo ine sindikufuna kuti ndikhale wabodza.

²³³ “Tsopano, nchifukwa chiani ine ndinapita ku Arizona nthawi yoyamba?” Inu munamvetsa zimenezo. Ine ndinapita mu Dzina la Ambuye, chifukwa ine ndinatumidwa kumeneko mwa masomphenya. Ine ndinabwereranso nthawi yachiwiri pa cholinga. Ingozisiyani izo zokha. Ine ndikudziwa chimene ine ndinapitira uko; ine sindingathe kumakuuzani chirichonse. Pamene iwe—mdierekezi sakudziwa—sangathe kuzitenga izo kuchokera mu mtima wanga. Ngati ine ndiziyankhula izo nkuzitulutsa, ndiye iye akhoza kuzitenga izo, koma iye sa—iye sangathe kuzitenga izo pamene izo ziri mu mtima wanga. Ngati ine ndinganene, “Dikirani mpaka izo zifike pochitika!”... Ingokumbukirani, gwirani tepi iyi; ine ndinapita ku Arizona pa cholinga. Chonde pirirani nane. Mukuona? Inu muzingochita zimene ine ndikukuuzani inu kuti muzichita (mukuona?); basi—kuchita momwe ine ndikunenera kuti muzichita. Mukuona?

267. M’bale Branham, ine ndiri ndi mafunso ena amene ine ndikukhumba kuti ndifunse—ndikufunsemi inu. Ine ndawamva anthu akunena kuti inu mwawalangiza anthu kuti agulitse zawo zonse. . . (Mwinamwake ine ndilisiye ilo lokha nalonso. Tiyeni tiwone. Chabwino, ndi nthawi kale yoti tizipita. Ife mwinamwake tidzalitenga ili pambuyo pa chakudya, koma i—ine ndidzaliyankha ili kapena ndidzayesera mwakukhoza kwanga. Ine sindikudziwa; ilo langoperekedwa kumene kwa ine. Mukuona? Billy anandibweretsera ine odzaza mdzanja apo pomwe—apo pa khomo. Mukuona?) Ine ndawamva anthu akunena kuti inu mwawalangiza anthu kuti agulitse nyumba zawo zonse ndi kuti akutsatireni inu ku Arizona k—kapena iwo sadzakhala ali mu mkwatulo. Kodi izo ndi zoonza?

²³⁴ Limenelo ndi bodza. Mukuona? U-nhu!

. . . kapena kodi ife tigulitse manyumba athu, kapena kodi inu munazinena konse izi?

²³⁵ Ayi, bwana! Ine sindinazinene zimenezo! Ngati chirichonse, ine ndawalangiza anthu kuti asachite zimenezo. U-nhu! Kukumbukira, mukukumbukira loto la “Junie” Jackson nthawi

ija pamene ine ndinapita kumeneko? “Junie” analota kuti iye anaziwona izi...Ndi angati akukumbukira lotolo, ndi momwe Ambuye anaperekera kutanthauzira. Phiri lalikulu lija, ife tinali titaima pa ilo, ndi zilembo zakale zofufutika pamenepo; ndipo ine ndinali kuyesera kuti ndizitanthauzire izo, ndipo ine sindinali kutha kuchita izo. Ndipo i—ine ndinali kuzitanthauzira izo kwa iwo. Nditatha kutanthauzira zonsezo, zonsezo zitanthauziridwa, ndiye ine ndinafikira pamwamba ndipo ndinatenga (mu loto lake tsopano) mtundu wina wa—chokhala ngati chitsulo ndipo ndinangodula pamwamba pa phirilo ndipo ndinayang’ana mkati umo, ndipo umo monse munali moyera-mwachipale, monga nsangalabwi. Koma umo munali mosalembedwa, ndipo ine ndinati, “Inu nonse mukhale kuno ndi kumayang’ana umu pa izi tsopano, pamene ine ndikupita kutali.”

²³⁶ Ndipo “Junie”...Onse awo anapita pamwambapo ndipo abale onse ndi onse akuyang’ana pa iwo, wina...Iwo sankatha kuzimvetsa; anati, “Chabwino, kodi inu mukudziwa chiani? Izo sizinalembedwe nkomwe apa,” komabe iye anali akuwerenga kunja kwake kwa izo. “Chifukwa chiani izo sizinalembedwe mkati umu? Ife sitikutha kuzimvetsa.”

²³⁷ Ndipo Junior anapotoloka pamenepo ndipo anayang’ana, ndipo iye anandiwona ine ndikupita cha kumadzulo, ndi kupita cha kolowera dzuwa, kupita pamwamba pa phiri limodzi, phiri lina, mofulumira kwenikweni, kumangopita...Ndiyeno iwo anapotoloka nayang’ana ndipo anandiwona ine nditapita; gulu lalikulu lonse la iwo linachoka napita chaku njira imeneyo, ndipo iwo ankafuna kupita *uku* ndi kukachita *izo*, nditawauza ine kale kuti akhale pamenepo. Akhale pamenepo, akhale pomwe pano; malo ake ndi anowa.

²³⁸ Ndiyeno, pamene ine ndinachita izo, ndiye—ndipo ine ndinapita ndendende basi; ndipo pang’ono pokha zitachitika izo, Mngelo wa Ambuye anawonekera kwa ine, nkuti, “Pita uko ku Arizona kutaliko.” Ine ndinamva kuphulika kuja kukuchitika ndipo ndinapita kumeneko, ndipo kodi chinali chiani icho? Mnyamata uyo analota loto limenelo molondola ndendende basi, ndipo Ambuye anapereka ufulu...Kumbukirani, ine ndinati, “Pali chinachake chimene ine ndikupitira kumeneko.” Ndipo pamene ine ndinapita uko, icho chinali chinsinsi cha Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri, zimene zinasindikizidwa umo mkati mwa phiri lija la Ambuye. Ndinabwerera kuno komwe ndi kutsegula kwa Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri. Mukuona?

²³⁹ Ayi, inu musati muzichita zimenezo. Ngati inu mukufuna kuti mupiteko, zimenezo ziri kwa inu. Chifukwa, ine sindiri... Mai, ine sindikusamala komwe inu mupita, koma kuti mungochita zimenezo, mukuganiza kuti Mkwatibwi adzapita kuchokera kumeneko, inu mukulakwitsa.

240 “Komanso ine ndamva izi...Ine ndiri (Ndirole i...Ine ndazitenga izo molakwika penapake apa. Tiyeni tiwone)... mkwatulo. Kodi izi ndi zoon kapena kodi ife tigulitse manyumba athu, kapena kodi inu munayamba mwanenapo izi?” Ayi, ine sindinanene konse zimenezo. Ine sindina...Ine nthawizonse ndawalangiza anthu kuti muzikhala kumene inu muli ndi kumapitiriza pitirizabe mpaka Yesu abwere. Ngati ine ndakuuzani inu nthawi zambiri, mulole tepi iyi ikhale chikumbutso; mulole tsiku lino likhale chikumbutso; mulole mawu anga akhale chikumbutso; ine sindinayambe, pa nthawi imodzi, kumuuzapo konse aliyense, kubapo konse anthu, kuyesera konse kuti ndimutenge winawake kuti azibwera ku mpingo uno! Ine sindinachitepo...Kufika pa kuwauza iwo kuti asiye mipingo yawo yomwe ndi kugulitsa katundu wawo ndi zinthu, Mulungu akudziwa kuti ine nthawizonse ndimawalangiza anthu kuti akhalebe ali Akhristu ndi kumakhala kumene inu muli mpaka Mulungu adzakuitaneni inu. Aliyense akudziwa zimenezo. Khalani uko komwe! Koma tsopano, kuti ndiwauze anthu...Winawake akati, “Chabwino, ine ndikufuna kuti ndipite cha uku. Ine ndikufuna kuti ndizikakhala...” Inu pitani kulikonse kumene inu mukufuna kuti mupiteko; izo zonse ziri bwino. Ine sindikusamala kumene inu muti mupite; imeneyo si ntchito yanga pa izo.

241 Koma tsopano, kuti muziganiza kuti...Onani, kodi icho chimachita chiani? Izo zimayambitsa kachiphunzitsa kotsatira munthu (mukuona?), ndiyeno ine ndilowa mu vuto. Iwo ali ndi gulu kunja uko pakali pano limene liti likhale pa chithandizo posakhali tsapa. Ndiyeno kodi izo zidzakhala chiani? “Ife tadzera kuno pofuna mkwatulo wa Mkwatibwi.” Izo ndi basi zimene manyuzipepala akuziyembekezera! Iwo akuyembekezera kuti atenge zimenezo pamene iwo ati agwere poti azithandizidwa ndipo sangathe kubwerera ku makwawo. Ndiye kodi iwo adzachita chiani?

242 “Chabwino, ife tamutsatira M'bale Branham kuno. Amayenera kuti akhale...” Ndipo ine ndiri wosalakwa basi pa izo momwe ine ndingathe kukhalira ndiri. Anthu okondeka, okoma, i—iwo akudziwa kuti ine ndimawakonda iwo, ndipo ngakhale mu kulakwitsa kwawo. Ndipo iwo...Bwanji, a...Iwo...ine ndikuwakonda iwo mulimonsebe. Mukuona? Ine ndikuwakonda iwo; iwo ndi ana anga; koma basi iwo sakundimvera ine, chimene ine ndikuyesera kuti ndiwauze iwo. Ine ndikuyesera kuti ndichititse chinachake mu Dzina la Ambuye, ndipo iwo sakundilola ine kuti ndichichite icho. Mwaona? Iwo mwakuchita akupita motsutsana ndi ine mmalo mokhala ndi ine. Iwo akuchita...

243 Kodi ine sindinakuuzeni inu kuti ngati konse uthenga ungtati ulalikidwe, kwa kudzakhala kuli komwe kuno pa kachisi uyu; chirichonse chimene ine ndikanati ndichichite,

ine ndikanamabwera kuno ndi kudzakuuzani inu poyamba, molunjika kumene kuchokera pa kachisi uno? Ilo ndi lonjezo langa!

268. Ndiponso, ine ndamva kuti pali chiphunzitso chatuluka, kuti bukhu limene inu munalilemba zaka zingapo zapitazo lokamba za mkate wa moyo. . . Iwo akutanthauzira izo kuti ife tonse tizikhala ndi inu kapena tiuphonya mkwatulo.

²⁴⁴ Chabwino, bukhulo liri kulakwa. Bukhu la *Mkate wa Moyo*, ine ndikulikumbukira ilo tsopano. Uko kunali kudyetsa mpingo konsekonse, kulikonse. Mwaona, vuto lake liri. . . Tsopano, tsopano, anthu inu, inu ndi olimba inueni, koma iwe umayenera kukhala nazo izo. Izo zimatsatira msonkhano uliwonse. A—a. . .

Ine ndinali kuwerenga za Marteni Lutera kuno osati kale litali, si kudzifanizitsa tokha ndi izo; koma uku ndi kukonzanso chimodzimodzi monga uko kunali. Ndipo—funso linali. . . A—azambiriyakale, iwo anati, “Ndi chinthu chopambana kuganiza kuti Marteni Lutera akanatha kuwutsutsa mpingo wa Katolika ndi kudutsa nazo izo. Icho chinali chinthu chodabwitsa, koma,” anati, “chinthu chodabwitsa kwambiri cha Marteni Lutera sichinali chimenecho. Momwe iye akanathera kuugwira mutu wake pamwamba pa kutengeka konse kumene kunkatsatira msonkhano wake ndi kukhalabe woona kwa Mawu, kuitanidwa kwake. . .” Mukuona?

²⁴⁵ Ayi, bwana! Musati muziika zanzanu. . . Mwamuna aliyense kapena mkazi amene angaike chirichonse ku chimene ine ndikunena, Sali kukhulupirira zimene ine ndikunena. Iwo sali. . . Iwo akuti. . . Iwo. . .

269. Ndiponso za mabanja awa amene agulitsa zonse ndipo asamukira ku Sierra Vista, Arizona, kumene iwo atanthauzira kuchokera mu imodzi ya matepi anu yotchedwa (miniti chabe) “Betelehemu Wamng’ono”—“Betelehemu Wamng’ono,” mkwatulo udzakachitikira mu Arizona. Kodi inu munawalangiza iwo kuti apite kumeneko?

²⁴⁶ Ine ndithudi sindinatero. Pamene iwo analemba kalata ya zimenezo, winawake kuno mu Connecticut kapena chinachake, ine ndinayankha kalatayo mobwezera ndipo ndinati, “Inu mukupanga kusuntha koipa kumene inu munayamba mwakupangapo mu moyo wanu. Musati muzichita zinthu monga zimenezo.” Mwaona, inu simungathe. . . Chabwino, inu musingokumbukira, anthu inu. . . Tsopano, inu nonse mukudziwa kuti ine sindikuwauza anthu amenewo kuti azichita zimenezo; ine ndikuwauza iwo kuti asachite zimenezo. Koma inu mukuona, izo zikuyenera kutsatira msonkhano. Nchifukwa chiani anthu amanditcha ine *Mesiya*? Nchifukwa chiani anthu. . .? Iwo ali ndi kutenga. . . Chabwino, munthu wina kunja uko anandiwonetsa ine tsiku lina, iye anali ndi kanthu

kakang'ono ndipo iye anali kupita—amapitiriza, ankafuna kuti anthu onse azibatizidwa mu dzina langa. Izo zingandipange ine kukhala wotsutsakhristu! Koma ine sindine wofuna zinthu zimenezo, ndipo anthu nonse inu mukudziwa zimenezo. Koma inu mukuona, izi ziyenera... Izo zikungouzindikiritsa kuti Uthengawu ndi woona.

²⁴⁷ Kodi iwo sanabwere ndi kudzayesa kumuuza Yohane, a—amene anatsogolera kudza koyamba kwa Khristu, “Kodi inu sindinu Mesiya?”

Iye anati, “Ine sindiri! Ine sindine ngakhale woyenera kumasula nsapato Zake. Ine sindiri woyenera ngakhale kuti ndiyang'ane pa Iye.” Mukuona? Koma iye anati, “Iye amene akudza pambuyo panga...”

270. Tsopano, M'bale Branham, kodi ife tikuphonya pa chinachake? Anthu awa akudzinenera kuti akukhulupirira mawu aliwone amene inu mukuwanena kuti ndi owona. (Koma iwo sali! Iwo sali kukhulupirira izo. Zochita zawo zomwe zikutsimikizira kuti iwo sali.) Chonde ndiroleni ine ndidziwe yankho lanu lolunjika: inde kapena ayi (Inu mwalipeza ilo! Chabwino.) za zinthu izi, ndipo ngati izo ziri zoona, ife tikufuna tikonzekere kuti tikalumikizane nawo ena onse a iwo kumeneko—onse a iwo. Ine ndikukuthokozani inu mochuluka kwambiri chifukwa cha mayankho anu ku mafunso awa, pamene ine ndikhala ndikuyembekezera kuti ndiwamwe iwo Lamlungu ili, ngati Ambuye achedwa.

²⁴⁸ O, mai! Chabwino, M'bale, Mlongo, i—ine ndikuyembekeza izo zamveka (mukuona?) kuti ine sindinatero, sindikutero... Tsopano, ngati anthu... O, zedi, ngati inu mukufuna kuti mubwere uko ku Arizona kumadzakhalako... Ndipo tsopano, ine ndidzakhala ndiri uko ku Arizona mwinamwake gawo loyamba ili. Ine ndidzayenera kuti ndidzabwererense kuno. Ine ndidzayenera... I—ine ndikufuna ndikakhale kumeneko; ana ali athanziko ndi chirichonse. I—ine ndikufuna ndikakhale kumeneko kanthawi pang'ono, ndipo ine ndiri ndi cholinga. Kumbukirani tsopano, pa tepi, PAKUTI ATERO AMBUYE, ine ndiri ndi cholinga pochita zimene ine ndikuchitazi; inu mukudziwa ine ndiri nacho; koma ine sindingathe kukuuzani inu zimenezo.

²⁴⁹ Nchifukwa chiani ine ndikukuuzani inu kuti musagulitse manyumba anu? Inu mudzakhala mukusowa, ndipo inu mudzakhala muli ku mathero aafupi a chingwe. Musati muchite zimenezo. Ine sindikakhala ku Arizona koma kanthawi pang'ono kokha. Bwanji? Ine sindingathe kuchita izo tsopano.

²⁵⁰ Ngati ine ndiwalola anthu amenewo kuti azikakhala kumeneko ndi kumapitirira pa chithandizo, nchiani chiti chidzachitike? Ndiye, izo ndizo ndendende basi zomwe

zipembedzo ndi onse a iwo akuyembekezera. “Aha, ine ndinakuuzani inu zomwe zinali kumbuyo kwa iye, sukulu ina ya aneneri kapena chinachake!” Mukuona? Ndi zimenezotu, izo ndi basi zimene iwo akuziyembekezera! Pambuyo pa zonsezo, anthu amenewo, ine ndiri ndi chowayankhira pa iwo; ngakhale iwo sanachite zimene ine ndinawauza iwo kuti achite, ndipo iwo achita ndendende. . . Inu mukuti, “Asiyeni iwo apite; i—iwo achita zimene inu munawauza iwo kuti asachite!” Zimenezo siziri mu mtima wanga. Ine ndikufunabe kuti ndipite kukawafuna iwo. Iwo ndi ana anga. Ine ndikhoza kudzawapatsa iwo kakhofi pang’ono pamene ine ndidzawabwezeke iwo, koma i—koma i—ine ndithudi ndipita mowatsatira iwo. Ndipo kodi ine ndikachita motani kumeneko?

251 Iwo anati, “Ife tabwera kudzatsatira Mawu.” Ine ndiribe ngakhale mpingo woti ndiziwatumizako iwo kumeneko. Mtundu wa mpingo komwe iwo azikapitako uko ndi mtundu womwewo umene inu mumawusiya ku malo ena, mwinanso moyipirapo. Mukuona? Ndipo iwo samapita ku mpingo mulimonse, ndipo ine ndiribe mpingo woti ndizikawalalikirako iwo. Ndiye ine ndiri wokakamizidwa mwamakhalidwe kuti ndiwachotseko ana anga ku Arizonako, kumene. . .

252 Ine ndikufunsemi inu chinachake. Ine ndalalikirapo kupitirira mauthenga sate mu mpingo uno chaka chathachi. Ndipo kwa zaka zisanu, nditachoka, kuyambira pamene ine ndakhala ndiri mu Arizona, ine ndalalikira ochuluka mu mpingo uno mu chaka chimodzi kuposa momwe ine ndinachitirapo mu zaka zisanu nthawi ina iliyonse (ndithudi!), muno mu mpingo. Kuno ndiye ku maziko a kwathu; kuno ndi ku likulu langa; kuno ndi kumene ife takhazikikako. Tsopano, gwirani izo mu malingaliro palibe kanthu chomwe chiti chichitike. Tsopano, ngati inu muli amzeru, inu mugwira chinachake. Ziribe kanthu chomwe chichitike, kuno ndi kulikulu kwathu, kuno komwe! Ndipo sungani zimenezo mu malingaliro ndipo mudzalozere mmbuyo ku tepi iyi tsiku lina, kuti inu munandimva ine ndikunenera. Chabwino, zikumbukirani zimenezo!

253 Ngati inu mukufuna—ngati inu mukuyenera kuchoka ndi kumabwera ku mpingo, musati mupite uko kuti mukaupenze iwo, chifukwa ine sindiri ngakhale kumeneko. Ine ndiribe malo oti ndizipitako; ine ndiribe malo oti ndizikalalikirako. Iwo sangandilole ine kuti ndizikalalikirira mu mipingo yawo. Ine ndiribe ngakhale malo, ndipo ine ndinamulonjeza bamboyo pamene ine ndinafika uko. . . Iwo onse ankachita mantha kuti ine ndimabwera kumeneko ndi kudzamanga chinyumba chachikulu—nkuchotsa anthu mu mipingo. Koma chimenecho si cholinga changa cha moyo. Mukuona? I—ine ndimawafikitsa anthu populumutsidwa. Izo ziri kwa iwo. Monga Msamariya anabwera uko ndipo anamutengera bambo uja ku nyumba ya alendo, ndiye nkuwasiya iwo kuti aziwasamalira iwo kuchokera

pamenepo mpakana. Ine sindiri kuno kuti ndidzaphwasule mipingo, ine ndiri kuno kuti nditengere otembenuka kwa Khristu! Mukuona? Ndipo izo zimandipangitsa ine kukhala wosamvetsedwa pakati pa anthu (mukuona?) p—pamene iwo akutanthauzira mwanjira yawo yawo ndipo osati—ndi—kunena zimene ine ndiri kunena. Mukuona?

254 Kodi inu simukukumbukira masomphenya aja? Ndi angati akukumbukira loto la Junior Jackson? Ndipo onse a iwo akutsatira izo ndendende basi. Kodi chinali chiani icho? Khalani kuno mpaka ine ndipite kutaliko! Mukuona? Ndi kukatenga kutanthauzirako ndi kukabwererako.

255 Tsopano, ine ndiri ndi chinachakenso mu mtima wanga chimene ine ndachenjezedwa ndi Ambuye kuti ndichichite, kusuntha kwina koti ndikupange kokhudza za kachisi uyu, ndi tchalitchi ichi; kuti ine ndiyenera ndipite uko kapena kwinakwake kwa kanthawi pang'ono. Izo ndi za kwa cholinga, cholinga chachikulu, cholinga chimene inu simukudziwa kanthu ka icho. Koma kumbukirani, ine sikuti “ndikungoyenda” mozungulira, chifukwa ine ndikuchita ngati ine ndiridi. Ine ndikugwira ntchito mu chifuniro cha Ambuye, utali wonsewu momwe ine ndikudziwira kugwira kwake ntchito mu zimenezo. Mukuona? Ndicho chifukwa chake ngati inu mukukhulupirira zimene ine ndikunena, ndiye inu zichitani zimene ine ndikunena kuti muzichita (mukuona?), ndiye mvetserani kwa ine ndi kundikhulupirira ine monga m'bale wanu. Ngati inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri, musati muzitanthauzira molakwika mawu anga!

256 Ngati pali chirichonse, kotero ndithandizeni ine, ngati pali chirichonse chimene inu mukuyenera kuti muchidziwe chimene Mulungu angandiuze ine, Mulungu akudziwa ine ndikanati ndikuuzeni inu ndendende basi! Ndipo musati muziwonjezera kwa izo kapena kuchotsa kwa izo; inu muzingochita izo mwanjira yomwe ine ndikuzinenera izo (mukuona?), chifukwa ine ndikukuuzani inu kuchokera mu mtima wanga mwakupambana kumene ine ndikudziwira. Mukuona? Inu muzingokhulupirira zimenezo. Basi—muzitenga ba—basi zimene ine ndikunena pa izo, ndi kungozisiya izo kuti zipite monga choncho. Chabwino.

257 Kotero tsopano, ine ndiyenera ndikawabweretse ana amenewo mobwerera kuno kuti azidzadya chinachake. Iwo ali uko mu chipululu akufa ndi njala.

258 Mtumiki anabwera kwa ine tsiku lina, anati, “M'bale Branham, iwo akulowa mu kachiphunzitso kotsatira munthu koipitsitsa kumusi uko kamene inu munayamba mwakawonapo.” Anati, “Aliyense wa iwo, mmawa uliwonse, iwo amatuluka; ndipo iwo amati sapita kukagwira ntchito, tayandikira kwambiri ku mkwatulo.” Iwo sapita kukagwira

ntchito. Chabwino, izo zikungosonyeza kuti inu simukumvetsa nkomwe. Mukuona? Kulondola. (Tepi iyi ikupita kumeneko!) Kotero, inde, bwana! Inu muyenera kutenga phunziro kuchokera kwa chiswe, Baibulo limatero, inu mukudziwa. Ngati icho sichingagwire ntchito, icho sichingadye. Kotero izo ziri ndendende basi zolondola.

P—pano, ndangotola imodzi ya izi.

271. Ziri . . . (Ine sindikudziwa. Mwaona, izi ndi zina basi—ndi zosiyana—ndi kulemba kwa dzanja losiyana ndi zinazi. Basi kuti ndikusonyezeni inu, ine ndikuganiza pali pafupi eyiti kapena teni a awa mmenemo. Mukuona?) K—kodi mpingo wangwiro kwambiri udzakakhala uli ku Tucson, Arizona? Ine ndikufuna kukhala mu chifuniro changwiro cha Mulungu. Kodi ife tisamukire ku Tucson?

²⁵⁹ Si linanso konse—kulemba kwa dzanja lina. Ziri . . . ine . . . Kungoyang’ana mozungulira pano; ine ndingakusonyezeni inu angati amene alipo pa funso limodzi limenelo. Ine sindi . . . I—ine sindikanatha kuwapeza iwo, ine ndikuganiza. P—pano . . . ine ndiri nawo ena ndawalemba chizindikiro apa, “Ine ndikudziwitsani inu.”

272. M’bale Branham: Chonde . . . (Tiyeni tiwone.) Podziwa kuti inu ndinu mneneri, ndipo ora limene ife tiri kukhalamo, lidza—ndipo mneneri wa ora limene ife tiri kukhalamoli (Ndicho chimene izo ziri.), kodi kudzafika nthawi pamene anthu a Mulungu adzayenera kuti athawire ku Arizona limodzi ndi inu? Ngati ziri choncho, kodi inu mudzatidziwitsa ife pamene nthawiyo idzafika?

²⁶⁰ Zedi ndidzatero. Ine ndidzakuuzani inu. Ine ndidzakuuzani inu. Tsopano onani, pali malembedwe a manja awiri osiyana, anthu awiri osiyana. Mukuona? Apo pali malembedwe a dzanja limodzi, ndipo apo pali enanso. Mukuona? Izo ndi zimene zikuyenera kukhala, zimene ziri mu malingaliro a mpingo. Mukuona? Chabwino, tiyeni tingozitengera izi pokhazikitsidwa. Tiyeni tiwone ngati ine ndikanatha kupeza . . . Tiyeni tiwone.

273. M’bale Branham . . . (Pali limodzi lina, losiyana lonse kwathunthu.) M’bale Branham, ena anakumvetsani inu kuti mumanena mu uthenga wanu wa “Kwawo kwa Mtsogolo kwa Mkwatibwi ndi Mkwati” kunali koti kudzakhala (Ayi, ili ndi losiyana.)—idzakhala mailosi fiftini handiredi kuchokera pa kachisiyu—mwamphwamphwa—seveni handiredi mbali iliyonse (Mwakuyakhula kwina, kachisi kukhala ali pakati penipeni nkukhala seveni handiredi mbali iliyonse—zidzakhala mailosi fiftini handiredi.O!)—mbali iliyonse. Kodi izi ndi zoono? Ine ndikukhala kunjwa kwa dera ili; kodi ine ndisamukire mmenemo?

261 Ayi, Wokonedwa, inu musati muchite zimenezo. Penyani! Tsopano, inu mukuona kuphweka kwake momwe ziriri kwa anthu? Ndi angati anali kuno pamene ine ndinkalalikira uthenga umenewo? Ine ndinanena kuti pamene ine ndinkayeza Yerusalemu Watsopano, kuti iwo udzakhala uli wamphwamphwa mailosi fifitini handiredi. Ine ndinanena kuti iwo uzidzafikira pafupifupi kuchokera ku Maine mpaka ku Florida, ndi mailosi sikisi handiredi kumadzulo kwa Mississippi; izo zikanakhala mwamphwamphwa mailosi fifitini handiredi. Ine ndinati Mzindawo, mwa kulingalira kwanga, udzakhala uli pa malo pomwepo pamene mneneri Abrahamu ankawufunafuna Mzinda umenewo, kumene sikudzakhala kulinso nyanja. Baibulo linati sikudzakhala kulinso nyanja, chimene chiri pafupi magawo atatu pa anayi a dziko lapansi liri madzi. Ndipo uko sikudzakhala kulinso nyanja; kotero, iwo sungati ukhale uli Mzinda wawukulu kwambiri utakhala mu malo monga amenewo. Ine ndikukhulupirira iwo udzakhala uli pa malo aang'ono amenewo pamene iwo akukangamira mochuluka kwambiri, ndipo Mulungu anabadwira, kumeneko mu Betelehemu. Ine ndikukhulupirira uko kudzakhala uko komwe ku Palestina, kumene iwo uti udzatukuke kuchokera pa dziko lapansi uko komwe ndi kudzakhala phiri limenelo.

262 Koma, mzanga wokonedwa, izo ziribe kanthu kochita ndi kachisi uyu. Mukuona? Abrahamu, Isaki, Yakobo, Paulo, oyer a onse, iwo anafa konse konse pa dziko lapansi, anawotchedwa, anamizidwa mmadzi, anadyedwa ndi mikango, ndi china chirichonse; ndipo iwo adzatulukira kuchokera mu mng'alu uliwonse, mpita, ndi ngodya ya mdziko. Ine ndikuyembekeza ine ndiri mmenemo. Ine sindikudziwa komwe nditi ndidzakakhale ndiri, koma kulikonse kumene kuli, ngati ine ndiri mu gulu limenelo, palibe kanthu kangathe kundiletsa ine kukakhala ndiri kumeneko! Mukuona? Ndipo ine sindikusowa kudzakhala ndiri pa malo ena ake aliwonse. Malo okha amene ine ndikuyenera kukhala ndirimo ndi mwa Khristu, pakuti iwo amene ali mwa Khristu Mulungu adzawabweretsa palimodzi ndi Iye. Ine sindikusamala komwe uko kuli, Iye adzawabweretsa. . . Ndikwirireni ine mwa Yesu.

263 Tayang'anani pa aneneri awo kumbuyo uko. Iwo ankadziwa mwa maganizo enieni, tsopano, kuti chiukitsiro choyamba, zipatso zoyamba, zikadzakakhala ziri mu Palestina. Abrahamu anawagula malowo, ndipo iye—osati—ndipo iye anakamuikako Sarah. Ndipo iye anabala Isaki. Isaki anaikidwa pambali pa abambo ake ndi amake. Isaki anabala Yakobo; Yakobo anakafera mu Israeli—mu Igupto, anabweretsedwanso mu Palestina. Ndiyeno, Yosefe nayenso anakafera kumeneko. Ndipo iwo anabweretsanso mafupa a Yosefe, chifukwa iye anati, “Anapangitsa. . .” anachita kumulumbiritsa Yosefe pa izo—Yakobo, kuti iye sadzamuika iye kumeneko, koma

adzamubweretsanso iye ku dziko lolonjewedwa. Yosefe anati, “Tsiku lina Ambuye Mulungu wanu adzakuchezerani inu. Undirole ine—mafupa anga adzapite ndi kukaikidwa limodzi ndi bambo anga.” Ndipo iwo anatero, chifukwa, pokhala aneneri, iwo ankamvetsa kuti zipatso zoyamba za chiukitsiro zikadzakakhala mu Palestina.

264 Tsopano, Baibulo linati...Ndipo ngati inu mukunditcha ine mneneri, ine sindimanena kuti ine ndiri; koma ngati inu mumanditcha ine zimenezo, kumbukirani, ine ndikunena kwa inu mu dzina la mneneri (mukuona?)—mu dzina la mneneri, chiukitsiro ndi mkwatulo zidzakhala za konsekonse mu dziko lonse! Ziribe kanthu kumene inu muli, pamene ora limenelo lidzabwera, inu mudzakwatulidwira mmwamba kukakomana naye Iye! Ndizo zonse! Palibe kanthu kati kadzakuletseni inu, ziribe kanthu kumene muli. Ndipo ine ndikungoyembekeza kuti ine ndidzakhala kumeneko, mmodzi wa iwo. Ine ndikungodalira ndi kuyembekeza mwa Mulungu kuti ine ndidzakhala mmodzi wa iwo ndipo aliyense wa inu adzakhala umo—mofanana.

Tsopano, kodi ife tiri nayo nthawi ya lina? Ndiye iyo ingokhala ili basi (mukuona?)—basi pafupifupi 1:00 koloko.

274. Wokonedwa M'bale Branham: Akazi anga ndi ine tinasiyana. Iye akundisumira ine pofuna chisudzulo. Iye si Mkhristu, ndipo ine ndikukhulupirira Uthengawu ndipo ine ndikufuna kuti iye apulumutsidwe (Kodi zimenezo si zabwino? Umenewo ndiwo mzimu weniweni wa Chikhristu. Mukuona?) ndipo ndikukhulupirira. Kodi ine ndichite chiani? Ife tirinso ndi anyamata awiri. (Alembapo dzina lawo.)

265 M'bale, penyani, ndiroleni ine ndikuuzeni inu, iye akakusumirani inu pofuna chisudzulo; uyo ndi Satana. Mukuona? Akanati asachite zimenezo, koma ngati inu muli Mkhristu ndipo simunachite kanthu mu dziko koti kamutchinge mkazi ameneyo, ndiye ndi Satana akuchita zimenezoyo. Iye akungoyesera kuti akung'ambeni inu apo.

266 Tsopano, ngati iye ali mmodzi wa osankhidwa a Mulungu, iye adzabwera kwa Iye. Ngati iye asali, iye si woyenera kumudandaulira. Ndiye ngati izo zitero... Ngati inu muzidandaula izo ziphwasula thanzi lanu, ndipo izo ndi zimene Satana akufuna kuti achite. Iye akugwira ntchito, ine ndikudziwa, pa inu. Kotero inu mungochipereka chinthu chonsecho kwa Mulungu ndi kupitirira patsogolo kumamutumikira Mulungu mosangalala basi momwe inu mungathere. Mulungu asamalira zina zonse zakezo. “Onse amene Atate andipatsa Ine adzadza kwa ine.” Zigwadani pa mawondo anu; ine ndipemphera nanu inu kapena chirichonse. Ine ndipempherera vutolo. Muzingoti, “Ambuye Mulungu, ine ndikumukonda iye; iye ndi mayi wa ana anga,” (ngati iye

ali) ndi kuti, “I—i—ine ndikungochipereka chinthu chonsechi kwa Inu, Ambuye. Ine ndikufuna iwo kuti apulumutsidwe, Inu mukudziwa kuti ine ndikutero; koma ine sindingapitirire patsogolo pena. Iye apita kukandisudzula ine mulimonse. Ine sindinachite kanthu kalikonse; ngati ine ndatero, ululirani izo kwa ine; ine ndipita ndikazikonze zimenezo. Ine ndikachita chirichonse.” Ndiye chiperekeni icho kwa Ambuye ndipo mungozisiya izo zokha ndiye, mungozisiya izo zokha. Zipitani apo pomwe kumakhala moyo chimodzimidzi basi—ngati kuti palibe chimene chachitikapo konse. Ndipo Mulungu asamalira pa zina zonse za izo.

275. Tsopano: M’bale Branham, kodi ndi chiani zonse izi za anthu (O, kachiwiri!) kusamukira ku Arizona? Tafotokozani izi. Apo pali mtundu wina wa malembedwe. Onani, mukuona?

Chabwino, ife tafotokoza kale zimenezo (mukuona?), chomwe zimenezo ziri.

276. M’bale Branham, kodi Mkwatibwi adzadutsa mu kuzunzidwa momwe atumwi a mpingo woyambirira anachitira?

²⁶⁷ Ayi, ine ndangofotokoza kumene zimenezo maminiti angapo apitawo. Ayi, chinthu chotsatira ndi mkwatulo tsopano. Kumbukirani, ife tiri pa dziko lolonjezedwa; ife tiri pa malire. Inu mukukumvetsa kuyenda kwa Israeli?

277. Kodi ndi kololedwa—kugwiritsa ntchito mtundu uliwonse wa kuteteza kubala?

²⁶⁸ Ine kulibwino ndizisiyire zimenezo mpaka madzulo ano (mukuona?), chifukwa ziri. . . ine ndikufuna kuti—ine ndikufuna kuti ndiyankhule chinachake pa izo.

278. M’bale Branham, ine basi...(ine ndikudikirira basi maminiti atatu ena ngati ine ndingathe. Ndiroleni ine nditenge chinachake chachifupi pano mwina.) Ine sindingathe kudzipereka kwathunthu kwa Yesu. Kodi ine ndiri ndi mzimu woyipa?

²⁶⁹ Ndiroleni ine ndingotsiriza nthawi ina yonse pa izo apo. Inu simukutha kudzipereka kwa Yesu? Iwo sakutha. . . Mukuona, ine sindikumudziwa kaya mwamuna kapena mkazi; ine sindikanatha kudziwa yemwe iye ali. Mulungu akudziwa zimenezo.

²⁷⁰ Inu simungathe kudzipereka kwa Yesu. Bwanji? Chavuta ndi chiani? Ngati inu muli mkazi, inu simumakhala mukudzipereka kwa mwamuna wanu kuti mukhale mkazake, dziperekeni zonse zimene inu muli? Dona wamng’ono pamene inu munakwatiwa, waukoma, munamenyera moyo wanu wonse kuti mukhale waukoma; koma tsiku lina inu munamupeza mwamuna amene inu munamukonda. Inu munali wake kwathunthu.

Zinthu zimene inu munkamenyana nazo moyo wanu wonse ndi kumayesera kuti muzikhala woyera, ndi momveka, ndi mwaukoma; tsopano, inu mukupereka pang'ono paliponse pa izo kwa mwamuna mmodzi. Kodi ndi kulondola uko? Inu mwadziika nokha kwathunthu mmanja mwake; inu ndinu wake. Zonse zomwe inu munaziimira mwa ukhondo, ndi mwakhalidwe, ndi chirichonse monga choncho, tsopano inu mwazitembenusa izo kwa mwamunayo, chifukwa inu mwadzipereka nokha kwa mwamunayo. Kodi inu simungathe kuchita chinthu chomwecho kwa Yesu Khristu? Kungodzipereka nokha mwanjira imeneyo—zonse zimene ine ndiri, malingaliro anga onse, maganizo anga onse. Ndithudi.

271 Ine sindikuganiza kuti inu mwagwidwa ndi mzimu woipa; ine ndikuganiza kuti mzimu woipa umakudzozani inu ndi maganizo awo a mtundu umenewo, kumayesera kukupangitsani inu kumaganiza kuti inu simungathe kudzipereka nokha kwa Mulungu. Pamene... Ndiroleni ine ndikusonyezeni inu chinachake. Chifukwa chiani inu mungamafune kuti mudzipereke kwa Iye? Chifukwa pali chinachake kunjira uko chikuitanira kwa inu kuti mudzipereke. Icho ndi chizindikiro chabwino kwambiri kuti inu mukuyenera kudzipereka nokha.

272 Tsopano, zonse zimene inu mungachite, M'bale kapena Mlongo (akhoza kukhala munthu wachichepere kapena wachikulire, chirichonse chimene ali), inu munati... Sangathe kudziyeza okha basi chotero kuti iwo angathe kudzipereka okha kwathunthu. Kungodzipereka nokha uko. “Ambuye, kuganiza kwanga, zanga zonse zimene ine ndiri, i—ine ndikufuna kuti ndizipereke kwa Inu. Moyo wanga, ine ndikuwupereka ngati moyo wa kutumikira. Nditengeni ine, Ambuye, ndi kundigwiritsa ine ntchito basi momwe ine ndiri.” Ndipo ndi chinthu chophweka chotero; ine ndikukhumba mpingo ukanati kwenikweni... ine ndikukhulupirira ng—ng—ngati kachisiyu tsopano, akanati apindule pa mafunso amenewa... Kodi inu mukuwakonda iwo? Chabwino. Iwo athandiza pang'ono.

273 Tsopano onani, pa izi, ngati mpingo ukanamafunsa kokha mafunso amenewa (inu mukuona?), kufunsa zinthu izi: ngati iwo angati azichita *izi*, kapena kuchita *izo*, ndi chirichonse, ine ndiyesera kuti ndichite mopambana zomwe ine ndingathe. Ngati ine ndakulangizani inu molakwika, izo sizinali konse mu mtima wanga kuti ndichite zimenezo. Ngati ine ndanena chirichonse cholakwika kungoti ndikweze maganizo ena anga anga ndi zinthu, osati—p—podziwa kuti izo ndi zolakwika kuti ndichite zimenezo kapena kuti ndikuuzeni inu zimenezo, ine ndingakhale ndiri wachinyengo wonyansa. Ndiko kulondola. Koma kuchokera mu mtima mwanga, ngati ine ndikulakwitsa, Mulungu akudziwa (mwaona?) ine ndazichita izo ndi zonse zomwe ziri mwa ine kuti ndiyankhe mafunso anu.

274 Ndipo kwa inu atumiki uko mu dziko kumene tepi iyi idzapita, ine sindinanene zinthu izi kuti ndikupwetekeni inu. Ine ndinanena izo chifukwa ine ndimakukondani inu. Mukuona? Ndipo ine moonadi, ndi mtima wanga wonse. . . Ndi. . . Tsopano, ine sindikuyesera kugwirira ntchito kuti ndikusonyezeni zimenezo—kuti i—ine ndikudziwa chinachake chimene inu simukudziwa za icho. Icho si chimenecho, m'bale wanga. Ine ndikungochita izi chifukwa ine ndikukukondani inu, ndipo i—i—inukundikonda ine, ine ndikukhulupirira.

275 Bwanji ngati inu mukanandiwona ine ndikupita mmusi ndi mtsinje mu ngalawa yokalamba, kunja kuno pa mtsinje uwu, pafupi ndi kumene ife tiri pakali pano, kuno ku kachisi, Mtsinje wa Ohio; ndipo mtsinjewo nkukhala uli wodzaza ndipo ukusefukira; ndipo mathithi ali basi mmusi mwanga. Ndipo inu mukudziwa kuti ngalawa imeneyo siikadutsa pa mathithi amenewo; iyo basi siichita zimenezo. Ndipo apa ine nditakhala mmenemo ndi mutu wanga ntaugonekera mmbuyo, ndi kuimba, ndi kupuma, ndi kupita mmusi momwe—kuyandama chammusi umo—mosangalala kutsika ndi mtsinje umenewo; ndipo inu mukudziwa kumusi uko ine ndikachita ngozi. Ngati inu mukundikonda ine, inu mungakuwe, kapena inu mungalumhire mu ngalawa, ndi kuthamangira kumeneko, ndi kudzandikhoma ine pa mutu ndi chinachake, kundibweretsa ine umo. “M'bale Branham, inu mwasokonezeka malingaliro! Inu mwasokonezeka malingaliro; mathithi ali apa pomwe!”

276 Ndipo ine ndikanati, “O, khala chete! Ndisiye ine ndekha!” Ndipo komabe inu mukundikonda ine mulimonse. Inu mungachite chirichonse mu dziko; inu mungandigwire ine. Ngati inu mukanati—ngati inu mukanati muiphwasule ngalawayo, inu mukanandichotsamo ine mmenemo, chifukwa inu mukundikonda ine; inu mukudziwa chomwe chiti chikachitike.

277 Ndipo m'bale, ine ndikudziwa izo ndi zomwe ziti zikachitike kwa chipembedzo chimenecho. Icho sichilimba mu mafunde. Mukuona? Inu mukupita molunjika kumene ku Bungwe la Mipingo ya Mdziko; ndipo tsopano, inu mwina muyenera kutenga icho kapena icho ndi choti chitulukemo momwe ife tiriri tsopano. Koteru, izo ziri basi ndendende, inu muyenera kupanga kusankha kwanu. Ndipo i—ine sindikutanthauza kuti ndikhale. . . Ine ndikanafuna kuti ndiiphwasule ngalawayo, chabwino; ine ndikanafuna kuti ndipange chirichonse chimene ine ndikanatha, osati kuti ndikupwetekeni inu, m'bale, koma kuti ndikudzutseni inu kuti inu mukulakwitsa. Musati muzichita zimenezo!

278 Ndipo ubatizo wa mmadzi uwu mu Dzina la Yesu Khristu, palibe munthu pa nkhope ya dziko lapansi angathe kuwutsutsa iwo mwa Lemba. Palibe munthu angatsutse izo. Palibe Lemba limodzi. . . Anthu inu, abale inu—inukundikonda ine, ine ndikukhulupirira,

muzingokumbukira, kafufuzeni mu Baibulo; kapezeni malo amodzi pamene wina aliyense anabatizidwapo konse mu Chipangano Chatsopano (iwo sankabatizidwa mu Chakale, koma mu Chipangano Chatsopano)—pamene wina aliyense anabatizidwapo konse mwa njira ina kuposa mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu; ndiye mubwere mudzasonyeze izo kwa ine. Kapena pitani mukapeze bukhu la mbiriyakale pamene iwo anabatizidwapo konse kwa mazana a zaka pambuyo pa imfa ya atumwi otsiriza. . . Mpingo wa Katolika unayambitsa ubatizowo. Katekizimu wawo amanena chinthu chomwecho, wogwiritsa ntchito dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera.

²⁷⁹ Pa kukambirana ndi wansembe, komwe kuno ku Mpingo wa Mtima Woyera, anandiuza ine chinthu chomwecho. Anati mpingo wa Katolika unkatizira monga choncho, pamene ine ndinamuuza iye kuti ine ndinamubatiza msungwana wa a Frazier uyu, pamene bishopu ankafuna kuti adziwe. Iye anati, “Kodi iwe ungalumbirire pa maneno awa?”

Ine ndinati, “Ine sindimalumbira konse.”

Iye anati, “Bishopu akufuna kuti iwe utero!”

²⁸⁰ Ine ndinati, “Bishopu ayenera kuti atenge mawu anga kapena musati muzikhulupirire izo, china chirichonse chimene iye angafune.” Mwaona? Ine ndinati, “Baibulo linati tisamalumbire konse.”

Ndipo iye anati, “Chabwino, nha. . .” Iye anati, “A. . .”

²⁸¹ Ine ndinati, “Ine ndinamubatiza iye mwa ubatizo wa Chikristu mu madzi, ndinamumiza iye pa phazi la Spring Street mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu.”

Ndipo pamene wansembeyo anazilemba izo, iye anati, “Umo ndi momwe mpingo wa Chikatolika unkatizira kale.”

Ine ndinati, “Liti?”

Iye anati, “Mu masiku a atumwi.”

Ine ndinati, “Inu mumawatcha iwo Akatolika?”

Iye anati, “Zedi, iwo anali.”

²⁸² Ine ndinati, “Ndiye ine ndine Mkatolika wabwinoko kuposa momwe inu muliri. Ine ndimatsatira chiphunzitso chawo.” Ndiko kulondola. Mwaona, mukuona? Iwo amadzinenera zimenezo, koma siziri choncho.

²⁸³ Mpingo wa Katolika unakhazikitsidwa ku Nicea, Roma, pansu pa Konstantini, pamene mpingo ndi boma n—zinalumikizana palimodzi, n—ndipo boma linaupatsa mpingo chuma, ndi zinthu monga choncho; iwo makamaka ankaganiza kuti iwo anali mu Zakachikwi. Iwo ankaganiza iwo anali atagunda Zakachikwi. Zimenezo zinali zakachikwi za Satana. Ndizo ndendende kulondola. Inu musati muzikhulupirira zinthu zoterozo. Inde, bwana!

284 Tsopano, koma... Ndiye pamene iwo anapanga—kapena anali mmalo mokhala nalo—fano, iwo anamuchotsa apo—iwo anamuchotsa apo Venus, anaikapo Maria; anamuchotsa apo Jupiter, anaikapo Paulo kapena Petro. Komwe uko k—ku Vatican, uko komwe mu—Roma tsopano, mu Mzinda wa Vatican momwe, choimikidwa cha mapazi naintini cha Petro, iwo amadzinenera kuti apsyopsonapo zitatu za zala zimenezo za phazi la choimikidwa chimenecho. Mukuona? Ndipo chirichonse chiri...

285 Zonse kumatsika... Tinapita ku tchalitchicho, Billy ndi ine, mmawa wina kumeneko, tinapita mmusi mu chipinda chapansi kumene amawaika mamonki onse ndi zinthu monga choncho ndi kuwasiya mafupa awo azivundira mu fumbi limeneli—fupa limodzi kuvunditsidwa ndi limzake kumeneko—ndiyeno nkutenga mafupawo ndi kupangira zolumikiza za zolumikiza zopepuka za manja amafupa zikulendewera monga *chonchi*, ndi zigaza; ndipo anthu obwera mmenemo azipukuta zigaza zimenezo mpaka zayera, kuyesera kuti azipeza madalitso kuchokera ku zigaza za anthu okufa amenewo. Ndi machitidwe a zamizimu. Mukuona?

286 Ndipo ndi kumene izo zinayambira uko komwe, mu Roma, ndipo uko ndi kumene mpando wa chirombo uli, ndipo kuchokera kumeneko kunabwera manthu hule wamkulu. Ndipo ana ake aakazi ali timahule ndendende basi momwe iye aliri, chifukwa iye analipatsa dziko lonse chikho cha mkwiyo wake—chikho cha umboni wake, chimene chinasakanizidwa mmenemo ndi ndulu ya dziko lapansi. Ndipo iye anali ndi umboni wake. Iye anati, “Ine ndikukhala ngati namwali, ndipo i—ine ndikukhala ngati wamasiye (ine ndikutanthauza), ndipo sindiri wosowa kanthu”; ndipo iye sakudziwa kuti iye ndi womvetsa chisoni, wopandapake, wakhungu, wosauka, ndipo sakudziwa izo. Ndi zimenezozo. Ndipo zimenezo ndi za mpingo wa Katolika kuphatikizapo chipembedzo cha Chiprotestanti chirichonse! Koma mu chisokonezo chonse icho kunja uko, uko kuli anthu ofunika amene amawakonda Ambuye Mulungu ndi mtima wawo wonse, solo, ndi malingaliro. Ndipo iwo akuganiza kuti akulondola. Iwo akuganiza kuti iwo akuchita zolondola. Mulungu adzakhala Woweruza Wamkulu.

287 Kwa ine, ngati Mulungu ati adzauweruze mpingo ndi dziko—mpingo wa Katolika umenena chomwecho—ndiye ine ndinamufunsa bambo uyu amene ine ndinkafunsidwa naye... Iye anati, “Mulungu adzaweruzza dziko ndi mpingo.”

Ine ndinati, “Utiwo?”

Iye anati, “Mpingo wa Katolika.”

288 Ine ndinati, “Mpingo wa Katolika wake uti? Iyo ndi yosiyana umodzi kwa umzake.” Mpingo wake uti? Wa Greek Orthodox kapena wa Chiroma? Kapena ndi uti umene Iye ati

adzaweruze nawo ilo? Ngati Iye ati adzaliweruze ilo ndi mpingo wa Chiprotestanti, utiwo? Wa Methodist, Baptisti, Chilutera, Chipentekoste; kodi Iye adzaliweruza ilo ndi uti? Baibulo linati Iye adzaweruze dziko ndi Yesu Khristu, ndipo Yesu Khristu ndiye Mawu. Kotero kwa ine, ndi Mawu a Mulungu amene Iye ati adzaliweruze nalo dziko lapansi. Ndiko kulondola. Ndipo ine ndikukhulupirira ziweruzo Zake ziri mu dziko lapansi tsopano, ndipo ine ndikukhulupirira. . . Tiyeni ife tifunefune ndi mtima wathu wonse kuti tithawe mkwiyo wa chiweruzo cha mkwiyo wa Mulungu umene uti udzatsanuliridwe pa dziko losakhulupirira ili; ndipo palibe njira yina konse yomwe ilo lingathawire izo—kuzithawa izo.

²⁸⁹ Sizidzatheka nkomwe, nkomwe, nkomwe kubwera chipulumutso kwa dziko kenanso. Iwo adutsa mzere wawo pakati pa chisomo ndi chiweruzo. Pali. . . Inu mukhoza kuika Abraham Lincoln mu dera lirilonse la mu United States, ndipo izo sizidzatha kutembenuza nkomwe gulu ili la “Marike” ndi “Maelvisi” kubwerera kwa Mulungu.

²⁹⁰ Pamene inu munawona mu pepala (ine ndiri nazo izo. Ndibweretsa izo kwa inu madzulo ano ngati inu mukufuna kuti muziwone izo usikuuno), kumene mpingo wa Chipresbateria (ambiri a inu mwina munaziwona izo)—mpingo wa Chipresbateria ukudutsa mu misa kapena k—k—kupyola mu sakramento ndi roko ndi rolo. Abusa ataima pamenepo akuwomba manja awo monga choncho; ndipo iwo anali akudutsa mu njira ya mtanda ndi “kumavina izo” ngati roko ndi rolo mu mpingo wa Chipresbateria.

²⁹¹ Ndipo pamene gulu lapansi motsika ili, likufuula, lauwe la Mabitoloji, limene likutchedwa chomwecho, limene lafika pansu pa munthu ndipo akufuna kuti akhale tizirombo. . . Iwo anakana chigwirizano cha ntchito ya madola zikwi zana mu St. Louis masabata angapo apitawo; sakanalola kuleka pofuna zimenezo. Anabwera kunoko, gulu la achichepere, zigawenga za anthu Achingezezi kumeneko ali ndi tsitsi lawo likulendewera pansu mpaka mmaso awo. Ndipo tsopano, iwo ali ndi chipembedzo chao chao chimene iwo akuyambitsa. Inu mwaziwona izo mu magazine ya *Look*. Mukuona?

²⁹² O, momwe dziko lino lavundira. Palibe chiyembekezo kwa ilo konse; iwo adutsa mzere wolekanitsa pakati p—pakati pa kulingalira ndi nzeru zawamba, nanga tikati pakati pa chipulumutso.

²⁹³ Anthu sakutha ngakhale kuweruza. Ife tiribe amuna panonso monga ife tinkakhalira nao. Ali kuti Patrick Henry? Ali kuti Abraham Lincoln?—amuna amene angathe kuima chifukwa cha kukhudzidwa kolimba.

²⁹⁴ Ali kuti amuna awo amene angadzuke apo ndi kuwapangitsa akazi openga awa kunja uko, odzivula okha

ndi—ndi kumatuluka pamaso pa amuna awa; ndiyeno—ndi kumawayendetsa iwo kunja uko monga gulu la odzivula, ndiyeno nkumamuika mnyamata mu chilango amene angamunene mmodzi wa iwo? Kuli kuti kungalira kwanu? Nzeru wamba ndi chiani? Ngati iye akudziika yekha kunja uko, musiyeni iye azipita ngati galu. Inde, bwana! Ngati iye sati apitenso ku... makhaliidwe a wamba a iye oposa awo... Ali kuti malamulo amene angaziletse zimenezo?

²⁹⁵ Komwe kuno mu Louisville, Kentucky, masabata awiri apitawo pamene mkazi uja ali ndi—amayesera kuti apange—ayike dzina lake mu pepala, anavala kabudula wosambira wa pulasitiki, anayanda napita kumeneko kuchokera ku Brown Hotel; ndipo mpolisi anayesera kuti amuimitse iye, ndipo sanaime ayi; anamuseka iye. Ndipo iye akanaponyera mfuti pa iye kuti amuimitse uyo; iye anamukankhira iye mu galimoto ndipo anamupangitsa iye kuti akakomane naye ku sitieshoni ya polisi chifukwa chovala mopanda khalidwe ndi zinthu monga zimenezo, ndipo iye anapita ndipo anakakomana... Inu mukudziwa zimene iwo anachita pa izo? Anamuchotsa ntchito mpolisiyo.

²⁹⁶ Mulungu thandizani fuko limene lavundali! Iwe sungadutse nazo kupatula ngati utachita zolakwika. Ife tikhoza kusadutse nazo, koma tingathe kukafika kumwamba; ndipo uko ndi kumene ife tikuyembekezera. Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu.

²⁹⁷ Ambuye Yesu, lolani M'busa wamkulu abwere ndi kudzatichotsa ife mu izi, Ambuye. Ife tikumuyembekezera Iye. Ife tikuyang'anira ora limenelo. Pamene ife tikuliwona dziko litavunda kwambiri. Inu munati ilo likanadzakhala mwanjira imeneyi. Aneneri anu aakulu ananenera kuti maora awa akanadzakhala ali kuno. Ife tikuwakhulupirira aneneri, Ambuye; ife tikuwakhulupirira iwo.

²⁹⁸ Ndipo tsopano, ife tikupemphera, Mulungu, kuti Inu mutipatse ife aneneri kuti atanthauzire Mawu awa kwa ife, kuti ife tikhoze kumadziwa ngati tikulondola kapena tikulakwitsa. Ife tikuwona aneneri abodza akuwukapo; iwo ali mu zipululu, Mzinda wa Salt Lake, madera onse a fukoli, mitundu yonse ya zipululu, ndi mitundu yonse ya zipinda zobisika, mitundu yonse ya Atate Aumulungu, ndi zina zotero, kulikonse.

²⁹⁹ Powawona abale osauka achikuda awo, alongo kunja uko tsopano; iwo amafuna kusakanikirana. Mwamsanga pamene iwo anakupeza iko... Uko nkulondola; iwo amayenera kukhala nako iko; iwo ndi abale ndi alongo. Tsopano, pamene iwo akupeza iko, iwo ayipirapo kuposa kale. Izo zikusonyeza kuti ndi zodzozedwa ndi chikominisi. O, Mulungu, kodi anthu osauka awo angawone zimenezo? Kutu izo zimangochitidwa... Chabwino, izo zikuyenera kuti zichitidwe, Ambuye.

300 Bwerani, ndi chimene ife tikufuna. Inu mungobwera, Atate. Ife tikuyembekezera. Bwerani, Ambuye, titengereni ife mkhwapa Mwanu. Tikhululukireni ife machimo athu. Palibe ayi—palibe chilungamo panonso mu dziko muno. Chinthu chimodzi chikukoka motsutsana ndi chinacho, ndipo komabe izo zangokhala zodyedwa kwambiri ndi mphutsi mpaka inu—mulibenso zomveka mmenemo. Inu munati thupi lonselo langosanduka ngati mabala onunkha. Zoonadi, gome lirilonse liri lodzaza ndi masanzi. Inu munati, “Ndani amene ine ndingamuphunzitse chiphunzitso? Nndani amene ine ndidzamupangitse kuti amvetse mu tsiku limenelo?” Gome lonse la Ambuye liri lodzaza masanzi. Ife tikuziwona izo, Ambuye. Ife tikuziwona oralo pano. Tithandizeni ife, chonde.

301 Wokonedwa Mulungu, ochuluka a mafunso awa pano okhudza anthu kubwera ku Arizona. O, wokonedwa Mulungu, lolani anthu okondeka, ofunikira awo... Iwo akamvetsera kwa tepi iyi kumeneko. Aloleni iwo adziwe kuti ine sindine wolamalira mwankhanza kuti ndiziwauza iwo koti azikakhala, zoti azichita. Ndipo mulole iwo amvetse bwino bwino zimenezo. Ngati iwo akulikonda dziko limenelo, inenso ndiri, asiyeni iwo akhale kumeneko, Atate. Koma pamene iwo akuphunzitsa kuti mkwatulo uyenera kubwera kuchokera kumeneko, ndipo uko kokha, kapena kuti iwo akuyenera kumakhala ali ndi ine, wochimwa wosauka, wosayenera, waue, wopulumutsidwa mwa chisomo cha Mulungu—kuchita kuti azikhala pondizungulira ine... Ambuye, ine ndikufuna kuti ndikhale pozungulira—ine ndikufuna kuti ndikhale pomwe pali Paulo; ine ndikudziwa kuti iye apitako. Ndi Petro, ndi Yakobo, ndi Yohane, iwo ali mu Palestina anaikidwa penapake kumeneko. Ine ndikudziwa ine ndidzapita limodzi nawo iwo ngati Inu munali nalo dzina langa pa Bukhu lija chikhazikitsireni maziko a dziko. Ine ndidzakhala ndiri kumeneko. Ndipo ine ndikupemphera, Mulungu, kuti aliyense wa iwo adzakhale ali kumeneko. Ndithandizeni ine, Ambuye, kuti ndiwasonkhanitse iwo onse abwerere kuno kwinakake, kumene iwo angathe... Iwo akufuna kuti azimvera utenga ndi aphunzitsi aakulu awa monga M'bale Neville, ndi M'bale Capps, n—ndi abale ena onse awa kuno: “Junie,” ndi M'bale Ruddell, ndi o, J.T., ndi onse awo—onse awo: M'bale Collins, ndi M'bale Beeler, ndi M'bale Palmer, n... Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu mungopereka izi kwa awa... .

L—l—lolani iwo abwere kuno kumene iwo amaumva Iwo kwenikweni, ngati iwo akufuna kuti aziumva Iwo, osati kuthamangira kutali uko ku chipululu icho. Iwo akuyesera kuti azichita ndendende zimene Lemba ili linawauza iwo kuti asachite. “Onani, iye ali mu chipululu; musazikhulupirire izo ayi! Onani, ziri mu chipinda chobisika; musakhulupirire izo ayi!” Ambuye, ine ndikuyesera mwa kupambana kwanga kuti

ndiwachenjezo iwo, koma izi zonse zikusonyeza kuti oralo lafupikira tsopano. Mithunzi ya usiku ikugwa.

³⁰² Ine ndikupempherera chifundo, Ambuye. Khalani ndi chifundo pa ine; ndithandizeni ine. Izo zikundipangitsa ine manjenje, Atate. Ine ndikupemphera kuti Inu mundithandize ine. I—ine sindikufuna kuti ndisindikize moyo wanga... Ntchito yanga yonse kuno ikhale ili kunja kuno wotengeka wina akutsogolera gulu lina kapena kachiphunzitso kotsatira munthu mu chipululu kwinkakwake. Musalole dzina langa kuti lipite pansi monga choncho, Ambuye. Ine ndamenyera molimba pofuna izi. Ndine wodzipereka mu izo momwe ine ndingakhali ndiri. Mulungu, musalole izi kuti zichitike. Ndithandizeni ine mwanjira ina. Ine sindikudziwa zoti ndichite; ine ndikungodalira pa Inu, koma Inu mundithandize ine. Ine ndichita chirichonse chimene Inu muti mundiuze ine kuti ndichite. Ine ndine wantchito Wanu; awa ndi ana Anu. Ambuye, awa... Ochuluka a anthu awa, nainte naini pa handiredi, Ambuye, ndi olimba kwenikweni. Iwo akukhulupirira; iwo akudziwa; iwo akumvetsa. Ndipo iwo akudziwa kuti si ineyo; koma ine ndikudziwa zinthu izi ziyenera kuchitsatira chitsitsimutso chirichonse, ndipo ichi chiribe kutetezeka kwa izo. Kotero ine ndikupemphera kuti Inu mutithandize ife tsopano.

³⁰³ Tithandizeni ife pamene ife tikupita kukakhala ndi chakudya chochepa cha masana lero, Ambuye. Dalitsani kusonkhana kwathu palimodzi. Dzatisonkhanitseni ife mobwerera muno mofulumira madzulo ano. Ambiri a iwo asowa kuti apite kwawo tsopano, Ambuye. Iwo ayenera kuti apite—kwawo, ndipo ine ndikupemphera kuti Inu muwathandize iwo. Mulole iwo akakhoze kutha mwanjira ina, Ambuye, kuti adzaipeze tepiyo kuti adzamve mafunso ena onsewo. Mwinamwake lawo silinayankhidwe. Ine ndikupemphera kuti Inu muwathandize iwo, Ambuye.

³⁰⁴ Ndithandizeni ine mwaliwiro kwenikweni usikuuno kuti ndingoyankha mafunso awa ndi kutengeramo lililonse la iwo amene ine ndingathe. Mpaka ife tikomane muno madzulo ano, Inu mutatidalitsa ife. Mu Dzina la Yesu ine ndikupemphera. Amen.

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye,
Poti Iye anayamba kundikonda,
Nagula chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

³⁰⁵ Zinalamba pamene, ine ndinalamba izo kuti nthawizonse zizikhala patsogolo panga: “Khristu patsogolo panga, pamene ine ndikuyankha mafunso amenewa.” Kodi inu mukukhulupirira kuti ine ndimanena izo kuchokera mu mtima wanga? Chirichonse ndi chochokera mu mtima wanga kuti ndithandize.

Ena a iwo akhoza kubwera kudzatenga maphukusi awo pano.

³⁰⁶ Wokonedwa Mulungu, apa pali mipango, maphukusi ali apa. Izo zikupita kwa odwala ndi osautsika. Lolani wotanthauzira wamkulu wa Mawu, Mzimu Woyera amene anawalemba Iwo, mulole Iye abwere pafupi tsopano chifukwa cha gawo ili la utumiki ndipo adzadalitse zovala izi. Ambuye, ngati ine ndikuganiza za inemwini, ndine yani kuti ndigonetse thupi langa losayera, lauve molambatitsa pa mipango iyi imene ikuima pakati pa imfa ndi moyo kwa ochuluka? O, Mulungu, ine ndikunjenjema. Koma pamene ine ndikuganiza kuti... Inu simukundiwona ine, Inu mukungomva liwu langa. Ilo likubwera kupyolera mu Magazi a Ambuye Yesu kumeneko. Tsopano, ine ndikukhulupirira kuti Inu mundiyankhira ine basi monga Inu munamuchitira Iye, chifukwa Iye anapita ine ndisanabwere kuti akakhale pa dzanja lamanja, kumwamba uko, la Ufumu mmwamba umo. Ndipo Magazi Ake ali kumeneko monga chitetezero, ndipo ine ndaphimbidwa pansi pa Magazi amenewo.

³⁰⁷ Ine ndikukhulupirira, Ambuye, kuti Inu mukawachiza iwo, pakuti iwo ali osowa. Iwo sakanati akhale ndi izi zitaikidwa apa. Ine ndikupemphera kuti Inu muwapangitse aliyense kukhala bwino. Pamene ine ndikudziyika ndekha modzilambatitsa pa izo, monga... Iwo amati anatenga kuchokera ku thupi la Paulo... Iye anali wochimwa basi nayenso, Ambuye, wopulumutsidwa mwa chisomo Chanu. Anthu ankamukhulupirira iye, ngakhale iye ankawazazira iwo ndi chirichonse, koma iwo anakdziwa kuti iye anali wolishya. Iwo anakdziwa iye—anatumizidwa kuchokera kwa Inu, chifukwa Inu mumadzitsimikizira Nokha mwa utumiki wake. Mulungu, anthu awa akukhulupirira chinthu chomwecho lero. Ine ndikupemphera kuti Inu muwathandize iwo tsopano ndi kumuchiza aliyense mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

³⁰⁸ Kodi inu muli ndi njala? Chabwino. Ine ndiri ndi njala yofuna mafunso enanso. “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu alionse amene atuluka kuchokera mkamwa ya Mulungu.” Tsopano, ine mwinamwake... Ena a mafunso awa, ine ndikhoza kusakhala nawo iwo molondola; ine ndangochita mopambana momwe ine ndingathere. Usikuuno, ine ndiyesera kuti ndiyambire basi pa 7:00 koloko. Chabwino, tchalitchi chitsegulidwa pa 6:30. Ndipo inu amene mungathe kutsalira... Inu amene simungathe, ife tikumvetsa; zimenezo ziri bwino bwino. Koma ine ndiyesera kuti ndilitenge lirilonse la awa momwe ine ndingathere kutero usikuuno. Mulungu akadalitseni inu mpaka ife tidzakomane.

Tsopano, tiyeni ife time pa mapazi athu ndi kuimba nyimbo yabwino yakale iyi, nyimbo yathu yobalalitsira, *Tenga Dzina la Yesu Limodzi Nawe*. Chabwino.

Tenga Dzina la Yesu nawe,
Mwana wachisoni ndi watsoka;
Lidzakusangalatsa ndi kukutonhoza,
Litenge, kulikonse upita.

Dzina lofunika, kukoma kwakeko!
Chiyembekezo cha padziko ndi chisangalalo
cha Kumwamba;
Dzina lofunika, kukoma kwakeko!
Chiyembekezo cha padziko ndi chisangalalo
cha Kumwamba.

³⁰⁹ Ine ndikufuna kuti ndipange kulengeza uku. Billy anangonena kuti anatenga chopereka chachikondi mmawawu (mukuona?), ndipo anati iwo anali ndi chopereka chabwino chachikondi. Ine ndinamupangitsa iye kuti apite kumbuyo kwa nyumbayi ndi kukaima kumbuyo uko. Kwa anthu kuno amene sanabwere atakonzeka, mulibe ndalama ya chakudya chanu, Billy akupatsani inu ndalama ya chakudya chanu ndi za—kuti mukalipirire mtengo wa hotelo kapena mtengo wa motelo, chirichonse chimene icho chiri. Inu mutenge ndi kukalipirira izo tsopano. Ngati inu muli . . . Ngati inu mungathe kukhala . . . Billy akakumana nanu inu kumbuyo uko ndi kukatenga dzina lanu ndi kumene inu mukukhala, ndipo ife tilipirira chakudya chanu ndi mtengo wa hotelo yanu kuchokera mu chopereka chachikondi chimene ananditengera ine mmawa uno.

Mpaka tidzakomane! mpaka tidzakomane!
Mpaka tidzakomane pa mapazi a Yesu;



Khalidwe Dongosolo ndi Chiphunzitso cha Mpingo, Bukhu Lachiwiri
(Conduct, Order And Doctrine Of The Church, Volume Two)

Mauthenga awa a M'bale William Marrion Branham olalikidwa ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito ndipo anadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Ndipo kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org